


KODI MOYO WANU NDI WOYENERA UTHENGA?

 Tiyeni tikhalebe chiimire mphindi chabe, pamene ife tikuweramitsa mitu yathu tsopano ndi kuyang'ana kwa Ambuye. Ngati pali zopempha zirizonse zoti zidziwike kwa Mulungu, inu mungatero tsopano pa nthawi ino pongokweza dzanja lanu kwa Iye, monga *choncho*, ndipo muchigwire pa mtima wanu chimene mukuchifunacho.

² Atate athu Akumwamba, ife tiri othokoza chifukwa cha tsiku lina. Ndipo tsopano ilo layamba kupita; ilo likhala mbiriyakale. Misonkhano ya mmawa uja yadutsa kale. Mawu amene ananenedwa ali mu mlengalenga, pa tepi, ndipo ife tidzayenera kuti tidzakumane nawo Iwo tsiku lina. Iwo akuyenera kudzakhala olondola kapena olakwika. Ndipo ife— ife tikukhulupirira kuti Iwo ndi olondola, chifukwa Iwo ndi Mawu Anu.

³ Tsopano, ife tikupemphera kuti Inu mupereke kwa ife, usikuuno, zopempha zimene ife tikuzipempha. Ndipo manja athu, ife tawakweza, tikupempha zosowa. Inu mukudziwa zimene ife tikuzisowa, ndi zimene ife tikuzipempha. Chotero ife tikupemphera kuti Inu mutiyankhe ife, Ambuye, ndipo mutipatse ife zokhumba za mtima wathu, ngati izo, tingazigwiritse ntchito izo pokulemekezani Inu. Perekani izi, Ambuye.

⁴ Chizani matenda pakati pathu. Mutengere kutali tchimo lonse ndi kusakhulupirira. Mutipatse ife Anu...gawo la madalitso Anu kenanso, usikuuno, Ambuye, pamene ife tikusinkhasinkha pa Mawu, ndi nthawi imene ife tikukhalamo. Ife tasonkhana pamodzi, Atate, osati kwa cholinga chirichonse koma kuti tidzayesere kuphunzira momwe tingakhalire abwinoko, ndi kukhala moyandikira pafupi ndi Inu. Pakuti ife tikuliwona tsiku likuyandikira, ndipo ife tikuyenera kudzisonkhanitsa tokha pamodzi mowirikiza, ndi kudzatenga malangizo kuchokera kwa Inu. Perekani izi, Atate, mu Dzina la Yesu. Amenii.

Zikomo inu. Inu mukhoza kukhala.

⁵ Ine ndikudziwa kwatentha kwambiri, ndipo malo onse ndi ozadza mmene alirimu. Ndipo chotero ndife opepesa kuti tiribe...chobweretsa mpweya wozizira chirichonse. Ndipo ine...Mwinamwake icho chidzakhhalapo...Pali zinthu ziwiri zimene ine ndikufuna kuti ndiwuchitire mpingo, mwamsanga ine ndikabwerera mmene ine ndikufunira, ngati

ine ndingadzabwerere ku misonkhanoko bwino. Ine ndikufuna a—piyano, pamene iyo ingadzamakhale *chonchi*, kuti wapiyano azidzayang'ana kwa osonkhana. Ine ndikufuna limba lidzakhale mbali *iyi*; ndi chobweretsa mpweya wozizira. Ndiye ine ndikumverera kuti izo zikhoza kudzakhala chomwecho. Ndipo chotero ife tiri...Ife tiwadallira Ambuye, ndipo ndikudziwa kuti Iye apereka izo kwa ife.

⁶ Ine ndikukhulupirira, iwo anandiiza ine, M'bale Hickerson wangotenga kumene *ichi* kuchokera mmagazini. Iye anadzaika icho pa desiki yanga kumbuyo uko. Icho ndi kuwundana kwa Angelo kuja chimene chiri mmagazini chimene chimakambidwa. Mukuona maonekedwe a piramidi? Tamuonani Uyu kumbali *iyi*, wa phiko losongoka, akubwera ndi chidali Chake chitatuluka monga *choncho*, kumbali ya dzanja langa lakumanja. Monga ine ndinayankhulira kuchokera pa guwa lomweli ili, miyezi ndi miyezi ndi miyezi yapitayo, mwaona, ndi Icho apo. Ndipo *Look* maga-...Kapena, *Life* magazine ili ndi Chimenecho, ya—ya Meyi, ya Meyi 17, ine ndikukhulupirira ndi choncho. Nkulondola uko? Ya Meyi 17, imeneyo. Akazi a Wood amandiiza ine lero kuti ambiri amawaimbira iwo ndi kumawafunsa. Zimenezo ziri mu ya mu Meyi, ya Meyi 17.

⁷ Iwo ndi mtambo wachinsinsi. Mtambowo ndi wa twentesikisi mailosi mulitali ndi sate mailosi chopingasa. Ndipo ndicho chimene ife timanena pano. Uko ndi kumene Mngelo wa Ambuye anadzatsika ndi kudzagwedeza malowo. Ndipo paliponse...Izo zinamveka mofuula...

⁸ Ine ndikudziwa pali munthu mmodzi, ngati...Ine ndikuganiza, M'bale Sothmann, ine ndinamuwona iye kanthawi kapitako, penapake. Iye ali pano. Iye anali ataima...Eya. Kumbuyo komwe *kuno*. Iye anali ataima pafupi pamene izo zimachitikira. Ine ndikuganiza kuti ine sindinali patali kwambiri ndi iye. Ine ndinangomuwona iye, ndinayesera kumubaibisa iye. Kungoti, ine ndinatenga zopenyera patali zake. Kutu, a—nyama, zimene ife tinali kusaka, zinali... Sizinali pa phiri ili. Tsopano izo zinapita ku phiri linalo. Ine ndinakazipeza izo, dzana lake, ndipo ndinadzawauza iwo koti apite. Ine ndinapita cha *uku*, kumene, ngati izo zikanazadzera njira iyi, ine ndikanadzangowombera mu mlengalenga ndi kuzithamangitsira izo mbali imeneyo, kuti iwo akakhoze kupeza yawo—yawo—nyama yawo. Chotero, zinali nguluwe zimenezo.

⁹ Ndipo chotero ine ndinadzapita, mbali iyi, ndipo izo kunalibeko. Izo kunalibekonso kumbali iliyonse. Ine ndinamuwona M'bale Fred akutuluka, ndipo izo kunalibeko. Iye anabwerera mmbuyo, ndipo M'bale Norman anapita kuseri kwa phirilo. Ndipo ine ndinapotoloka, ndinadzapita mmusi mu kaphompho kakang'ono ndipo ndinadzakwera mmwamba, basi ndekha ndekha, pafupifupi mailosi ndi theka kudutsa malo ena amiyala. Ndipo ine ndinadzakhala pansu ndipo ndinali

ndikungoyang'anayang'ana pozungulira. Kunali kukuyamba kucha tsiku limenelo.

Ndipo ine ndinali ndikutola zijazi, zimene ife timadzitcha uko, mitu ya mbuzi. Izo zimakhala chinachake ngati chisoso. Ndikuzichotsa izo pa mwendo wa thalauza langa, chimodzimodzi basi mofanana ndi momwe ine ndinaziwona ndekha ndikuchita izo pamene ine ndinali kuno ndikumakuuzani inu za masomphenya, miyezi sikisi, pafupifupi, izo zisanachitike. Ine ndinati, "Izo ndi zachirendo. Taonani mmene ine ndiriri mwangwiro kumpoto kwa Tucson, kukhala ngati kumpoto chaku mmawa. Kupangitsa . . ."

"Tucson," inu mukukumbukira, ine ndinati, "kummwera chakumadzulo pang'ono."

Ndipo ine ndinati, "Izo ndi zachirendo." Ine ndinali kuyang'ana pa chisoso, monga *chonchi*, ndikuchichotsa icho pa langa. . . chochuluka cha icho, ndikuchichotsa pa mwendo wa thalauza langa. Ngati inu simunayambe mwapitako kumeneko, ilo ndi dziko lachipululu. Ilo si longi ngati kuno, nkomwe. Pafupifupi kuchulukitsa ka twente kuwala kwake; ndipo kulibeko mitengo ndi zinthu monga tiri nazo kuno. Kwangokhala akaloga basi ndi mchenga.

¹⁰ Chotero ine—ine ndinali ndikungoyang'ana pa izo, monga *choncho*. Ine ndinangokwezera maso anga mmwamba. Ndipo pafupifupi, ine ndingati, theka la mailosi kuchokera kwa ine, ine ndinawona gulu lonse la. . . gulu la nguluwe, zitagona, zikubwera cha kumapeto, kumene izo zinali kudya malwa enaake. Ndipo ine ndinaganiza, "Tsopano, ngati ine nditangotha kumutenga M'bale Fred ndi M'bale Norman kuti apite kumeneko, malo ake ndi amenewo."

¹¹ Ndipo madzulo apambuyo pake, Mzimu Woyera unali wochulukira kwambiri mu msasamo, mwakuti Iye anali kundiuza ine zinthu zimene zinali zitachitika ndi zimene zimachitika. Ine ndinachita kudzuka ndikumachokapo pa msasa wangawo.

Ndiyeno, mmawa wotsatira uwo, ine ndinali nditapita kumtunda uko. Ndipo ine ndinayambapo. . . Ine ndinati, "Tsopano, ngati ine ndingathe kukafika kwa M'bale Fred, ine ndimuzungulitsa iye phiri ili," limene liri pafupifupi ma—mailosi mbali *iyi*. Ine ndinachita kupita pafupifupi—pafupifupi mamailosi awiri, kapena abwinoko, kukamutenga iye, mwinamwake atatu. Kubwerera mbali *iyi*, kutsetserekeru uku, chimene ife timachitcha "njira ya nguluwe," nkudzabwerera chokwera monga *chonchi*, pamwamba pa mapiri amiyala, osongoka awa, ndi kudzathamanga chotsika njira *iyi*, kudulira ndi kubwerako, ndi kumapita ndikutsikira mbali *iyi* ndi kukamutenga iye. Ndiye iye anachita kutsetserekeru mmusi mwa phiri, kuti akamutenge M'bale Norman, amene mwinamwake anali pafupifupi mamailosi foro kapena faifi,

kenako nkumabwerera. Ndipo ine ndinali woti ndikaika ka—kachidutswa kakang’ono ka Kleenex kamene ine ndimati ndikapachike pa chidutswa cha—cha lijowe pamenepo, kuti ine ndidzathe kuzilozera ndekha kuti ndi mpita wuti ndidzatulukire pamene ine ndizidzabwerera.

¹² Ndipo ine ndinangodutsa pa mtumbira wawung’ono kumene kuli miyala yambiri yosongoka, ndipo uko kuli—kanjira ka agwape amabwera akutsetserekerera kumbali inayo, pafupifupi, oh, forte, mayadi fifite pansi pa mtsinjewo. Izo zinali pafupifupi, oh, izo zinali kutacha tsikulo, ine ndingati eyiti koloko, kapena naini. Kodi inu mukuganiza kuti ndi chinachake monga choncho, M’bale Fred, mwinamwake naini koloko, chinachake? Ine ndinathamangira mbali *inayi*, mwamsanga, kuwopetsa kuti nguluwe zisandiwone ine. Izo ndi nkhumba zakuthengo, inu mukudziwa, ndipo izo ndi zowopsya ndithudi.

¹³ Chotero ine—ine ndinapita ku phiri mbali *iyi*, ndipo ndinadulira, ndinayambapo, ndinathamanga chokwera phiri. Ndipo ine ndimangothamangira kumeneko, mu kakang’ono, chimene ife timachitcha, modutsa agaru. Ndipo mwadzidzidzi, dziko lonselo linangochita phokoso. Ine sindinayambe ndamvapo kuphulika koteroko! Linangogwedezeke, ndipo miyala inagudubuzika. Ndipo ine ndinamverera ngati ine—ine ndiyenera kuti ndinalumpha mapazi faifi kuchokera pansi, zinawoneka chomwecho. Izo basi—zinangondiwopsya ine. Ine ndinaganiza, “Oh, mai!” Ine ndinaganiza kuti ndawomberedwa. Kuti winawake. . . Ine ndinali nditavala chipewa chakuda. Ine ndinaganiza kuti iwo mwinamwake aganiza kuti ndine nguluwe ikuthamanga chokwera phiri, winawake wandiwombera ine. Izo zinamveka mwaphokoso kwambiri, pa ine kumene, monga choncho. Kenako, mwadzidzidzi, Chinachake chinati, “Yang’ana mmwamba.” Izo zinali pamenepo. Kenako Iye anandiuzza ine, “Ndiko kutsegulidwa kwa Zisindikizo Zisanu Ndi Ziwiwi zimenezo. Bwerera kwanu.” Chotero, ndine ndiri kuno.

¹⁴ Ine ndinadzakumana ndi M’bale Fred ndi M’bale Norman, pafupifupi ora kenako, pamene ine ndinapezana nawo. Iwo anali akusangalala ndipo akukamba za izo. Ndi zimenezotu. Ndipo sayansi ikunena kuti ndizosatheka kuti—kuti mtundu uliwonse wa—wa chifunga kapena chirichonse chingakwere patali chomwecho, chifunga, mame. Mukuona? Izo zimagopita basi. . . Ine sindingadziwe. Ine—ine. . .

¹⁵ Ife, pamene ife tikupita kutsidya kwa nyanja, ife timayenda mapazi naini sauzande. Izo ndi pamwamba pa namondwe. Izo ndi pafupifupi mamailosi foro. Ndikuti, tiyeni tinene kuti, mwinamwake izo ndi mamailosi fiftini mpaka inu simungapezenso mame. Koma apa ndi mamailosi twente sikisi, ndipo iwo unapachikika pamenepo tsiku lonse. Mukuona? Iwo sakudziwa chimene Icho chiri. Koma, tikuthokoza Ambuye, ife tikudziwa.

Zikomo inu, M'bale Hickerson. Ine ndiisunga iyo pa desiki langa uko. Ndipo pamene ife tizidzalemba bukhu, bwanji, ndiye ife tikhoza kudzakhala nayo iyo.

¹⁶ Ine ndiri ndi cholemba chaching'ono apa chimene chinaperekedwa kwa ine. Ine ndikukhulupirira pakhala pali kuwonjezekera kwa chiwerengero chikhaliireni ine kuno komaliza. Ine ndikuganiza dzina lake ndi—ndi . . . lotsiriza, dzina la abambo ake, David West. Ndipo tiri ndi mnyamata wamng'ono apa amene akufuna kuti amupereke kwa Ambuye. Nkulondola uko? Kodi izo ndi usikuuno, kapena zinachitika Lachitatu usiku? Ine sindikudziwa. Izo ziri . . . Usikuuno? Izo ziribwino. Chabwino, nanga bwanji . . . Inu ndi David, si choncho? Ndi chimene ine ndimaganza kuti inu munalali. Chabwino. Bwanji mumubweretse mnyamata wamng'onoyo kuno?

Ngati mlongo wathu angabwere kuno pa limba iyi, ndi kudzatipatsa ife nyimbo ya *Abweretseni Iwo Mkati*. Abusa, ngati iwo angathe, mubwere kuno, ndipo tidzamupereke mnyamata wamng'ono uyu kwa Ambuye. Tsopano, ife timayesetsa kuzisunga izo Mwamalemba.

¹⁷ Uyu ndi mdzukululu wanu, M'bale West. Sizikuwoneka ngati ndi choncho, ndi choncho? Mlongo West, inu mukuganiza chiyani za zimenezo? Si choncho izo . . . Inu mukudziwa chimene ine ndikuganiza, ngakhalebe? Inu mukudziwa, ndine agogo, nanenso.

Izo zikundikumbutsa ine za M'bale Demos Shakarian. Iye anali ataima pamaso pa gulu lalikululu la anthu. Iye amasokoneza chirichonse monga mmene ine ndimachitira, inu mukudziwa. Iye anali ataima pamenepo. Iye anati, "Inu mukudziwa," anati, "Ine—ine ndinamuuza Rose, ine ndinamverera," ameneyo ndi mkazi wake, anati, "ndinamverera wokalamba kwambiri chikhaliireni agogo aakazi." Iye anati, "Ayi. Ine ndimatanthauza agogo- . . ." Inu mukudziwa, ine . . .

¹⁸ Inu simuli nokha, M'bale West. Tiripo ambiri a iwo muno. Ndipo izo ziri bwino. Ine ndikuganiza ife tikhoza kuziyamikira kwenikweni zidzukululu zathu. Izi sizi . . . Ndikuyembekeza kuti izi sizikumveka moipa. Koma ife timakhala ndi nthawi yochulukana ndi iwo, ine ndikukhulupirira, kuposa mmene ife tinkachitira ndi athu—ana athu. Ine ndinamufunsa mkazi wanga zimenezo, tsiku lina. Anati, "Ndithudi. Iwe umawakonda iwo kanthawi pang'ono, nkuwabwezera iwo kwa amayi awo, nkumapitirira."

¹⁹ Chabwino, ine ndiri ndi mdzukululu wamwamuna wamng'ono kumbuyo uko. Iye anati, "Papa, akulalikira. Papa, akulalikira." Ndipo iwo anatenga chopereka usiku wapitawu Lamlungu, ndipo icho chinali chiri pa tebulo. Iwo anadzamulowetsa iye, kumbuyo uko, ndipo—ndipo iye anandimva ine kudzera pa maikofoni. Iye anati, "Papa, akulalikira. Papa, akulalikira."

Ndipo Billy anati, “Inde, ali pansanja *apo*.”

Iye anati, “Ayi.” Ndipo choperekacho anachimwaza pansi ponsepo. Iye—iye amafuna kuti abwere kuno, inu mukudziwa. Ndipo iye nthawizonse amangondifuulira ine, mukudziwa, akandiwona ine pa msonkhano uliwonse. Iye amafuula, “Papa, akulalikira.” Anafuula mokuwa ndithudi. Chotero ine ndikudziwa iwo ndi okongola.

Ndimati, ine ndikudabwa ngati ine ndingabwereke lina la tsitsi limenero? Iye sakulisowa ilo tsopano. Ine ndikulisowa. Dzina lake ndi ndani? [Mlongo West akuti, “David Jonathan.”—Mkonzi]. David Jonathan. Kodi limenero si dzina lokongola? Chabwino, ine ndikuyembekeza moyo wake udzafanana ndi dzina limene iye watchulidwalo. David, mfumu, David; yemwe, Khristu adzakhala pampano wake; ndiponso Jonathan, mzake wokonedwa. Ine—ine ndikukuuzani inu, iwo ndi anyamata aang’ono okonedwa. Iye timawayamikira iwo, kwambiri. Ine...Iye akudzuka. Ndipo iye akhoza—iye akhoza kufuula “ameni” mwabwino monga ena onse a iwo, inu mukudziwa, chotero ife sitilola kuti izo zitisokoneze ife. Iye tikumupereka iye kwa Ambuye.

Ine ndikuganiza izo ndi zokoma kwambiri, kukhala ndi banja laling’ono, limene Mulungu waika muchisamaliro chawo mnyamata wamng’ono ngati uyu, ndipo nkubwera kudzamupereka iye kwa Ambuye. Ndipo pamene inu muchita zimenezo, izo zimawonetsera kuti inu simuli...kuti inu mukubwezera kwa Mulungu icho chimene Mulungu anapereka kwa inu. Mulungu amudalitse iye.

Tsopano, ngati inu mukufuna kuti mumunyamule iye, ine ndikukhulupirira mwinamwake amayi ake akhoza kumunyamula iye mwabwino pang’ono kuposa mmene ine ndingamunyamulire. Ndipo bwanji ife tingoika manja pa iye? Kodi inu mungasankhe kuti muchite zimenezo? Chifukwa, ine ndikuwopa kuti ndikhoza kumugwetsa iye kapena, osati kumugwetsa iye, kumuswa iye kapena chinachake chimzake, inu mukudziwa. Ndipo ine nthawizonse ndimawopa kuwaswa iwo, inu mukudziwa. Wanga—wanga... .

Meda anati, kumbuyo uko... .Ine ndikuganiza iyi ndi ntchito imodzi pa guwa imene iye amakhala ngati amandisilira nayo ine, inu mukudziwa. Iye amakonda kuwayangata a... .

Chabwino, yang’ana kuno, iye andiyang’ana ine. Iye ndi mnyamata wabwino. Inde, bwana. Mwinamwake ine ndikhoza kumunyamula iye. Ine ndikudabwa. Oh, mlongo, musatero... . ine ndikudalira kuti iye sagwa. Apa, kodi iye si wokongola? Wokongola? Iwe uli bwanji? Chabwino, tsopano, zokoma.

Tiyeni tiweramitse mitu yathu.

Ambuye Yesu, zaka zambiri zapitazo, pamene Chikristu chinkabadwa mmaonekedwe a Munthu wotchedwa Khristu,

Mesiya wodzozedwa, Dzina Lake anali Yesu. Anthu amabweretsa makanda awo kwa Iye, kuti Iye adzayike manja Ake pa iwo ndi kuwadalitsa iwo. Ndipo Iye anati, “Lolani ana aang’ono adze kwa Ine, ndipo musawaletse iwo ayi, pakuti wotere uli Ufumu wa Kumwamba.” Banja lokoma laling’ono ili, azigogo awo ndi iwo akhala otsatira owona a Mawu.

Ambuye Yesu, ine ndikumubweretsa, ndipo ndikumuyangatira kwa Inu, usikuuno, abusa ndi ine, David Jonathan West wokoma wamng’ono uyu. Ine ndikumupereka iye kwa Inu, kuchokera kwa amayi ndi adadi. Ine ndikumupereka iye kwa Inu, Ambuye, kuti akhale ndi thanzi, mphamvu, moyo wautali wa utumiki, kuti akalemekeze Mulungu Wamphamvuzonse, Amene anamubweretsa iye kubwera mu dziko lino. Mulole madalitso a Mulungu akhale pa iye. Mulole Mzimu Woyera ukhale pa mwana uyu. Ngati mawa ati adzakhalepo, mulole iye adzanyamule Uthenga umene makolo ake ndi azigogo ake akuwuchengeta kwambiri lero. Perekani izi, Ambuye. Tsopano, mu Dzina la Yesu Khristu, ine ndikukupatsani Inu mwana uyu, mu kuperekedwa kwa moyo wake. Amenii.

Ine ndikukhulupirira kuti iwo akufuna kuti atenge chithunzi cha mnyamata wamng’ono. [Kamera ikukhethemura—Mkonzi]. Ine ndinalumphu, inenso.

Mulungu akudalitseni inu, mlongo. Inu muziwakonda ndi kuwachengetera Ambuye Yesu nthawizonse, ndipo mnyamata wamng’ono akakuzidwe mu kuwopa Mulungu, ndipo mudzakhale ndi mnyamata wamng’ono wodabwitsa. Ine ndikutsimikiza. Mulungu akhale nanu.

Ine ndikukhulupirira iye anagwetsa choseweretsa chake chaching’ono? Iwo anachitola icho? Oh, mai!

Tsopano tiyeni tiimbe nyimbo yaying’ono ija, *Abweretseni Iwo Mkati*. Aliyense, pamodzi tsopano, chifukwa cha mnyamata wamng’ono. Chabwino, mlongo.

Bwezatu, bwezatu,

Bwezatu anawo kwa Yesu.

²⁰ Ine sindikudziwa manja abwinoko oti nkuwaikamo iwo. Inu mukuwadziwa? Manja a Ambuye Yesu!

²¹ Tsopano, ine ndikudziwa kukutentha kunja uko. Ine ndikufuna ndinene kwa woyang’anira pa malo, mchimwene wanga, Doc, kapena winayo, iwo amene amasalira izo. Alongo ena akuipitsa masiketi awo ndi—ndi mafuta amene ali pa mpando. Ndi angati amene apakidwa ndi iwo? Ine ndikudziwa, pali mkazi wanga, ana anga aakazi awiri, Betty Collins wamng’ono, Akazi a Beeler, ena a iwo. Ndi chinachake, mafuta pamenepo. Ngati inu mungayang’anitsitse izo, Doc, pamene inu mungathe. Ndizo, ine ndikukhulupirira, ndizo pamene iwo. . . Ndi mafuta kapena penti, kapena chinachake,

pamene iwo akugwira ntchito, mmipandoyo. Ndipo si choncho? [M'bale Edgar "Doc" Branham akuti, "Palibepo mafuta pa iyo, oti tichotsepo."—Mkonzi]. Chabwino, ine—ine sindikudziwa chimene izo ziri, ndiye. Chinachake ine basi. . . Zinanenedwa kwa ine, ndipo ine ndinati ine ndikazitchula izo kwa—kwa Doc. Chabwino.

Tsopano, msonkhano wa pemphero wa Lachitatu usiku. Ulipo uliwonse? Inu munalengeza? Inu mwapanga zolengeza zanu, M'bale Neville? Zolengeza zonse zabwera.

²² Tsopano, ngati Ambuye alola, Lamlungu likubwerali mmawa, ine ndikufuna kuti ndidzayankhule pa phunziro la kuwutsutsa m'badwo uno chifukwa chomupachika Khristu. Inu mukuti, "M'badwo uno sukanachita zimenezo." Ife tidzapeza ngati iwo anatero, kapena ayi, molingana ndi Mawu. Tsopano, Lamlungu likubwerali mmawa, ngati Ambuye alola. Ngati, tsopano, ngati—ngati—ngati chinachake chingachitike. . .

²³ Ine ndikuyenera kukakhala ku Houston sabata ino, aponso, mu msonkhano waukulu, umene ukanditengere ine mpaka Lamlungu, chotero ine sindikudziwa ngati ine ndidzakwanitse kapena ayi. Koma ife tiri ndi ma Lamlungu angapo oti tizipitirira, izo zisanafike, mulimonse. Kenako ife tizidzapita ku Chicago ku msonkhano waukulu, kapena msonkhano mu Chicago, sabata lomaliza mwezi uno. Ndipo kenako ine ndidzayenera kuti ndidzatengere banja langa kubwerera ku Arizona, pakuti—pakuti tchuthi chawo chatha ndipo ana akuyenera kuti azibwerera ku sukulu.

²⁴ Tsopano, ndi angati anasangalala ndi kuwerenga kwa Mawu, ndi madalitso a Ambuye? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi]. Ife tonse tinatero, mopambana kwambiri.

²⁵ Tsopano, kukutentha, ndipo ine ndikudziwa ena a inu muzibwerera kwanu usikuuno. Ine ndikudziwa M'bale Rodney ndi Charlie, ndi iwo, akuyenera kuti ayendetse mitunda yaitali. Ndipo dikirani miniti, inu muli pa tchuthi, sichoncho inu? Chabwino, ine ndamva kuti inu mukukawedza.

"Ambuye samamuikira munthu nthawi pamene iye akuwedza. Iwe sumakalamba mulimonse pamene iwe ukuwedza." Chotero, tsopano, atsikana inu muzipita nawo iwo. Mukuona? Ndipo ine ndidzabwera ndi kudzakujowinani inu, ngati ine ndingathe. Ndipo inu mukudziwa, "Ambuye wabwino," iwo anati, "samamuikira nthawi munthu pamene iye wapitia kokawedza." Muzichita zochuluka za izo pamene inu—pamene inu mukuzimva kuti mwabalalika. Ndi chinthu chabwino kukapumulirako mofatsa, chimene ine ndinayamba ndachipezapo mmoyo wanga, ndicho kupita kokawedza.

²⁶ Ine ndinali ndi khadi yaying'ono, nthawi ina, yochokera kwa Bambo Troutman. Alipo amene akuwakumbukira Bambo Troutman, kampani ya aisi mu New Albany? Iye anali ndi

khadi laling'ono kumeneko, imati, “Ndapita kokawedza.” Ndi kumapitirira, kumati, “Munthu amene ali ndi . . . Mwamuna aliyense, azibale ake, azipita kokawedza. Akakhala ndi dzanja lothandiza iye nthawizonse adzathandizira, kuwedza.” Anali ndi pafupifupi zinthu eyiti kapena teni zosiyanasiyana. Kenako pamene iye anafika mmusi pansu, anati, “Munthu amakhala pafupi ndi Mulungu pamene iye ali kokawedza.” Chotero ine ndikuganiza izo ndi zolondola ndithu. “Olemera ndi osauka onse amakhala chimodzimodzi, akamakawedza.” Mukuona? “Nthawizonse amathandizira, pamene akukawedza.” Ndipo chirichonse chimati, “Ndapita kokawedza.”

²⁷ Chabwino, ine ndikuuzani inu kuwedza kwina kumene ine ndakhala ndikuchita kwa pafupifupi zaka sate firii zapitazi, kwakhala kuli kuwedza miyoyo ya anthu. Ambuye atithandize ife kuti timupindulire aliyense amene ife tingampeze.

²⁸ Tsopano, usikuuno, izi akujambula. Tsopano, mmawa uno, (ngati Jim ali pano, kapena akujambula), ine—ine ndikuganiza, pa tepi, winawake anaitanira tcheru changa kwa izo, ine ndinati, “Kutuluka kwachiwiri.” Ine sindimatanthauza *kwachiwiri*. Izo ndi, “Kutuluka kwachitatu.”

Mzimu Woyera mmawonekedwe a Lawi la Moto, Mulungu kutsika mmawonetseredwe, anatulutsa kutuluka koyamba, ndipo—ndipo mmbuyo mu . . . anamutulutsa Israeli kuchokera ku Igupto.

Kutuluka kwachiwiri kunali Khristu akuwubweretsa Mpingo kuwuchotsa ku Chiyuda.

Ndipo, *Kutuluka Kwachitatu*, ndi pamene Lawi la Moto lomwelo likumuchotsa Mkwatibwi kuchokera mu mpingo. Mukuona? Kumuchotsa ku chathupi; kumuchotsa ku chauzimu; ndipo Chauzimu kuchokera kwa chauzimu. Zitatuzo, mwaona, Chauzimu kuchokera mu mpingo, kani. Tikatero ife tiri nazo zitatuzo, mibadwo itatu ya izo.

²⁹ Tsopano, usikuuno, ine ndimafuna kuti ndipange tepi ina, ndipo iyo ikutchedwa: *Kodi Moyo Wanu Ndi Woyenera Uthenga?* Mwinamwake sititenga nthawi yaitali kwambiri. Chabwino, basi Malemba angapo ndi zolemba zimene ine ndiri nazo apa, koma poyamba ife tikufuna kuti tiwerenge Mawu a Mulungu. Ife tisanachite zimenezo, ife tingoweramitsa mitima yathu kwa Iye kwa kamphindi.

³⁰ Ambuye Yesu, mwamuna aliyense, mwathupi, kapena mkazi, kapena mwana, akhoza kutsegula masamba a Baibulo ili, koma palibe aliyense amene angathe kuwulula Ilo koma Inu. Ine ndikupemphera, Ambuye, pamene ndikutenga mutu uwu monga waikidwa pa mtima panga kuti ndiwutumize kupita ku mafuko, kwa anthu, kuti iwo akakhoze kudziwa mtundu wa moyo umene ukufunikira kwa iwo kuti aziwukhala. Pakuti, ambiri amandifunsa ine, “Kodi Moyo wa Chikhristu ndi moyo wopita ku

tchalitchi? Kodi ndi kuthandiza osauka, osowa? Kapena kodi ndi membala wosajombajomba? Kodi ndi kuzipereka kokhulupirika ku mpingo?” ndi mafunso oterowo. Atate, mulole yankho lolondola libwere usikuuno, kudzera mmawu awa, pamene ife tikuyesetsa kuti—kuti tiwabweretse iwo kwa anthu. Mu Dzina la Yesu Khristu, ife tikupempha izi. Amen.

³¹ Tsopano mutsegule mu ma Baibulo anu, ku Bukhu la Luka Woyera, ndipo ife tiyambira pa mutu wa 14 ndi ndime ya 16, kuti tiwerenge Malemba angapo ngati poyambira, kwa maziko, a ichi chimene ife titi tiyesere kuti tichiike pafupifupi maminiti sate mpaka forte. Tsopano, ndime ya 16 ya mutu wa 14 wa Luka Woyera.

Kenako anati iye kwa iye, Munthu wina anakonza mgonero wawukulu, ndipo anaitana ambiri:

Ndipo anatumiza antchito ake nthawi ya mgonero kuti akanene kwa iwo amene anaitanidwa, Bwerani; pakuti—pakuti zinthu zonse tsopano zakonzedwa.

Ndipo iwo onse ndi mtima umodzi anayamba kupereka tizifukwa. Woyamba anati kwa iye, ine...ndagula malo, ndipo ine ndikuyenera kupita kukawawona iwo: ine ndikukupemphani kuti musandiwerengere ine.

Ndipo wina anati, ine ndagula magoli asanu a ng’ombe, ndipo ndikupita kukaziyesa izo: ine ndikupempha kuti inu musandiwerengere ine.

...wina anati, ine ndakwatira mkazi, ...chotero ine sinditha kubwera.

Chotero wantchitoyo anabwera, ndipo anawaonetsa ambuye ake zinthu zonse izi. Kenako ambuye wanyumbayo pokhala wokwiya anati kwa wantchito wake, ...

Zindikirani, si antchito. “Wantchito.”

...Pita kunja mwamsanga mmisewu ndi mmakwalala, ndi mmizinda, ndipo ukabweretse osauka, ndi olumala, ndi opinimbira, ndi akhungu.

Ndipo wantchitoyo anati, Ambuye, ndachita monga inu mwalamulira, ndipo komabe muli malo.

...ambuye anati kwa wantchitoyo, Pita kunja mmisewu yaikulu ndi mmalire, ndipo ukawakakamize iwo kuti abwere, kuti nyumba yanga idzadzze.

Pakuti ine ndinena ndi iwe, Kuti palibe mwa anthu awa amene anaitanidwa adzalawe mgonero wanga.

³² Tsopano, kodi inu munazindikira, panali zikoka zitatatu, kapena kuitana kutatu, kwa izo? Pamene iwo anapita, poyamba, ndi kukaitana iwo amene anali, kapena, anaitanidwa kuti

abwere, ndipo iwo sanachite izo. Chotero apo panadzapita msonkhano wa machiritso, anapita kukatenga akhungu ndi opinimbira. Ndipo komabe malo anali alipobe, chotero iye anapita ndipo anawakakamiza abwino, oyipa, ndi osayanjanitsika; iwo abweremo.

³³ Tsopano, inu mumawerenga fanizo lina la izi, chinachake mwa dongosolo limenelo, mu Mateyu 22:1 mpaka 10, ngati inu mungakonde kuti mudzawerenge izo, nthawi ina. Koma ine—ine ndinatenga mutu uwu kuchokera pamenepo: *Kodi Moyo Wanu Ndi Woyenera Uthenga?*

³⁴ Tsopano, Yesu apa akuti. . . Munthu nthawizonse wakhala akuyesetsa kuti awiringule, kuti asalandire Mawu a Mulungu a kuitana Kwake. Ngakhale zitakhala kuti zatsimikiziridwa motsindika kwa iwo, kuti ndi—kuti ndi Mgonero Wake ndi kuitana Kwake, koma munthu mowirikiza amakhala akuwiringula. Ndipo ngati inu mungawerenge Mateyu Woyera 22, inu mudzapeza kuti kuwiringulako kunapangidwa pamenepo, aponso. Ndipo—ndipo iwo amayesetsa. . .

³⁵ Izo zinapita mmibadwo yonse. Zinapita mu m’badwo, ndipo anati mwamuna anawaitana iwo, ndipo—ndipo anali ndi munda wa mpesa. Ndipo ife tikupeza fanizo limenero. Ndipo mmene iye anawatumizira antchito ake kuti akatenge kuchokera mmunda wake wa mpesa. Wantchito woyamba amene anabwera, kodi iwo anachita chiyani? Iwo anamuthamangitsa iye. Wantchito wotsatira anabwera, iwo anamugendanso iye. Ndipo iwo anakhala akumuthamangitsa wantchito ndi watchito; amuna ankhanza. Mfumu potsiriza, inatumiza, mwana wake. Ndipo pamene mwana wake anabwera, ife tikupeza, kuti, “Iwo anati, ‘Uyu ndi wolowa. Ife timupha iye, tikatero ife titenga zinthu zonse.’” Kenako Yesu anati kwa iwo, “Mfumu inatumiza ndipo anakapha ambanda awo, ndipo anakawotcha mizinda yawo.”

³⁶ Tsopano, ife tikuwona, pamene Mulungu amuitana munthu, kuti akachite chinachake, kapena kuti alandire kuitana kumene Iye wamupatsa iye, ndipo iye nkukana, ndiye palibe chimene chimatsalira, chifundo chikakanidwa, koma chiweruzo. Ngati inu mudutsa malire a chifundo, ndiye kuti pali chinthu chimodzi chokha chimene chimatsalira, ndipo chimenecho ndi chiweruzo. Ndipo ife tikupeza kuti munthu wachita zimenezo mmibadwo yonse. Izo zakhala zikuchitika, pafupifupi m’badwo uliwonse, mu Baibulo.

³⁷ Pamene Mulungu anamutuma Nowa, wantchito Wake, ndipo napanga njira yothawirapo kwa anthu onse amene ankafuna kuti—kuti apulumutsidwe. Koma anthuwo anangomuseka ndi kumunyoza Nowa. Koma Mulungu anapanga njira, koma iwo anali ndi chowiringula. Izo sizinali molingana ndi kawo—kaganizidwe kawo kamakono. Izo sizinatero. . . Izo sizinali

mmene iwo anakazifunira izo, chotero iwo anawiringula mmasiku a Nowa.

³⁸ Iwo anawiringula mmasiku a Mose. Iwo anawiringula mmasiku a Eliya. Iwo anawiringula mmasiku a Khristu. Ndipo iwo akuwiringula lero.

³⁹ Tsopano, Iye akuyankhula molunjika kwa Israeli, iwo amene anaitanidwira ku phwando, zimene ine ndikhoza kuziikanso lero kwa anthu, mpingo, amene aitanidwa kuti abwere ku phwando, ndipo sakuchita izo, phwando lauzimu la Ambuye. Ndipo iwo akulephera kuchita izo. Iwo sakufuna kuti achite izo. Iwo ali ndi zinthu zina zoti azichita. Iwo akupeza zowiringula.

⁴⁰ Tsopano, ngati Israeli, zaka thuu sauzande zapitazo, akanavomereza kuitanidwa kumene iwo anapatsidwa, iwo sibwenzi ali mmene iwo aliri lero. Zaka thuu sauzande zapitazo, Israeli anakana kuitanidwa kuti abwere ku phwando la ukwati, ndipo iwo anakana izo ndipo anapita ku chiweringu. Koma, monga Yesu ananena, iwo anagenda ndi kupha aneneri amene anatomizidwa kwa iwo, powiringula, tsopano, kuwiringulako amapanga tsiku lililonse.

⁴¹ Iye tikupeza, mmasiku a Yesu, kuti Iye sanatero—Iye sanayanjane ndi wina aliyense wa iwo. Iwo anati, “Ndi liti limene Munthu uyu anapeza kuphunzira uku? Ndi sukulu iti imene Iye akuchokerako? Kodi Uyu si Mwana wa akalipentara? Kodi amayi Ake samatchedwa Maria? Kodi abale Ake si, Yosefe ndi Yakobo, ndi ena otero? Ndipo kodi alongo Ake sali ndi ife? Ndiye ndikuti kumene Munthu uyu anatenga ulamuliro uwu woti azichitira izi?” Mukuona? Mwakuyankhula kwina, Iye samayanjana ndi iwo. Chotero iwo anati, “Iye ndi Bezezebule. Iye ndi Msamaria. Iye ali ndi chiwanda, ndipo Iye ndi wamisala. Iye ndi—Iye ndi. . . Iye ndi Munthu yemwe ali ndi mzimu woyipa, ali wa chipembedzo, ndipo wamupangitsa Iye misala. Ndipo ndi zimenezo. Iye akumayenda uko ngati munthu wamisala. Inu musamamusamale Iye.” Ndipo ife tikudziwa zimene zinachitika kwa Israeli. Ndipo iwo anafuula. Iwo anali otsimikiza kwambiri kuti Munthu ameneyo amalakwitsa, mpaka, oh, pamene iwo anamuweruza Iye, iye anati—iye anati, “Mulole Magazi Ake akhale pa ife ndi pa ana athu.” Ndipo Iwo akhala ali pamenepo chiyambireni.

⁴² Yesu anali kuyesetsa kuti awauze iwo kuti zowiringula zawo ndi zimene zimapha aneneri, ndi zimene zimapha olungama amene amabwera. Iwo amavomereza tizikhulupiriro tawo timene anthu anali atawapatsa iwo, mmalo motenga Mawu a Mulungu. Ndipo, pochita zimenezo, anali atawapanga Mawu a Mulungu kukhala opanda mphamvu.

⁴³ Tsopano, inu mukuyenera kusankha kumati, mu izi, kuti *Ichi* ndi chifuniro cha Mulungu ndi chokhumba cha Mulungu, kapena mwinamwake chinachake chimene inu mwachiganizira,

chabwino kuposa chimene *Ichi* chiri. Tsopano, inu mukuyenera kutenga chimodzi kapena chinacho. Inu simungamtumikire Mulungu ndi mammoni. Ndipo inu mukuyenera kunena kuti, “Ichi ndi Choonadi,” kapena “Icho ndi gawo la Choonadi,” kapena “Icho si chonse Choonadi,” kapena “Icho sichinaikidwe pamodzi molondola,” kapena “Icho sichinatanthauziridwe molondola.”

Ndipo Baibulo linanena, kuti, “Mawu a Mulungu alibe kutanthauzira kwamseri.” Palibe wina aliyense akuyenera kuikapo kutanthauzira kwa Iwo, Iwo analembedwa basi mmene Mulungu akufunira kuti Iwo atanthauziridwe. Basi chimene Iwo akunena, Zimenezo, ndi zimene zikuyenera kukhala. Muzingowatenga Iwo mmene Iwo anayankhulidwira, mmene Iwo analembedwera Apa.

⁴⁴ Tsopano, iwo amavomereza tizikhulupiriro tawo. Iwo amawapanga malonjezo a Mulungu kukhala opanda mphamvu kwa iwo. Iwo amazilambalala Zimenezo. Iwo amazilumpho Izo.

⁴⁵ Tsopano, ngati Russia akanavomereza Mdalitso wa pentekoste, zaka sevente-faivi zapitazo, pamene Mzimu Woyera unagwa mu Russia, iwo sibwenzi ali achikominisi lero. Tsopano, zaka sevente-faivi zapitazo, iwo anali ndi chitsitsimutso chachikulu mu Russia. Mulungu anabwera pakati pawo, ndipo iwo anali ndi zitsitsimutso zazikulu, njira yonse mpaka mu Siberia. Ndipo kodi iwo anachita chiyani? Iwo anaukana Iwo. Ndipo lero, dzikolo linapita, ndipo mipingo siimakhala ndi tchalitchi, pokhapokha atapatsidwa chilolezo. Ndipo iwo awonongedwa mpaka ku chiweruzo. Asochera potsatira kukwiya kolusa kwa chikominisi uku; agulitsidwa kwa mdierekezi.

⁴⁶ Zaka fifite zapitazo, Mzimu Woyera unagwa mu England. Zitangotha zimenezo kunabwera George Jeffreys, ndi F.F. Bosworth, ndi Charles Price, Smith Wigglesworth, ankhondo aakulu amenewo a chikhulupiriro, zaka fifite zapitazo, ndipo anampatsa England chitsitsimutso cha Mzimu Woyera. Koma kodi iwo anachita chiyani? Iwo anawaseka iwo, anakawaika iwo mndende, anawatcha iwo amisala, ankaganiza kuti iwo achita misala. Mipingo inkawaletsa anthu kuti asabwere kudzawamvera iwo. Ndipo iwo anali kuchiritsa odwala, ndi kumatulutsa ziwanda, ndipo anachita ntchito zazikulu. Ndipo chifukwa chakuti England, ngati fuko, anakana Uthenga, ake—machimo ake amadziwika pa dziko lonse. Kulibeko nkomwe—fuko lachinyengo kwambiri mu dziko lonse, ngakhale kuphatikizirapo Rome ndi France, kuposa England. Ilo ndi mayi wa chinyengo. Komweko kumene Finney ndi ambiri a amuna opambanawo analalikirako, mu—Haymarket, ndi Charles G. Finney, ndi Wesley, ndi kumatsika mmusi, ndipo ilo linakana Izo.

47 Ndipo tsopano, ngakhale sabata lathali, kapena awiri, mu mapepala, inu mukapeza pamene amuna awo opambana afookera kwambiri ku—ku kugonana kwa akazi, mpaka akazitape anabwera. Ndipo wamkulu wawo anadzawapeza ochuluka ena a iwo. Magazini analemba zimenezo. Tchimo lawo la chisembwere, mu boma mwawo momwe, abzala dzina lawo lamanyazi kudutsa mdzikoli. Chifukwa chiyani? Iye anachikana Choonadi. Iye anali ndi chowiringula chake, ndipo iye wathedwa. England yense anasulutsidwa, ndi Mulungu, kalekale. Ngati . . .

48 America, zaka fifitini zapitazo, pamene chitsitsimutso chachikulu cha machiritso chinkapitirira kuchokera ku pentekoste, chinadzafalikira mu fukoli, ndipo kunadzachitika zitsitsimutso ku likulu, Washington, DC. Mapurezidenti, mapurezidenti achiwiri, anthu otchuka, akazembe; zinthu zazikulu zinachitika, akazembe ndi—ndi amuna anachiritsidwa. Monga, Congressman Upshaw anakhala wolumala kwa—kwa zaka sikisite-sikisi, ndipo iwo sakanakhoza kutembenuza nkhope zawo ndi kunena kuti izo sizinali chomwecho. Izo zinali pamaso pawo pomwe, koma iwo anazikana Izo.

49 Ndipo, usikuuno, ndi chifukwa chake fuko lino langokhala. Ilo lathedwa. Palibenso chiyembekezo kwa ilo, nkomwe. Ilo linadutsa mzere wa pakati pa chiweruzo ndi chifundo. Ndipo ilolasan khirama amene ilo liri nawo kuno, kuti lizilamulira fuko. Ndipo ilo lavunda, mpaka mkati. Ndale zake zavunda. Zikhalidwe za fuko lino zatsika kuposa chirichonse chimene ine ndingachiganizire. Ndipo kachitidwe kake ka chipembedzo ndi kovunda kwambiri kuposa makhalidwe. Ilo likusanduka, pochita izi, ilo tsopano ladzijowinita lokha, mipingo yonse iyi, ndi ya fukoli, yakalowa mu chitaganya cha mipingo, ndipo yatenga chiremba cha chirombo. Ndi chinthu bwanji! Chifukwa chiyani? Khristu anawapatsa iwo mwayi, “Bwerani ku phwando Langa,” phwando la pentekoste, zimene zimatanthauza “fifite.”

50 Pamene Mzimu Woyera unatsanuliridwa pa Russia, iwo anaitanidwira ku phwando la pentekoste, phwando lauzimu, ndipo iwo anaukana Iwo. England, Mzimu Woyera unatsanuliridwa pa iwo, ndipo iwo anawukana Iwo. America, Mzimu Woyera unatsanuliridwa pa iwo, ndipo iwo awukana Iwo.

51 Iye anaitana katatu. Katatu, Iye anawatuma, ndipo iwo sanamvetsere ku phwandolo. Kenako Iye anawatumanso, ndipo Iye anati, “Pitani ndipo mukawakakamize anthu amenewo kuti abwere. Gome likuyenera kuti likonzedwe. Gome lakonzedwa. Malo alipobe.” Ndipo ine ndikukhulupirira, kuti, mwinamwake, mwinamwake mkati mwa miyezi pang’ono ikubwerayi, kapena chinachake, kapena chaka, kapena chirichonse chimene icho chiri, Mulungu atumiza kugwedeza kwina kudutsa dzikoli, pakuti winawake akadali kunja uko, kwinakwake,

amene ali Mbewu yokonzedweratu, amene Kuwala kuyenera kukagwerapo, kwinakwake, kwinakwake mdziko. Fukoli, palokha, lapita.

⁵² Ine ndinali kuyang'ana mu magazini ya *Life* ya sabata ino; kumusi ku, chabwino, kumusi ku Little Rock, tsiku lina, kapena, kani, Hot Springs. Ndipo kumeneko ine ndinawona, ine ndikukhulupirira anali kazembe wa mzinda wa New York, ali ndi wina wokhala ngati wodzivula ku Honolulu, akuvina ndi iye. Tsopano . . . Ndipo apa, mmusi mwake, munali mwamuna wina wodziwika. Oh, ndi chamanyazi bwanji! Tayang'anani pa fuko lathu lero. Taonani chikhalidwe cha lathu—cha fuko lathu. Taonani kumene ilo lapita, momwe ilo lamilira motsika.

⁵³ Tayang'anani pa kachitidwe kathu ka chipembedzo lero. Zatheka bwanji kuti mipingo ingakhoze kulowa mu chikhalidwe chimene iyo ilimo tsopano? Ndi chifukwa chakuti iwo akana ndipo awukana Uthenga wa Mulungu, kuitanidwa kuti abwere ku phwando. Kodi inu mungautche moyo ngati umeneyo woyenera Uthenga? Inu mungautche moyo, umene ungakhazikitse ndi kumaloleza a—anthu awo kuti azichita zinthuzo, kumasuta ndudu?

⁵⁴ Tsiku lina, kumusi kuno, mpingo winawake, timu yaing'ono inayake yamasewero imasewera kuno pa bwalo, ndipo mnyamata wamng'ono wa mlamu wanga ndi wosewera woponya mpira wa imodzi ya matimuwo. Ndipo chotero iye anali kumeneko akuponya, ndipo kumeneko kunali timu ya mpingo imasewera. Ndipo kumeneko kunali abusa, ndi anyamata aang'ono awa pa bwalopo, akusewera. Ndipo abusawo amasuta ndudu pambuyo pa ndudu, mpingo woyandikana nafe kwenikweni kuno. Ndipo tangoganizani munthu . . . Ndipo ngakhale anthu amene anakhala mwa omvetsera anaziwona izo. Koma izo zafika pakuti iwo sakusamala nkomwe za izo.

⁵⁵ Mpingo winawake waukulu, mpingo wa Baptisti, umene ine ndimawudziwa, umaloleza mpingo kutuluka kaye Sande sukulu, maminiti fifitini owonjezera, kuchitira kuti abusa ndi onse a iwo akakhoze kuima panja ndi kumakasuta, iwo asanabwerere kuti adzatumikire ntchito ya Ambuye. John Smith, woyambitsa wa mpingo umenewo, anapemphera molimba, kuti Mulungu atumize chitsitsimutso, mpaka maso ake anatupa nkutsekeka usiku, ndipo mkazi wake ankachita kumutsogolera iye pa tebulo ndi kumakamudyetsa iye ndi supuni. Ngati . . . Mwamuna ameneyo angadzuke mmanda ake ngati iye atadziwa kuti mpingo wafika mu chikhalidwe chimenecho. Ndi chiyani chimenecho? Iwo anaitanidwa kuti abwere, ndipo anakana izo. Ndi cho chinthu chokhacho. Ndipo inu mukukumbukira, Yesu anati, apa, kuti iwo amene anaitanidwa, ndipo anakana kuitanidwako, sadzalawa nawo mgonero Wake.

⁵⁶ Pamene Mulungu atumiza Mzimu Woyera ndi kukagogoda pa khomo la munthu, ndipo iye mwadala nkuwukana Iwo, nthawiina iye adzawukana Iwo kwa nthawi yake yotsiriza, ndiyeno inu simudzakhala munthu wa mwayi. Inu mukhoza kukhala mu tchalitchi ndi kumamvetsera Uthenga, ndipo nkumagwirizana nawo Uthengawo. Inu mukhoza kuchita zochulukana monga ngati, “Ine ndikudziwa Iwo ndi woona,” koma osaika konse chala pa Iwo, kuti muwuthandizire Iwo, inumwini. Mukuona? Inu kumangomvetsera kwa Iwo, chifukwa inu mukuti, “Ine ndikukhulupirira Iwo ndi woona.” Kumeneko ndi kungowumvera Iwo chisoni.

Ine ndikhoza kunena kuti, “Ine ndikukhulupirira *amene*wo ndi madola teni sauzande.” Zimenezo sizikunthauza kuti ine ndiri nawo iwo. Mukuona? Ine ndikhoza kunena kuti, “*Amene*wo ndi madzi abwino ozizira,” koma nkukana kuti ndimwe iwo. Inu mukudziwa chimene ine ndikutanthauza?

Ndipo uwu ndi Moyo Wamuyaya. Ndipo kukana kuchita izo, tsiku lina inu mudzadutsa mzere wa pakati pa chiweruzo ndi chifundo, ndiyeno inu simudzakhalanso ndi mwayi wobwera ndi kudzawulandira Iwo.

⁵⁷ Kwa anthu inu amene mumabwera kuno. Ine ndiribe choyankhira pa iwo amene... kapena—kapena amene atumiki ena amawayankhula. Koma, ngati Iwo ali olondola, moyo wanu ukhale kwa Iwo. Kodi ndi chiyandinso chimene inu mungathe kuchipeza, chimene chingakhale chopindulitsa kwambiri kwa inu, kuposa kudziwa kuti inu mukhoza kukhala ndi Moyo Wamuyaya?

⁵⁸ Nanga bwanji ngati ine ndikanakhala kuti ndikupereka makapisolo kuno, amene, zatsimikiziridwa mwasayansi, zatsimikiziridwa mwasayansi kuti kapisolo iyi ikhoza kukupangitsa iwe kukhala moyo zaka sauzande? Chabwino, ine—ine ndingachite kukatenga gulu la asirikali kuno, ndi kumachita kuwankhira iwo kutali kuwachotsa pamalopo. Iwe sungachite kuzipangira izo kuitanira anthu paguwa. Iwe ungamachite kuwamenya kuti iwo achokepo, kufuna kuti akhale moyo zaka sauzande.

Ndipo, komabe, zatsimikiziridwa mwasayansi kuti ndi Mulungu Wamuyaya, mphamvu Yake yonse ya chiukitsiro Chake, imene inakulonjezani inu Moyo Wamuyaya, ndipo Satana nkudzaika ziwanda zake kunja uko ndi kumakukanizani inu kuti musafike kwa Iwo. Mukuona? Komabe, inu nkumakhoza kupenya, ndipo moganiza bwino nkuyang’ana pa nkhope kumene ya Iwo ndipo nkuwawona Iwo kuti ndi owona, koma kenako nkuwakana Iwo. Mukuona?

⁵⁹ Chinachake, mtundu wina wa kuwiringula. “Kwatentha kwambiri. Ine ndatopa kwambiri. Ine ndidzatero, mawa.” Basi mtundu wina wa kuwiringula, ndizo zonse zimene iwo amachita.

Pokana tsiku lakuchezeredwa, izo zimakulekanitsani inu kwa Mulungu.

⁶⁰ Tsopano, ife tikuzindikira. Ndipo, mu Chipangano Chakale, iwo ankakhala ndi chimene ankachitcha chaka cha chikondwerero. Apo pamakhala pamene anthu onse, amene anali akapolo, amakhala amfulu pamene lipenga lachikondwerero lalira. Ndiyeno ngati munthu sapita, ngati akhala ndi kuwiringula kwina kumene iye angapereke, kuti iye sakufuna kuti abwerere ku dziko la kwawo, zikatero iye amayenera kudindidwa m'khutu, ndi chisongole, pa nsanamira mu kachisi. Ndiyeno zinalibe kanthu kuti ndi zikondwerero zingati zimene zingabwerepo, munthu ameneyo amakhala kuti anagulitsidwa. Iye sakanadzatha kudzabwereranso ngati mbadwa mu Israeli, nkomwe. Iye anachita chiyani? Iye anakana kuitanidwa kwake. Iye sankasowa kuti alipire kalikonse. Ngongole ya ukapolo wake imakhala kuti yatha. Banja lake limakhala mfulu. Iye amakhoza kubwerera ku dziko la kwawo ndi kukatenga zolowa zake zomwe. Koma ngati iye akana kuchita zimenezo, ndiye iye samawerengedwa nkomwe ndi Israeli, ndipo cholowa chake chimaperekedwa kwa wina.

⁶¹ Tsopano, chinthu chomwecho mu thupi chimafanana ndi chazimu. Kutu, ngati ife, ngati olova a Moyo Wamuyaya, ndipo ife tikamva Uthenga ndi kudziwa kuti Iwo ndi woona, ndipo ife nkuwukana Iwo, ndipo nkukana kuchita izo kapena kumvetsera kwa Iwo, ife timatenga chiremba cha chirombo.

⁶² Tsopano, winawake anati, “Tsopano, padzakhala a—chiremba cha chirombo, icho chidzabwera tsiku lina.” Ndiroleni ine ndikuuzeni inu. Icho chinabwera kale. Mukuona? Mwamsanga pamene Mzimu Woyera unayamba kugwa, chiremba cha chirombo chinayamba kuchitika. Mukuona?

⁶³ Inu mumakhala ndi zinthu ziwiri zokha. Chimodzi cha izo, ndi, kuwuvomereza Iwo, ndiko kutenga Chisindikizo cha Mulungu. Kuwukana Iwo, ndiko kutenga chiremba cha chirombo. Kukana Chisindikizo cha Mulungu ndiko kutenga chiremba cha chirombo. Aliyense akumvetesa? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Kukana Chisindikizo cha Mulungu ndiko kutenga chiremba cha chirombo. Pakuti, Baibulo linati, “Onse amene sanasindikizidwe ndi Chisindikizo cha Mulungu anatenga chiremba cha chirombo.”

⁶⁴ Pamene lipenga lawomba, ndipo onse amene akufuna kumasulidwa amatha kupita. Iwo amene sakufuna, amadindidwa.

Tsopano, inu mukuona, chiremba cha chirombo, ngati ife titi tidzayankhule za icho mtsogolo, ndi pamene icho chiti chidzawonetseredwe, pamene iwe udzazindikire kuti ndi chimene iwe unachita kale. Mukuona? Ndipo chomwechonso ndi Mzimu Woyera, Iwo ndi wakuti udzawonetseredwa. Pamene

ife tidzawawona Ambuye Yesu akubwera mu ulemelero, ndipo nkudzamverera mphamvu yosandulitsa ija, ndi kudzawawona akufa akuuka mmanda, ndi kudzadziwa kuti mukutalika kwa kamphindi, ife tidzakhala titasinthika ndi kudzakhala ndi thupi ngati Lake. Izo zidzawonetseredwa. Kenako, nkudzawawona iwo amene anawukana Iwo, atasiyidwa pansu, kunjani.

⁶⁵ Kodi Yesu sananene kuti anamwali anatuluka kukakumana ndi Khristu? Ena a iwo anagona, ulonda woyamba, wachiwiri, wachitatu, wachinai, wachisanu, wachisanu ndi chimodzi, mpaka ulonda wa chisanu ndi chiwiri. Koma, mu ulonda wa chisanu ndi chiwiri, ndiye panadzabwera mfuu, “Taonani, Mkwati akubwera. Tulukani kuti mukakumane naye Iye.” Ndipo iwo amene anali akugona, anadzutsidwa. M’badwo wonse wa mmbuyo, mpaka ku Pentekoste, anadzuka. Mukuona? Kuyambira m’badwo wa chisanu ndi chiwiri, m’badwo wa mpingo wa chisanu ndi chiwiri, kudutsa njira yonse mpaka mmbuyo, anadzuka. Ndipo awa amene anali mu m’badwo wa mpingo uwu, amoyo, iwo anasinthidwa. Ndipo iwo anakalowa.

Pa nthawi yomweyo imene iwo anakalowa, namwali wopusa anabwera ndipo anati, “Ife tikufuna kuti tigule ena a Mafuta anu.”

⁶⁶ Koma iwo anati, “Ife tangokhala ndi otikwanira ifeeni. Pitani kwa iwo amene akugulitsa Iwo.”

“Ndipo pamene iwo anali kuyesetsa kuti alandire Mafuta awa, Mkwati anabwera.” Siinakhalepo nthawi mu mbiriyakale ya dziko, imene achi Episcopal, Baptisti, Methodisti, Presbateria...Mapepala adzaza. Mapepala achipembedzo akutamanda Mulungu, kuti anamwali opusa awo tsopano akuyesetsa kuti alandire pentekoste, akuyesetsa kuti alandire Mzimu Woyera. Ndipo kodi anthuwo sakuzindikira kuti izo sizichitika, molingana ndi Mawu a Mulungu? “Pamene iwo anali kuyesetsa kuti abwerere, Mkwati anabwera ndipo anadzamutenga Mkwatibwi. Ndipo iwo anakaponyedwa ku mdima wakunja, ku chiweruzo,” chifukwa iwo anakana kuitanidwa kwawo.

⁶⁷ Anthu onse aitanidwa kuti abwere. Mulungu, mu m’badwo uliwonse, amatumiza Kuwala Kwake, ndipo Iko kumakanidwa.

⁶⁸ Ndipo, tsopano, lero si losiyana ndi tsiku lina lirilonse, kukana tsiku la kuchezeredwa. Pamene Mulungu akuwuchezera Mpingo ndi anthu, mulandire Izo pamenepo. Musakane kuti mpaka chaka cha mawa, chitsitsimutso chotsatira. Oraloo ndi limenelo, “Lero ndi tsiku la chipulumutso.”

⁶⁹ Ndipo kumbukirani, Mulungu sanayambe watumizapo Uthenga, mu tsiku lirilonse, koma kuti Iye amawutsimikizira Iwo ndi chauzimu. Yesu anati, Iyemwini, “Ngati Ine sindikuchita ntchito za Atate Wanga, ndiye musandikhulupirire Ine. Koma ngati Ine ndikuchita ntchitozo, inu mukhulupirire

ntchitozo ngati inu simungandikhulupirire Ine,” ndipo pamene inu mukuziwona izo zikuwoneka bwinobwino ndipo—ndipo zikuwonetseredwa.

⁷⁰ Tsopano nthawi yafika yoti iye akuwukana Iwo, ndiye iye abowoledwa mu khutu ndi chisongole, zikatero iye sadzawumvanso Iwo nkomwe. Tsopano iye akudzitengera yekha kupita ku chitaganya cha mipingo, akupita ndithudi mpaka kukatenga chiremba cha chirombo.

⁷¹ “Chimodzi cha zokhumba chachikulu,” winawake wangondipatsa kumene ine pepala, papa watsopano uyu wanena kuti, “ali woti ayanjanitse mipingo pamodzi.” Iwo achita izo motsimikiza basi monga ine ndaima pano. Ndipo Achiprotestanti atsatira zimenezo. Mukuona? Chifukwa, mpingo...Baibulo linati, Paulo, mneneri wa Ambuye, anati, “Tsiku limenero silidzabwera pokhapokha padzabwere kugwa, kaye, ndipo kenako a...munthu wa tchimo asanaulidwe. Iye amene akukhala mu kachisi wa Mulungu, nkumadzikweza yekha, onse omwe ali pamwamba pa Mulungu; iye, ngati Mulungu,” kumakhululukira machimo pa dziko lapansi, ndi zina zotero. Mmene chinthu ichi chinachitikira! Koma izo sizidzachitika kufikira patadzakhala kugwako, kufikira mpingo udzayambe kuchoka ku phwando lauzimu, udzadzikokere wokha mmbuyo ndi kukadzipanga wokha bungwe. Zikadzatero ndiye kuti vumbulutso silinatsale ndi mpingo.

⁷² Kumbukirani, Israeli ankeyenda, usana ndi usiku, ndi Lawi la Moto. Pamene Lawi la Moto lija lasuntha, iwo ankasuntha nalo Ilo. Ndipo kumbukirani, Ilo limakhala Moto usiku, ndi Mtambo masana. Chotero Ilo limakhoza kubwera, masana kapena usiku, nthawi iliyonse. Koma, kulikonse komwe Ilo linali, kumeneko kumapangidwa chitetezero, kuti iwo asalephere kuliwona Ilo. Ilo limakhala Kuwala usiku, ndi Mtambo masana, ndipo iwo amalitsatira Ilo. Inde, bwana. Chinthu chomwe chomwecho!

⁷³ Martin Luther analiwona Ilo. Kodi iye anachita chiyani? Iye anatuluka mu Chikatolika. Koma kodi iwo anachita chiyani? Iwo anadzimangira mpanda waung’ono, anati, “Ndife Achilutera. Ichi ndi chimenechi.”

⁷⁴ Kenako Wesley analiwona Ilo likuyenda likuchoka kumeneko. Iye anapita. Kodi iwo anachita chiyani? Anazimangira izo mpanda waung’ono, anati, “Ichi ndi chimenechi.” Kodi Kuwalako kunachita chiyani? Kunasunthirabe chitsogolo, kenanso.

⁷⁵ Pentekoste analiwona Ilo. Kodi iwo anachita chiyani? Anatuluka mwa Achiwesley ndi Anazarene, ndi ena otero. Kodi iwo akuchita chiyani? Iwo akuzimangira izo mpanda waung’ono, wotchedwa, “Ife ndi aumodzi,” ndipo “Ife ndi autatu,” ndi “Ife

ndi a United,” ndi zonse izi. Kodi Iye anachita chiyani? Mulungu anangosamukamo mmenemo. Mukuona?

⁷⁶ Ife sitingathe kuchita zimenezo. Ife tikuyenera kutsatira, tsiku ndi tsiku, ora lililonse la tsiku, sitepe iliyonse ya njira. Ife tikuyenera kuti tizitsogozedwa ndi Ambuye Yesu Khristu. Ngati ife sititero, ife titenga moyo wachibungwe. Ndipo moyo umene sukumutsatira Khristu, tsiku ndi tsiku, si woyenera.

⁷⁷ Mwamuna yemwe amakhala Mkristu Lamlungu, ndipo akapita ku tchalitchi, amakhala kumbuyo uko ndipo kumaganiza kuti tchalitchicho ndi chake chifukwa iye amachita *ichi*, *icho*, kapena *chinacho*, ndipo Lolemba nkumakaba ndi kumakanama. Ndi akazi amene amapita ku gombe la chisawawa, ndi—ndi kumakayenda pa misewu, atavala zovala zopanda khalidwe!

⁷⁸ Ine ndimaganiza za—za mayi wa fukoli, samazipentapenta nkomwe, akamapita kwa a papa; ndipo akabwerako, ndi kudzayambitsa nthawi yometa phanke ya akazi mfukoli. Ndi madiresi onse awa, amenewo, pamene iye anadzakhala mayi, mkazi aliyense mdzikoli akufuna azivala imodzi ya madiresi achizimayi awa tsopano. Uko nkulondola. Ndi zitsanzo. Ndipo iwo amadziwa kuti anthu amenewo angachite zimenezo. Iwo amatsanzira mzimu wa mdziko. Ndipo zimenezo si za mu Mpingo wa Mulungu wamoyo.

⁷⁹ Akazi akuyenera aziyang’ana kwa Yesu Khristu. Inu mukuyenera kuyang’ana kwa Sarah ndi iwo aku Chipangano Chakale.

⁸⁰ Tsopano, iwo afika pakuti... Ine ndinali kulalikira usiku wina, kwina kwake, zokhudza akazi kuti azimvera amuna awo. Kumvera? Eya. Zimenezo zinachokamo mu mwambo wa m’banja, kalekale. Koma iwo sangachite zimenezo. Ayi, bwana. Iwo amakhala mu America, ndipo iwo amafuna kuti iwe udziwe zimenezo. Iwo sangamvere. Koma, ngati inu simukuchita zimenezo, musamayerekeze nkomwe kumadzitchula nokha Mkristu, chifukwa inu simuli. Ine sindikusamala kuti inu mumavina mochuluka bwanji ndi kuyankhula ndi malirime, ngati inu simukuwamvera amuna anu, inu mwachoka mu chifuniro cha Mulungu.

⁸¹ Mkazi amene amavala zazifupi ndi kumachita zinthu izi zimene iye amachita pa msewu, usadzitche wekha Mkristu. Iwe umafuna kuti ukhale ndi dziko ndipo koma uzigwirabe umboni wako. Iwe sungachite zimenezo Pamaso pa Mulungu, pamene iwe ukudziwa bwino kuti sukuyenera kuchita zimenezo.

⁸² Zindikirani, “amabowoledwa mkhutu,” amadindidwa, zikatero iwe sudzamvanso. Kumbukirani, chimenecho chimakhala chizindikiro cha kutsekedwa mmakutu. Iwe sudzalimvanso Ilo aponso. Iwe sudzamvanso. Iwe sudzathanso kenanso, kudzachitanso izo.

⁸³ Oh! “Iye sakhulupirira *Iwo*.” Oh, mai! “Musamuuze iye. Iye amakhulupirira izi.” Ayi. “Iye amakuuzani inu pomwepo. . .” Iye samawadziwa Iwo. Zingatheke bwanji kuti a—dona. . . Ndikungokufunsani inu, zingatheke bwanji dona. . .

Monga ine ndinayankhulira Lamlungu, Lamlungu lapitali usiku, sabata lapitalo usiku, pa “kuwala kothwanima kofiira,” mmene kuti—a—kuchita kwa akazi kwafika pokongola kuposa mmene kunayamba kwakhalirapo. Tsopano, izo si kanthu—sikuti ndikumutsutsa mkazi, tsopano, ndizo basi. . .koma momwe iye akuzilamulira izo. Mukuona? Chi. . .Iye ali chomwecho, kuti zimuike iye mu yesero, monga Eva anaikidwa pamaso pa mtengo.

⁸⁴ Munthu aliyense, mwana wamwamuna aliyense amene amabwera kwa Mulungu, amayenera kuti adutse ora ilo la kuyesedwa. Uno ndi m’badwo wa akazi, fuko ili liri, pamene iye akuyenera kudutsa mu kuyesedwa kumeneko. Ngati iye atakhala mkazi wokongola, ndipo nkumachita ngati mlongo, madalitso a Ambuye ali pa iye. Koma pamene iye angadzifikitse yekha po—pomadziwa izi, ndipo nkumakadziwonetsera yekha, mwamtheradi zimawonetsera kuti iye ali ndi—ndi mzimu woyipa pa iye. Iye samatanthauza kuti akhale mwanjira imeneyo, ine sindikuganiza, ambiri a iwo samatero. Koma iwo sakudziwa zimenezo.

⁸⁵ Kodi inu mungandiuze ine kuti mkazi, woganiza bwino angadziveke yekha, zovala zazing’ono izi zimene iwo akumavala kunja kuno pa msewu?

⁸⁶ Ine ndiri ndi atsikana awiri aang’ono akhala apa. Ine sindikudziwa kuti zidzawathera bwanji ana amenewo. Ine ndimangowapempherera iwo. Ana, lero, ine sindiri. . .Iwe sungadziwe. Ine sindikudziwa. Iwo si akuti sangachite zimenezo. Iwo akuyenera kudzaima pa mapazi awo awiri, pamaso pa Yesu Khristu, ndipo nkudzayankha. Iwo sangadzalowere pa chimene. . .pa—pa chimene ine ndimakhulupirira, ndi chimene amayi awo amakhulupirira. Ine sindimadziwa zimene iwo amachita. Koma ine kwenikweni ndikukhulupirira, mu ora lino, ngati atsikana amenewo atapita pa msewu, atavala zovala za mtundu umenewo, ndipo mwamuna nkuwapanga iwo chipongwe, ali mu zovala za mtundu umenewo, ine sindikukhulupirira, ngati ine nditakhala nawo mwayi, kuti ine ndingamadzudzule nkomwe mwamunayo. Zoono zimenezo. Ine ndingawadzudzule atsikanawo. Iwo samayenera kuti akachite zimenezo.

⁸⁷ Mvetserani. Ngati munthu angamaganize, ndi kumaphunzitsa kuti, “Munthu siwoposa chinyama. Iye anachokera ku mtundu wa zinyama.” Ndipo taonani, ndiye, inu mukamuike iye kunja uko monga. . .

⁸⁸ Inu mumamutengera garu kupita naye kwa wamkazi wamng'ono nthawi inayake, kudutsa mmipanda ndi china chirichonse, chifukwa wamkazi wamng'onoyo ali mu chikhalidwe chimenecho; nkhumba, ng'ombe, nyama ina iliyonse. Ndipo ngati ife tiri moyo wa chinyama; chimene, ife tiri, gawo lathupi. Ndiyeno pamene mkazi adziwonetsera yekha monga choncho, iye amatsimikizira kuti iye ali chinthu chomwecho chimene garu wamng'onoyo ali, kapena chinthu chomwe chomwecho, ndendende, chifukwa sibwenzi iye akuchita zimenezo. Iye amadziwa. Chirengedwe chimamuphunzitsa iye kuti mwamuna akamuyang'ana iye. Ndipo Baibulo linati, "Aliyense amene ayang'ana pa mkazi ndi kumusilira iye wachita naye kale chigololo mu mtima mwake."

⁸⁹ Izo zimaika nthawi yoyesedwa. Ndipo mdierekezi akuwakongoletsa akazi amenewo, ndipo akuwavula iwo, ndipo akumakawaika iwo kunja uko, kuti akakuyeseni inu. Amuna, muzitembenusa mitu yanu. Muzikhala ana aamuna a Mulungu. Akazi, inu muzivala ngati ana aakazi a Mulungu. Musadzayankhe za chigololo uko pa Tsikulo.

⁹⁰ Ngati mkazi ameneyo, ziribe kanthu kuti ndiwosalakwa chotani...Iye akhoza kukhala kuti sanayambe wapangapo cholakwika chirichonse, sanayambe wakhalapo nazo izo mmalingaliro ake kuti akachite zoipa. Koma pamene wochimwa uyo amene anayang'ana pa mawonekedwe abwino a mkazi uyo (podziwa kuti iye ndi mwamuna, ndipo chachikazi chimakhala mwa mmodzi...zokhudzira zimakhala mwa winayo, ndipo zamwamuna zimakhala mwa winayo), ndipo wochimwa ameneyo ayenera adzayankhe chifukwa cha izo pa Tsiku la Chiweruzo: Nndani anachita izo? Wolakwa adzakhala ndani? Si iyeyo. Inuyo. Ndi zimenezotu, kupanda khalidwe.

⁹¹ Tayang'anani pa fuko lino. Izo zinkachitika kuti, pamene iwo—iwo anali ndi madiresi ofika mmwamba mwa maondo amene akazi ankavala, ife tinkachita kutumiza ku Paris kuti abweretse iwo. Lero, Paris amabwera kuno kuti adzatenge iwo. Izo zafika ponyasa kwambiri mpaka Paris akulephera kukwanitsa izo. Nkulondola uko. Chonsecho...Bwanji? Kuwukana Uthenga. Bwanji?

Paris analibe Iwo. Iye ndi wani handiredi peresenti Chikatolika. Achiprotetanti amalephera ngakhale kuti akalowe kumeneko. Tamuwonani Billy Graham. Ine ndikuganiza muli Akhristu sikisi handiredi okha mu Paris yense, mwa mamilioni, Akhristu sikisi handiredi, Achiprotetanti. Amenewo si odzazidwa ndi Mzimu Woyera. Amenewo ndi mwamtheradi Achiprotetanti chabe, sikisi handiredi a iwo, kuchokera mwa mamilioni kuchulukitsa mamilioni. Iwo sanapeze mwayi woti awukane Iwo.

⁹² Koma anthu awa ali ndi Uthenga. Ndipo pamene iwo achoka ku Uthenga ndi Uthengawabwino umene iwo awuwona ukuwonetseredwa, nkumawusereula Iwo chifukwa chiphunzitsa china chakale cha wachiwerewere chawalukaluka iwo; ndipo m'busa wina ataima pa guwa, akuganiza mochuluka za dolla ndi tikiti ya chakudya kuposa mmene iye amachitira za moyo, anthu amene iye akuwalalikira, uko nkulondola, izo ndi zimene zachita izo. Tsopano iye akutsogolera dziko.

⁹³ Inu mukukumbukira, osati kale kwambiri, mu kachisi muno. Ine ndinalalikira pa phunziro, pafupifupi zaka twente zapitazo, “Ine ndikuwonetsani inu mulungu wamkazi wa America,” ndipo anali ndi wadama wamng’ono kuno, atakhala pamenepo ndi izo. Ndizo zimene izo ziri. Tsopano zafika pakuti, akulandira izo. Iwo akulandira zimene iwo anapempha. Ndipo iwo alandira izo. Ndizo zonse.

⁹⁴ Ayi. Iwo sakhulupirira izo. Ayi, bwana. Iwo amafuna kuti inu mudziwe kuti iwowo ndi mzika za America, ndipo iwo ali nawo ufulu wo—wochita mulimonse mmene iwo akufunira. Ine ndikungokhumba. . .

⁹⁵ Mundilole ine ndikuuzeni inu. Ine ndikuuzani inu tsopano. Ayi, bwana, ndale sizidzagwira konse ntchito. Ayi, bwana, demokalase siidzagwira konse ntchito. Demokalase yavunda, mpaka kufika pa fupa. Ngati iyo ikanamayendetsedwa pakati pa gulu la Akhristu, izo zikanakhala zabwino. Koma pamene inu mwakaiyika iyo kunja uko mdziko, izo zangosanduka kuyenda pa madzi wopanda nangula. Zoono ndithudi.

⁹⁶ Tayang’anani apa, lero. Chirichonse chikhoza kuchitika, ndipo basi iwo amangokhala. . . Chirichonse, akakokera ndale pang’ono, ndipo iwo sangamangidwe atapha munthu.

⁹⁷ Pamene ine ndinalalikira kumusi uko, usiku uja kuti ndikayesere kuti ndipulumutse miyoyo ya ana awiri aja. Iwo anali olakwa basi monga wolakwa angakhalire. Ngakhale woimira mlandu uja anandiimira kumbuyo kumeneko, ndipo iye anati, “Izo nzoona.” Iye anati, “Ine sindimakhulupirira kuchotsa moyo wa anthu.” Iye anati, “Ngati inu mungayang’ane pa zolembe zanu za zigawanga, ndi ndani amene amaphedwa pa mpando wamagetsi ndi zinthu? Si olemera. Iye amakhoza kukwanitsa kudzipezera womuimira mlandu ndi ziphuphu zina, tinjomba tina tauve, ndi magudumu ena *apa*, ndi zina *apo*, ndi kuchipanga chiphuphu chinthucho.” Iye anati, “Ndi ana osauka ngati amenewo, amene alibe ndalama zokwanira zoti akadzigulire chakudya chabwino, iwo ndi iwowo amene amalandira zimenezo. Amenewo ndi amene amawapha ndi magetsi, winawake amene ali ngati amene iwo amamutcha gulu la anthu osaphunzira, ndipo basi amangokakamirabe dzina la chilango chonyonedwa.”

⁹⁸ Ine ndinati, “Kupha koyamba kumene kunachitikapo mdziko, mchimwene mmodzi anamupha mzake, ndipo Mulungu sanachotse moyo wake chifukwa cha izo. Iye anaika chizindikiro pa iye, kuti pasakhale aliyense wakuti adzachotse moyo wake. Kulondola. Ameneyo ndiye Woweruza Wamkulu.”

Ndipo ine ndawona kuti anawachotsera chilangocho. Tsopano iwo akaimbidwa mulandu wina. Chifukwa, iwo akakhala moyo wonse tsopano, zimene ziti zidzakhale zaka leveni, ndipo mwinauwake adzatulutsidwa mwamsanga. Iwo ndi olakwa. Ndithudi. Iwo ndi olakwa. Iwo akuyenera kuti apititsidwe kokalangidwa, kwa moyo wawo wonse, koma osati awachotsera moyo wawo. Palibe munthu amene ali ndi ufulu wochotsa moyo wa munthu mzake. Ayi, bwana. Ine sindimakhulupirira zimenezo. Ayi, ndithudi.

⁹⁹ Oh! Iwo amati. . .Bwanji, iwo sakhulupirira kuti iwo ali kunja kwa chifuniro cha Mulungu, chifukwa ndizo zonse zimene iwo amazidziwa, zonse zimene iwo amafuna kuzimva. Iwo anatembenezira makutu awo motsutsana ndi Choonadi, kumeneko.

¹⁰⁰ Chomwechonso Igupto samafuna kudziwa kuti gulu lija la oyera adzigudubuza kumusi uko linali chifuniro cha Ambuye. Iwo akanafuna bwanji kuti adziwe kuti munthu wina wamisala anabwera kumeneko, akuchokera ku chipululu, ali ndi ndevu zikulendewela monga *chonchi*, ndipo anati, “Farao, ine ndabwera mu Dzina la Ambuye. Amasule ana amenewo?”

Farao nkudzati, “Ndani? Ine? Mponyereni iye kunja.” Mukuona? “Ine?”

“Ngati iwe suchita zimenezo, Ambuye Mulungu akantha fuko lino.”

¹⁰¹ Apobe, “Chidempete chokalambacho, mmasuleni iye azipita kwinakwake. Msiyeni iye azipita. Zikukhala ngati dzuwa laphika maganizidwe ake.” Mukuona? Koma izo zinabweretsa chiweruzo, chifukwa munthuyo anali mneneri ndipo anali ndi PAKUTI ATERO AMBUYE. Kulondola ndithudi. Iwo sanafune kuti akhulupirire zimenezo.

Rome sanafune kuti akhulupirire zimenezo, nayenso, koma izo zinachitika chimodzimidzi basi.

¹⁰² Israeli sanafune kukhulupirira kuti ameneyo anali Mesiya. “Iwo akanakwanitsa bwanji, gulu la—gulu la a Galileya?” Akuti, “Kodi onsewa si a Galileya? Kodi iwo akuchokera kuti? Kodi Iye amayenda ndi gulu la mtundu wanji? Osaukitsitsa kumene amene angasonkhanitsidwe pamodzi, ndiro gulu limene Iye amayanjana nalo. Amenewo ndi amene amabwera kudzamumvera Iye, ndi anthu osauka, anthu amenewo amene samadziwa kalikonse. Iwo si osankhidwa. Iwo siali—iwo si mtundu wa aluntha amene ife tiri. Iwo ndi gulu losauka.” Inu mumamva izo zikunenedwa za chitsitsimutso mu tsiku lino.

“Ndi gulu la mtundu wanji limene limakawamvera iwo? Ndi a mtundu wanji amene amapita ku misonkhano imeneyi? Kodi iwo ndi anthu a mtundu wanji?”

¹⁰³ Ine ndinamumva munthu akuti, osati kale kwambiri... Chabwino, iye anali ngati... Iye anali abambo ake a Hope omupeza. Ndipo ine ndinali kumuuzza iye za ubatizo wa Mzimu Woyera. Iye anati, “Tsopano, ndani angakhulupirire chinthu ngati chimenecho, pokhapokhapo mtundu wina wa gulu wonga iwe uli nawo kumeneko?” Iye anati, “Inu mukamulola *Wakuti-ndi-wakuti*, mwamuna wa malonda kuno mu mzinda, woyipa monga amakhalira onse, iyeyo akanena kuti walandira Mzimu Woyera, ndiye ine ndikhulupirira zimenezo.”

¹⁰⁴ Ine ndinati, “Musadandaule. Iye sadzanena konse zimenezo.” Mwamunayo anafa nthawi yomweyo, wopanda Mulungu. Mukuona?

Inu muzisamala zimene mukuchita. Muzisamala zimene mukunena. Inu mukufuna moyo woyenera Uthenga. Kulondola.

¹⁰⁵ Israeli sanakhulupirire zimenezo, gulu lija la anthu. “Wamisala uja, Dzina lake Yesu waku Nazareti, wobadwa,” iwo ankaganiza, “wobadwira pathengo.” Ndipo anthuwo amakhulupirira zimenezo. Chifukwa, iwo amati, “Ameneyo sanali wake. Bwanji, bambo Ake ndi a Yosefe, ndipo Maria anali woti akhala ndi Mwana uyu iwo asanati nkomwe... Anabadwa, bwanji, ndi wapathengo. Ndipo kodi Iye ndi ndani? Basi munthu wamisala. Ndi mmodzi wa anthu oseketsa aja. Musamapite kukamumvera Iye.” Kodi iwo anachita chiyani? Iwo anali akutumiza miyoyo yawo ku gehena. Iwo anatenga... .

¹⁰⁶ Yesu anati, “Asiyeni iwo okha. Ngati wakhungu atsogolera wakhungu, kodi awiri onse sagwera mu dzenje?” Uko nkulondola. Iwo samadziwa zimenezo. Iwo sakanakhulupirira Izo. Iwo sakanatero ayi.

¹⁰⁷ Iwo samatha kuwona kuti zingatheke bwanji kuti anthu ophweka aja ndi Uthenga wophweka, atakanidwa, zingapangitse fuko lalikulu kugwa nkukhala bwinja. Tsopano mvetserani. Iwo samatha kumvetsa kuti: gulu lofphweka, losadziwika, la wamba la anthu. Inu mukudziwa, Baibulo linanena kuti, “Anthu wamba ankamumva Yesu mokondwera.”

¹⁰⁸ Ine ndinali ndi chinachake chaching’ono chinachitika mu Mexico, osati kale kwambiri. General Valderna, wosankhidwa wa Mulungu, Kuwala kunamuwalira panjira yake kamodzi, mu umodzi wa misonkhano. Wankhondo wamkulu wa Chikatolika uja, mmodzi wa ankhondo aakulu mu Mexico, anabwera modzichepetsa ku guwa ndipo anadzalandira ubatizo wa Mzimu Woyera. Iye anabwerera ku Mexico. Iye anakhala akundilirira ine, kuti ndipite kumeneko. Potsiriza, ine ndinaganiza zopita kumeneko. Ambuye ananditsogolera ine; ndinali ndi

masomphenya. Ndinamuwuzwa mkazi wanga. Ndinapita kumusi uko.

Ndipo pamene iye anatero, iye pokhala mmodzi wa akulu awo ankondo, wamkulu wa nkondo wa nyenyezi zinai, iye anapita ku likulu, ku boma. Ndipo, iwo, iwo amatsutsana zolimba ndi Achiprotostanti kumeneko, inu mukudziwa. Chotero iwo ankadziwa kuti uwu ukakhala msonkhano wopambana, chotero iye anapita kumeneko ndipo anakatenga wolondera wachisilikari. Ndipo pamene iwo anatero, iwo anakapeza bwalo lalikululu. Ndipo iwo anali woti andilowetsemo ine monga choncho. Boma linali kundilowetsako ine.

Chotero, pamene iwo anatero, bi—bishopu, mmodzi wa mabishopu aakulu a mpingo wa Katolika, anapita kwa iye, kwa kazembe, ndipo anati, “Bwana, ine ndamva kuti inu mukumubweretsa amene si Mkatolika.”

Anati, “Inde. Pali vuto kutero?”

“Bwanji,” iye anati, “inu simungamubweretse munthu woteroyo kuno. Boma lino silinayambe ladziwapo kuchita chinthu ngati chimenecho.”

¹⁰⁹ “Koma,” anati, “ife tachita izo tsopano.” Iye anati, “Bwanji,” anati, “mwamunayo ndi mwamuna wolemekezeka. Ine ndamva kuti masauzande a anthu amabwera kuti adzamumvere iye. General Valderna, iyeyo ndi mzanga wa pamtima.” Iye anati...Ndipo anali ndi...Purezidenti nayenso ndi wa Chiprotostanti, inu mukudziwa, Methodist. Chotero iye anati—iye anati, “Mwamunayo ndi mwamuna wolemekezeka, mmene ine ndikudziwira.” Anati, “General Valderna kuno, iye anatembuzidwa ndi munthu ameneyo.” Anati, “Bwanji, iye ali, mmene ine ndikudziwira, ndi munthu wolemekezeka.” Anati, “Masauzande a anthu, iwo akuti, abwera adzamumvere iye.”

Ndipo bishopu uyu anati, “Ndi anthu a mtundu wanji amenewo, bwana? Osazindikira okhaokha. Iwo ndi amene amapita, kukamumvera munthu ngati ameneyo.”

¹¹⁰ Apurezidenti anati, “Bwana, inu mwakhala nawo iwo kwa zaka faivi handiredi, nchifukwa chiyani iwo ali osazindikira?” Zimenezo zinali zokwanira. Izo zinakhazikitsa izo. Oh, mai! Zimenezo zinawachotsa nyanga iwo. Inde, bwana. Eya.

¹¹¹ Kenako pamene mwana wamng’ono uja anawukitsidwa kwa akufa, ine ndinatimiza wothamanga kuti amutsatire munthuyo. Donayo anali kulankhula, mu Chispanish, “Mwanayu anafa, mmawa uno naini koloko.” Ndipo inali ikuvumba, mvula. Tikumakhala ndi wotembuzidwa kwa Khristu pafupifupi teni sauzande, usiku uliwonse.

Usiku wapambuyo wake, mwamuna wokalamba wakhungu anali atalandira kupenya kwake pa nsanja. Oh, usinkhu

wake kuchulukitsa katatu kapena kanayi kachisi uyu, ndipo pafupifupi kukwera mmwamba *chomwecho*, mashawelo akale ndi zipewa zitawunjikidwa. Ndipo ine basi . . .

¹¹² Iwo ananditsitsira ine pansi ndi zingwe, mu chozungulira, kuti akandilowetsemo ine. Ine ndinangoyenda kupita pamenepo ndi kuyamba kulalikirira, mwa chikhulupiriro.

Billy anabwera, anati, “Adadi, inu mukuyenera kuti muchite chinachake, mkazi uyo.” Anati, “Ine ndiri ndi othandizira firii handiredi ayima pamenepo. Iwo akulephera kumuimitsa mkazi wamng’onyo, akulemera mapaundi handiredi, pafupifupi.” Ndipo dona wokongola, wamng’ono wotalika pafupifupi *chonchi*, pafupifupi, oh, mwinawake mwana wake woyamba. Ine ndinganene kuti iye ndi wausinkhu wa twente firii kapena zaka twente faifi zakubadwa.

¹¹³ Ndipo iye anali ataima pamenepo, ndipo tsitsi lake likugwera pansi, ndipo atamuyangata mwana wamng’onyo. Ndipo iye amakankha mzerewo mwamphamvu. Azibambowo amakhoza kumukankhira iye mmbuyo. Iye amakhoza kukakwera pamwamba pa iwo, mwana ameneyo ali pa phewa pake, mulimonse, amadutsa pakati pa miyendo yawo, kapena chirichonse. Iwo amakhoza kumupititsa iye pamwamba apo, ndipo amachita kumuchotsa iye pa nsanjapo.

¹¹⁴ Ndipo iwo analibe khadi la pemphero kuti amupatse iye. Iye anati, “Ngati ine ndimulola iye kuti abwere kumeneko, Adadi, ali ndi mwana wakufa uyo, wopanda khadi la pemphero, ndi . . .” Anati, “Ena awo ataima pamenepo, akhala akuima apa masiku awiri kapena atatu, ali mu mvula imeneyo ndi dzuwa. Ndipo ndimulole iye awapitirire iwo,” anati, “izo ziyambitsa pho—phokoso kumeneko.”

¹¹⁵ Ine ndinati, “Izo ziri bwino.” M’bale Moore anali kumeneko, ndipo iye ndi wadazi ngati ine. Ndipo ine ndinati, “Iye sakudziwa kuti uyu ndi ndani, pachuluka anthu.” Ine ndinati, “Mtumizeni . . .” Ndipo—ndipo abale angapo, mmodzi wa abale ochokera kuno ku kachisi, amene anapita ku Ulemelero tsopano, ine ndikulephera kumuganzizira dzina lake basi pa nthawi ino, koma, iye anali kuima kumbuyo uko. Chotero ine ndinati, “M’bale Moore, pitani uko, mukamupempherere mwanayo. Iye sakadziwa kuti ndi ndani, kaya ndi ine kapena inu. Ingopitani kumusiko. Ndipo wosatha kuyankhula Chizungu.”

Ndipo chotero M’bale Moore anati, “Chabwino, M’bale Branham.”

¹¹⁶ Iye anayamba kuyenda chotsika. Ine ndinati, “Pamene ine ndimati, a- . . .” Ndipo ine ndinamuwona mwana wamng’onyo, mwana wamng’ono wa Chimexico atakhala patsogolo panga, akungosekerera. Ine ndinati, “Dikirani miniti.” Ndipo ine ndinati, “Muloleni dona wamng’onyo adutse.”

Billy anati, “Ine sindingachite zimenezo, Adadi. Iye . . .”

Ine ndinati, “Ine ndawona masomphenya, Billy.”

Anati, “Oh, izo nzosiyana.”

¹¹⁷ Chotero ife tinatsegula njira monga choncho ndipo anamudutsitsa iye. Apa iye anabwera, akugwa pa mawondo ake, ali ndi mikanda ya pemphero mdzanja lake. Ine ndinati, “Imilira.”

Chotero ine ndinati, “Atate Akumwamba, tsopano ine sindikudziwa chimene Inu muti muchite. Ine sindikudziwa ngati Inu mukungofuna kuti ine ndingomukhutitsa mkaziyu pomupempherera mwanayu, kapena chiyani. Koma,” ine ndinati, “Ine ndikuika manja anga pa mwana wamng’ono, mu Dzina la Ambuye Yesu.” Basi chinthu chomwecho mmene ine ndinachitira ndi M’bale Way, atagona apo pansi, atafa, tsiku lina. Ndipo bulangeti linasuntha, ndipo mwana wamng’ono uja anayamba kufuula. Ndipo iye anali atabwerera ku moyo wake. Pamene . . .

¹¹⁸ Ine ndinatumiza woti athamange, M’bale Espinosa, kuti apite naye kwa adokotala, ndipo akatenge umboni wolemba wochokera kwa adokotala, “Mwana ameneyo anafa.” Izo zinali pafupifupi teni koloko usiku umenewo. “Anafa mmawa umenewo naini koloko, mu ofesi yake, ndi chibayo.” Iye anatenga umboni wolembedwa wochokera kwa adokotala.

Amapepala sanathekungokhala chete, inu mukudziwa, chotero iwo anadzabwera. Iwo anadzandifunsa ine. Ndipo iwo anati kwa ine, iye anati, “Kodi inu mukuganiza kuti oyera athu akhoza kuchita zimenezo, nawonso?”

Ine ndinati, “Ngati iwo ali moyo.”

“Oh,” iye anati, “iwe sungakhale woyera mpaka iwe utafa.” Ndi zimenezotu. Mukuona? Ndipo anthuwo . . .

¹¹⁹ Inu mukuona, tsiku lina, kumene iwo anali ndi sisitere uyu amene iwo ankamuchita seweru, mu pepala? Chotero, woyera watsopano anafa, oh, zaka handiredi zapitazo, kapena chinachake chonga choncho, ndipo iwo anapanga a . . . anamuyeretsa iye tsopano, anampanga iye kukhala woyera. Ndipo iwo ananena kuti—kuti iye anadzuka kwa akufa ndipo anamupempherera munthu wina wodwala amene anali ndi khansa ya mmagazi. Si choncho izo? Izo zinali mu imodzi ya magazini. Tangoganizani mmene iwo amayesetsera kuzichita mwasewero izo, ndipo pamene pali mahandiredi ndi mahandiredi a zochitika ziri pansi pa mphuno kumene za anthu kuno. Chinthu chimenecho ndi chiyani? Kuti mpaka chinthucho chawapangitsa Achiprotestanti kulowa mu zimenezo, mwaona, kuchipangitsa icho kukhala chinachake.

Ndiyeno ntchito zenizeni za Ambuye, kumene zikuwonetseredwa mwangwiro, kutsimikiziridwa, iwo

sangayerekeze kuti izo zikhudze pepala. Ndi zimenezotu. Iwo anaitanidwa ndipo anakana. Inde, bwana.

¹²⁰ Iwo sangathe kumvetsa momwe Uthenga wophwekawo, anthu ophweka, kukana chinthu ngati chimenecho zingawapangitse iwo kupita mu chisokonezo.

¹²¹ Mkazi anati kwa ine, Grants Pass, Oregon, nthawi ina kale, mtsikana wa Chikatolika anabwera kuchokera kumeneko kuti adzadzudzule ndi kudzalemba. Iye anali mtolankhani wa nyuzipepala, ali ndi mpukutu wa ndudu mdzanja lake. Ndipo iye anati, “Ine ndikufuna ndiyankhule nanu.”

Ine ndinati, “Ndi chiyani chimene iwe ukufuna kuti unene?”

Iye anati, “Ine ndimafuna kuti ndikufunsemi inu mafunso ena okhudza chipembedzo chanu ichi.”

Ndipo ine ndinati, “Ndi chiyani chimene iwe ukufuna kundifunsa?”

Ndipo iye anati, “Inu mumachita izi ndi ulamuliro wanji?”

¹²² Ine ndinati, “Mu Dzina la Yesu Khristu, mwa kuitana kwa Umulungu.” Ndipo iye anapitirira, kumazinyozetsa. Ine ndinati, “Miniti chabe.”

Iye anati, “Ngati ine ndikanati ndiziyanjana ndi gulu la mbuli limenero uko,” iye anati, “ine sindikadafuna nkomwe kuti ndikhale Mkristu.” Iye anati, “Ndipo ngati iwo . . . Iwo amanena kuti anthu amenewo adzalamulira dziko lapansi tsiku lina.” Iye anati, “Ine ndikudalira kuti sindidzakhala ndiri kuno.”

Ine ndinati, “Musadandaule. Inu simudzakhalako.” Ine ndinati, “Inu . . . muyenera kudandaula za zimenezo.”

“Bwanji,” iye anati, “zotengeka zonse izo ndi kufuula!”

Ine ndinati, “Ndipo ukuti ndiwe wa Katolika?”

Iye anati, “Ine ndiri.”

¹²³ Ine ndinati, “Kodi iwe ukudziwa kuti namwali wodala Maria anachita kulandira Mzimu Woyera ndi kuyankhula mmalirime, ndi kuvina mu Mzimu, chimodzimidzi ndi mmene iwo anachitira, Mulungu asanamulandire iye? Inu mumamutcha iye amake a Mulungu.”

Iye anati, “Izo ndi zamkutu.”

Ine ndinati, “Miniti chabe. Ine . . .”

“Ine sindikuyenera kuti ndiziyang’ana pa Baibulo.”

¹²⁴ Ine ndinati, “Ndiye iwe ungaswiwe bwanji chimene chiri Choonadi kapena ayi?”

Iye anati, “Ine ndimatenga zonena za mpingo wanga.”

¹²⁵ Ine ndinati, “Awa ndi Mawu a Mulungu. Ndi Awa pomwe apa. Ine ndikukubetchera iwe kuti uyang’ane pa Iwo. Ndipo Mariya anali ndi iwo kumeneko mchipinda chapamwamba,

ndipo analandira ubatizo wa Mzimu Woyera monga ena onse a iwo anachitira. Ndipo inu mumamutcha iye amake a Mulungu.” Ine ndinati, “Ndiye nkumawatcha awo, ‘Mulu wa zinyalala, obwerera mmbuyo?’” Ine ndinati, “Usadandaule. Iwe sudzakakhalako Kumeneko. Iwe ulibe zochuluka zoti uzizidandaula, ngati izo ziri zonse zimene ukuzidandaula. Iwe kuli bwino uzidandaula za moyo wako wochimwa, mtsikana.” Ndipo ine ndinamusiya iye azipita.

¹²⁶ Tsopano taganizani za zonse izi, zophweka. Mulungu amazipanga izo kukhala zophweka kwambiri.

Zinatheka bwanji Ahabu, zinatheka bwanji Yezebeli, zinatheka bwanji anthu aja amene ankaganiza kuti Eliya anali mfiti, ankaganiza kuti iye anali wazamizimu? Ngakhale Ahabu anati, “Apa pali amene wayambitsa mavuto onsewa kwa Israeli.”

Iye anati, “Iwe ndi amene ukuvutitsa Israeli.”

¹²⁷ Fuko limenero likanakwanitsa bwanji kuganiza, kuti, kuwukana uthenga wa munthu wa nkhope yamanyenje woteroyo, wosavala zovala zaunsembe, ndi zina zotero, chikadakhala chiweruzo cha izo?

Zinatheka bwanji Igupto, wolamulira dziko lapansi, afarao, ndi gulu lawo ndi aulemu...? Dziko silinayambe lafikapo pa malo amenewo kenanso, mu sayansi ndi zina zotero. Iwo akanakwanitsa bwanji kuganiza, kuti kumukana mneneri wokalamba wa zaka eyite, wa manyenje akulendewela pansi, wa tsitsi la imvi, akutulukira pamenepo, wothawathawa? Ndipo nkubwera kumeneko ndi uthenga, “Inu muwalole iwo azipita, kapena Mulungu awononga fukoli.” Farao akanatha bwanji? “Iwe undimvere ine, Farao.”

¹²⁸ Farao anati, “Kukumvera?” Oh, iye, Farao! “Ndipo bambo wokalamba, chidempete china chokalamba,” iwo anaganiza, “kumukana munthu ngati ameneyo, zingawononge fuko?” Koma izo zinachita zimenezo. Oh, mai!

Tiyeni tiimikire, tiime maminiti pang’ono ndipo tikhale ndi pemphero, ndipo tiganizire. Kodi ndi tsiku lanji limene ife tikukhalamo? Kodi ife tiri pati? M’badwo wina wamakono, wasayansi. Ife tikuyenera kuganizira. Mwinamwake, inu muimikire, anthunu imani ndipo tipemphere kanthawi pang’ono, ndipo tiganizire pang’ono pokha, inu mungamverere bwino mutatha kutsiriza kuchita zimenezo. Uko nkulondola.

¹²⁹ Mkhristu si chida, kapena mtundu wina wa sipanala ya amakaniko kwa ulamuliro wawukulu wa chipembedzo. Uko nkulondola. Mkhristu si mtundu wina wa chida chinachake chimene chimapangitsa bungwe lachipembedzo kuti liziyenda. Mkhristu, ameneyo si Mkhristu. Mkhristu akuyenera kukhala wofanana ndi Khristu. Ndipo Mkhristu sangakhale Mkhristu kufikira Khristu atabwera mwa munthuyo, Moyu wa Khristu

mwa iye. Zikatero izo zimabala Moyo umene Khristu anakhala, ndipo iwe umachita zinthu zimene Khristu ankachita.

¹³⁰ Kodi ine ndikuyankhula za chiyani? Ubwenzi wawekha ndi Khristu. Kodi icho ndi chiyani? Kodi moyo wanu ndi woyenera Uthenga?

Tspano ine ndikuyesetsa kuika maziko amenewo apo, kuti ndikuwonetseni inu kuti, amuna ndi akazi amene anali akazi odziwika, amuna.

¹³¹ Baibulo linati. Kodi inu munazindikira? Lamlungu lapitali usiku, chinachake chimene ine ndinaiwala kuikamo, Genesis mutu wa 6 ndipo ndime ya 4. “Amuna awo amene anadzitengera kwa iwo akazi, kuti akhale akazi awo, anali amuna akale, odziwika.” Amuna odziwika, ananenera kuti adzabweranso. “Monga izo zinali mmasiku a Nowa, chomwechonso izo zidzakhala mu Kubwera kwa Mwana wa munthu.” “Amuna odziwika kumatenga akazi,” osati akazi awo, “akazi; kumayenda ndi matupi achirendo.”

¹³² Tayang’anani mu England, masabata angapo apitawo. Tayang’anani mu United States. Tayang’anani konsekonse, kwangodzaza ziwerewere. Amuna aakulu, otchuka, maudindo apamwamba, kubweretsa manyazi pa fuko, kutsatira akazi. Mwamuna wamkulu uja uko mu England, wokhala ngati wamkulu wa gulu lazigawenga, monga, bwanji, kodi inu munazindikira, iye anali ndi mkazi wokongola. Chithunzi chake chinali pamenepo, pamodzi. Tayang’anani pa wachiwerewere wa Chirussia uja, koma iye anali yense atavala za kugonana, ndipo anakaziponyera yekha kunja uko, kuti akawonetse thupi lake lachikazi. Ndipo mwamunayo anakopeka ndi zimenezo.

¹³³ Chimene ife tikusowa lero ndi ana aamuna a Mulungu. Ife tikusowa amuna mu boma, amene ali ana aamuna a Mulungu. Uko nkulondola. Chotero, mfumu yabwino, yaumulungu ikanaletsa zamkutu zonsezi. Sipakanakhala zolekerera. Monga anachitira Davide, iye anaimitsa izo. Ndithudi anatero, chifukwa iye anali mfumu. Ndipo uko kunali basi . . .

¹³⁴ Njira yeniyeni, ndiyo, Mulungu akhale Mfumu, ndipo Mulungu atumize mneneri. Kodi Samuele sanawauze iwo asanapeze kumse mfumu? Iye anati, “Mulungu ndi Mfumu yanu. Kodi ine ndinayamba ndakuuzanipo inu chirichonse mu Dzina la Ambuye koma chimene chinadzachitika?”

Iwo anati, “Ayi. Uko nkulondola.”

“Kodi ine ndinayamba ndakupemphanipo inu zakudya zanu?”

“Ayi. Inu simunatipemphepo ife zoti mukadye.”

“Ine sindinakuuzenipo inu chirichonse koma chimene chinali cholondola, pamaso pa Ambuye.” Anati, “Mulungu ndi Mfumu yanu.”

135 “Oh, ife tikuzindikira zimenezo. Ndipo ife tikudziwa kuti ndinu munthu wabwino, Samuele. Ife tikukhulupirira Mawu a Ambuye amabwera kwa inu, koma ife tikufuna mfumu, mulimonse.” Mukuona? Izo ndi zimene iwo amapeza.

136 Achipentekoste ankafuna bungwe, mulimonse. Iwo anapeza izo. Uko nkulondola. Ankafuna kuti akhale monga mipingo ina yonseyo. Inu muli. Pitirirani, izo, izo basi ndi zimene zimatengera. Koma Mulungu ndi Mfumu yathu. Mulungu ndi Mfumu yathu. Inde, bwana.

137 Ndi chiyani chimenecho? Ndi chifukwa chakuti anthu, monga iwo ankachitira mmasiku a Khristu, monga iwo akhalira nazo mu m’badwo uliwonse, iwo amapeza chowiringula. Iwo ali ndi tizikhulupiro tawo tawo. Inu mukhoza kusafuna kuti munene, “Ine—ine ndagula ng’ombe, ndipo ine ndikuyenera kupita kuti ndikawone ngati iyo—iyo izigwira ntchito kapena ayi, kapena izipereka mkaka, kapena—kapena ndi mtundu wanji umene iyo ili.” Inu mukhoza kusakhala ndi chowiringula chimenecho.

Koma nachi chowiringula chimene anthu akhoza kumanena, “Ndine wa Presbateria. Ife sitikhulupirira mu Zimenezo. Ndine wa Baptisti. Ife sitikhulupirira mu zinthu ngati Zimenezo. Chabwino, ndine wa Lutera.” Chabwino, izo ziribe kalikonse kochita ndi Izo. Izo sizikutanthauza kuti ndiwe Mkhristu. Izo zimatanthauza kuti iwe ndi wa gulu la anthu amene apanga bungwe. Ndipo iwe ndi wa loji ya Lutera, loji ya Baptisti, loji ya Pentekoste. Palibepo chinthu chokhala ngati Mpingo wa Pentekoste. Palibepo chinthu chonga Mpingo wa Baptisti. Iyo ndi loji ya Baptisti, loji ya Pentekoste, loji ya Presbateria.

Koma ulipo Mpingo umodzi wokha. Ndipo pali njira imodzi yokha imene iwe ungalowere mwa Iwo, ndipo ndiyo mwa Kubadwa. Iwe umabadwira mu Mpingo wa Yesu Khristu, nkukhala membala wa Thupi Lake, la nthumwi yauzimu ya Kumwamba. Kenako zizindikiro, zakuti Khristu ali ndi iwe, zimakhala moyo mwa iwe.

138 Akhristu, oh, inu muyenera kukhala ndi ubale wapanokha ndi Mulungu. Kuti mukakhale mwana wa Mulungu, inu mukuyenera mukhale pachibale ndi Mulungu. Iye ayenera kukhala Atate wanu, ndi cholinga chakuti inu mukhale mwana Wake. Ndipo ana aamuna Ake okha ndi ana aakazi amapulumsidwa, osati mamembala a mpingo, koma ana aamuna ndi aakazi. Pali chinthu chimodzi chokha chimene chingabale zimenezo, ndicho Kubadwa kwatsopano. Kubadwa kwatsopano ndi chinthu chokhacho chimene chingabale ubale kwa Mulungu. Nkulondola uko? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.] Ana aamuna ndi aakazi. Ndiye pamene izi zichitika, ndiye amuna . . .

¹³⁹ Funso lake ndi ili limene ine ndikufuna kuti ndikufunseni inu. Munthu amati, “Ife tichite chiyani ndiye titatha kubadwanso mwatsopano?” Ambiri amandifunsa ine funso limenelo. “Ndichite chiyani ndiye, M’bale Branham?” Ngati iwe wabadwa mwatsopano, chikhalidwe chako chonse chimasintha. Iwe umafa ku zinthu zimene iwe unayamba waziganizirapo.

¹⁴⁰ “Chabwino,” inu mukuti, “M’bale Branham, pamene ine ndinajowina tchalitchi, ine ndinapeza zimenezo.”

Chabwino, ndiye, pamene, Mulungu anati, “Yesu Khristu ndi yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Iye akuchiritsabe odwala. Iye akuwonetsabe masomphenya.”

“Koma, M’bale Branham, mpingo wanga!” Tsopano, iwe sunabadwe mwatsopano. Mukuona? Iwe sizingatheke kuti utero; pakuti, ngati Mulungu mwiniwakeyo, ngati Moyo Wake ukhala mwa iwe, monga ngati...inu muli mu...moyo wa abambo anu, ndipo, ngati Moyo wa Mulungu mwiniwakeyo ukhala mwa iwe, Mzimu kumene umene unali mwa Khristu, ukakhala mwa iwe, zingatheke bwanji Mzimuwo kukhala mwa Yesu Khristu ndi kulemba *Awa*, ndipo kenako nkudzatsikira mwa iwe ndipo nkuwakana Iwo? Mukuona? Sizingatheke zimenezo. Iwo udzavomereza Mawu aliwonse kuti ali chomwecho.

¹⁴¹ Ndiye, ngati inu mukuti, “Chabwino, ndine membala wabwino wa mpingo,” zimenezo ziribe chinthu chimodzi chochita ndi Iwo.

Ine ndikuwadziwa achikunja. Uko mu Afrika, pakati pa abale anga achikuda kumusi uko, ine ndinakapeza makhalidwe a anthu amenewo apamwamba kuposa—kuposa nainte peresenti ya anthu Achimerika. Bwanji, mmafuko ena kumeneko, ngati mtsikana wamng’ono sakukwatiwa mpaka kufika usinkhu winawake, kapena pamene iye wafika usinkhu winawake ndipo palibe wamutenga iye, iwo amadziwa kuti pali chinachake cholakwika. Iwo amamuchotsa iye. Iye amamuchotsa utoto wa fuko, ndipo iye amapita ku mzinda, kenako iye amangokhala chigawenga. Ndipo iye akakwatiwa, iye amakayesedwa unamwali wake. Ngati chophimba chaching’ono cha unamwalicho chinawekapo, ndiye iye amayenera kunena amene anachita zimenezo. Ndipo iwo amakawapha awiri onsewo, pamodzi. Kodi simungakhale kuphedwa kochuluka mu Amerika ngati zimenezo zitamachitika? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Mukuona? Ndiye inu mumawatcha iwo achikunja? Oh, mai! Iwo akhoza kubwera kudzawaphunzitsa anthu, amene amadzitcha okha mamembala a mpingo, momwe angakhalire oyera. Zoona zimenezo.

¹⁴² Sindinapezeko vuto limodzi lamatenda opatsirana pogonana mu ulendo wonsewo ku South Africa. Iwo alibe chinthu choterocho. Ndi zimenezotu. Mukuona? Zangokhala njira zathu zovunda, ngati azungu. Zoona zimenezo. Achoka kwa Mulungu.

¹⁴³ Pamene izi zidzachitika, chinthu chimene inu muti mudzachite nthawi imeneyo, inu mudzapeza kuti Mzimu umene udzabwere mwa inu, kuchokera ku Kubadwa kwatsopano, inu mudzakhulupirira ndipo mudzachita chirichonse chimene Mulungu ati azidzanena mu Mawu Ake kuti inu muchite. Ndipo chirichonse chimene Baibulo lizidzabwereza kuti inu muchite, inu mudzavomereza izo ndi “ameni.” Ndipo inu simudzasiya, usana ndi usiku, mpaka inu mutalandira izo. Zoon zimenezo. Zoon zimenezo. Ndipo mu nthawi yonse, inu ndithudi, pamwamba pa chirichonse, muzidzabala chipatso cha Mzimu.

¹⁴⁴ Inu mukuti, “Kodi ine ndizidzayankhula ndi malirime?” Inu mukhoza kudzachita zimenezo, ndipo inu mukhoza osamadzachita. “Kodi ine ndizidzafuula?” Inu mukhoza kumadzachita zimenezo. Inu mukhoza osadzamachita.

Koma pali chinthu chimodzi chotsimikizika chimene inu muti muzidzachita. Inu muzidzabala chipatso cha Mzimu. Ndipo chipatso cha Mzimu ndi chikondi, chimwemwe, mtendere, chikhulupiriro, kuleza mtima, chifatso, chifundo, chipiriro. Kupsyamtima kwanu sikudzakhalapo, “Oooh!” Muzingokumbukira, pamene inu mukhala ndi zimenezo, zimenezo zimawupatsa chiphe Mzimu Woyera kuti uchoke mwa inu. Mukuona? Pamene inu mufika pamalo amene inu mukufuna kukangana ndi aliyense amene inu mungakumane naye, pali chinachake cholakwika. Pamene inu mufika pamalo amene chi . . . mtumiki akawerenga kuchokera mu Baibulo, kuti ndi zolakwika kuchita chinthu chinachake, ndipo, inu nkuti . . . Ingokumbukirani, palibepo Chikhristu pamenepo nkomwe. Ndizo tsopano, kuti, “Ndi zipatso zawo inu mudzawadziwa iwo.” Ndizo zimene Yesu ananena. Mukuona?

¹⁴⁵ Ngati iwo ali Mawu, ndipo Mulungu ananena chomwecho, Mzimu umenewo mwa inu udzalumikizana ndi Mawu amenewo, nthawi iliyonse. Chifukwa, Mzimu Woyera weniweni udzalumikizana ndi Mawu, chifukwa Mawu ndi Moyo ndi Mzimu. Yesu anati, “Mawu anga ndi Moyo.” Ndipo ngati inu muli ndi Moyo Wamuyaya, ndipo Iye ndi Mawu, Mawu angathe bwanji kukana Mawu? Mukuona? Ndi munthu wa mtundu wanji ameneyo kuti angapangidwe kukhala Mulungu? Ndicho chinthu chimodzi choyenera kuchidziwa, kuti ndinu Mkhristu, pamene inu mungavomereze kwathunthu pa Mawu aliwonse a Mulungu.

¹⁴⁶ Ndipo inu mudzazipeza nokha mukuwakonda adani anu. Winawake akati, “Chabwino, iye sikanthu koma woyera wodzigudubuza.” Ndipo inu nkuyamba ku . . . Ah! Undisamale. Um-hum. Undisamale. Koma pamene inu mudzipezadi, nokha, kuti inu mukumukonda iye! Osalabadiira za zimene iwo akuchita, inu nkumawakondabe iwo. Mukuona?

¹⁴⁷ Zikatero inu mwayamba kupeza, ndipo chipiriro chanu chimachoka pa utali *wotere*, mpaka icho chimangokhala

chopanda malire. Aliyense akakhala kuti akunena zinthu zokhudza inu, “Chabwino, ine sindikusamala zimene inu mukunena!” Simumakondowezeke nazo. Ngati inu mukondowezeke nazo, inu bola mupite mukapemphere poyamba, inu musanayankhulenso ndi iwo kenanso. Eya. Eya.

Musamakhale mmakangano. Musamakonde kukhala mmakangano; ngati inu mumakonda kumuwona winawake akudzuka mu tchalitchi, ndikuti, “Inu mukudziwa chiyani? Ine ndikuuzani inu, *Wakuti-ndi-wakuti* anachita *chakuti-ndi-chakuti*.”

Inu muziti, “Tsopano, m’bale, manyazi pa inu.”

¹⁴⁸ Ngati inu munena kuti, “Oh, kodi ziri chomwecho?” Nkumamvetsera zoyaluka zimenezo? Musamale.

Mzimu Woyera si chithamphwi. Mukuona? Ayi, ayi. Ayi, ayi. Mtima umene wadzazidwa ndi Mzimu Woyera, umakhala wodzaza ndi chiyero, ungwiro. “Sumaganiza choipa chirichonse, sumachita choipa; umakhulupirira zinthu zonse; umapirira, kuleza mtima.” Mukuona?

¹⁴⁹ Musamakangane. Pamene banja liyamba kukangana, musamakangane nawo. Amayi anu akati, “Ine sindikulola iwe kuti uzipita uko, ku tchalitchi chakale icho, panonso. Chabwino, iwe, zonse zimene iwe ukuziganizira tsopano, iwe ukufuna tsitsi lako lizikula. Iwe ukuwoneka ngati agogo ena okalamba.” Iwe usakangane nawo iwo.

Ungoti, “Chabwino, amayi. Izo ziri bwino. Ine ndimakukondani inu, chimodzimidzi basi. Ndipo ine ndizikupempherani inu bola ndiri moyo.” Mukuona?

¹⁵⁰ Tsopano, osamakangana. Mukuona? Mkwiyu umabala mkwiyo. Chinthu choyamba inu mukudziwa, inu muwukwiyitsa Mzimu Woyera mpaka uchoka mwa inu, inu mudzakhala mukubweza kukanganako. Kenako Mzimu Woyera Iwo udzathawapo. Mkwiyu umabala mkwiyo.

Ndipo chikondi chimabala chikondi. Mudzikhala odzaza chikondi. Yesu anati, “Mukatero anthu onse adzadzziwa kuti ndinu ophunzira Anga, pamene inu muli ndi chikondi, kwa wina ndi mzake.” Ndicho chipatso cha Mzimu Woyera, chikondi.

¹⁵¹ Ndipo kodi inu mumadziwa, inu ndi mlengi wamw’ono, inueni? Inu mukudziwa zimenezo? Ndithudi. Inu mwawawonapo anthu amene inu mumangokonda kukhala nawo pafupi. Inu osadziwa chifukwa chake. Basi mtundu umenewo wa munthu wokonda. Kodi inu munayamba mwaziwonapo zimenezo? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Wachifundo basi, pamene, inu mumangokonda kukhala pafupi ndi iwo. Ndizo... Iwo amalenga chikhalidwe chimenecho, ndi moyo umene iwo amakhala, mmene iwo amayankhulira, machezedwe awo.

Ndiye, inu mwawawonapo iwo amene, nthawi zonse, inu— inu mumawathawa iwo. Nthawi zonse, iwo amafuna kuyankhula chinachake choipa, ndi kumamunena winawake. Kumati, “Oh, mai! Ndi awo akubwera apowo. Iwo amunyoza winawake pamenepo. Iye ali muno tsopano, iye ayankhula za munthu *uyu*. Zonse zimene iwo ati achite ndi kunena nthabwala zauve, kapena chinachake chokhudza akazi, kapena chinachake chonga zimenezo.” Inu basi mumangodana nazo kukhala pakati pawo. Mukuona? Iwo amalenga. Ukamawawona, ngati anthu abwino kwambiri, koma iwo amalenga chikhalidwe chimenecho.

Ndipo zinthu zimene iwe umaziganizira, zinthu zimene iwe umachita, zochita zake, zinthu zimene iwe umaziyankhula, zimalenga chikhalidwe.

¹⁵² Ine ndinapita mu ofesi ya mzibambo, kuno mu mzinda uno. Ndipo bambuyo ndi trastii, kapena dikoni, ndi choncho, mu tchalitchi chabwino. Ine ndinapita kumeneko kuti ndikamuwone bambo ameneyo pa zochitika zina. Ndipo ali ndi wailesi mmenemo, imaimba gwedemula ameneyo kapena kanindo, chirichonse chimene izo zinali, molimba basi mmene izo zimachitira. Ndipo ine ndikuganiza munali zithunzi zopachikidwa forte mu ofesi yake, za akazi amaliseche. Tsopano, inu simungandiuze ine momwe muliri dikoni, kapena mochuluka bwanji. Inu mundilole ine ndiwone zimene inu mumaziyang’ana, ndi zimene inu mumawerenga, ndi mtundu wa nyimbo zimene inu mumamvetsera, gulu limene inu mumayanjana nalo, ndipo ine ndidzakuuzani inu mtundu wa mzimu umene uli mwa inu. Mukuona? Eya.

¹⁵³ Inu mukamumva munthu akuti, “Ine ndimachita *zakuti-ndi-zakuti*? Gulu limenelo. . .” Ingokumbukirani, ine sindisamala zimene iye amanena. Zoyankhula zake zimayankhula mokweza. Zochita zake zimayankhula mokweza kuposa chimene chirichonse chinganene. Iye akhoza kuchitira umboni, kunena kuti iye ndi Mkristu, ndithudi, ndipo mwinamwake kuchita chirichonse. Koma inu muzingoyang’ana mtundu wa moyo umene iye akukhala. Zimenezo zimanena chimene iye ali.

¹⁵⁴ Tsopano, kodi inu mungaganizire kuti, munthu amene moyo wake ungamanene kuti, “Kukhulupirira machiritso Auzimu, ndi chinachake cha mbalame. Izo zinali zambuyo zaka zapitazo. Kulibeko chinthu choterocho lero”? Kodi umenewo ndi moyo woyenera Uthenga, umenewo, “Khristu anavulazidwa chifukwa cha zolakwa zathu, ndipo ndi mikwingwirima Yake ife tinachiritsidwa”? Inu nkuti, “Koma ndine dikoni.” Ine sindikusamala. Inu mukhoza kukhala bishopu.

¹⁵⁵ Pamene ine ndinamumva Bishopu Sheen akuyankhula, pafupifupi zaka ziwiri zapitazo, ndikubwera chotsika; sindidzatsegulanso kuti ndimumvere iye nkomwe. Pamene iye anati, “Munthu amene angakhulupirire ndi kumayesetsa

kuti azikhala moyo mwa Baibulo limenero, anali ngati winawake amene akuyesetsa kuti ayende mmadzi amatope.” Bishopu Sheen, kenako anadzapotoloka, anati, “Ine ndikadzafika Kumwamba, inu mukudziwa chiyani? Pamene ine ndidzakumana ndi Yesu, ine ndidzamuza Iye, ‘Ndine Bishopu Sheen,’ ndipo Iye adzati, ‘Oh, inde, Ine ndinamva amayi Anga akuyankhula za inu.’” Chikunja, amuna amene anganyoze Mawu amenewo. Mulungu awachitire chifundo. Ine sindine woweruza. Mukuona?

Mawu amenewo ndi Choonadi. Kulondola. Ndipo Mzimu wa Mulungu umazindikira Zolembe Zake Zomwe. Iye amazindikiritsidwa ndi Zolembe Zake. Izo—Izo—Izo zimayankhula za Iye. Ndipo inu mumazindikiritsidwa pokhulupirira Izo, ndipo Izo zimakupatsani inu zikalata zanu za kuzindikiritsidwa.

¹⁵⁶ Musamakangane ndi azimzanu. Ndipo musati—ndipo musamakhale ndi makangano apabanja awa, monga ine ndimanenera. Chikondi chimabala chikondi. Ndipo mkwiyo umabala mkwiyo.

¹⁵⁷ Tsopano, tsopano tiyeni tiwone. Tamuyang’anani Yesu, kwa miniti chabe. Iye anali chitsanzo chanu. Ine ndikudalira kuti inu simukutopa kwambiri. Onani. Tiyeni tiyang’ane pa Yesu, miniti yokha. Iye anali chitsanzo chathu. Iye ananena chomwecho. “Pakuti ine ndakupatsani inu chitsanzo, kuti inu muziwachitira ena monga Ine ndachitira kwa inu.”

¹⁵⁸ Tsopano penyani. Pamene Iye anabwera mdziko, pamene kunali zochuluka, kusakhulupirira kochuluka mdziko nthawi imeneyo kuposa mmene izo zinayamba zakhahirapo, izo sizinamubweze Iye nkomwe. Iye anapitirirabe kumalalikira chimodzimodzi basi, ndi kumachiritsa chimodzimodzi basi. Sizinamusokoneze Iye. Kunali otsutsa kumeneko. Munthuyo anatsutsidwa kuyambira nthawi imene Iye anali Khanda mpaka pamene Iye ankafa pa mtanda. Kodi izo zinamumitsa Iye? Ayi, bwana. Cholinga Chake chinali chiyani? “Nthawizonse kuchita zimene Atate analemba. Nthawizonse kuchita zimene zimamukondweretsa Iye.”

¹⁵⁹ Tamuyang’anani Yesu. Mukukamba za kuti ife tizidzichepetsa tokha? Pamene Mulungu Mwiniwake anadzakhala Khanda, mmalo mobwera mu ka—kabedi kakang’ono penapake mu nyumba yabwino, anakabadwira kunja uko pa mulu wa manyowa mu khola, pakati pa ana a ng’ombe ofuula. Iwo anamukulunga Iye mu nsalu za pa khosi, zinali zitachoka pakhosi la joko la ng’ombe. Wosaukitsitsa wa wosaukitsitsa, ndipo, komabe, Mlengi wa miyamba ndi dziko lapansi.

¹⁶⁰ Usiku wina wozizira, wamvula, iwo anati, “Mphunzitsi, ife tipita kunyumba ndi Inu.”

¹⁶¹ Iye anati, “Nkhandwe ziri ndi mphanga, ndipo mbalame ziri ndi zisa, koma Ine ndiribe ngakhale malo oti ndingagonetsepo mutu Wanga.”

Mulungu, Yehova, anadzichepetsa Yekha ndipo anadzakhala Munthu; anaimiriridwa mu thupi lochimwa, kuti adzakuwomboleni inu ndi ine. Ife ndi ndani ndiye? Iye anali chitsanzo chathu. Ine Ndine ndani? Sikanthu.

¹⁶² Ine ndimamuuza winawake, madzulo ano, mu msonkhano waung’ono. Ine ndinati, “Mwana wamwamuna aliyense amene wabadwa mwa Mulungu amayenera kuti ayese-dwe, poyamba, akwapulidwe.” Ine ndikukumbukira pamene ine ndinali nazo zanga, kapena ora langa lopambana. Pamene a—pamene munthu abadwa mwatsopano, pamakhala kamalo kakang’ono, ngati usinkhu wa chikhadabo chake, kamene Mulungu amakaika mwa iye, zochitika, ndipo iko kamagwera mu mtima mwake ndipo pamenepo kamazikika. Kenako Satana amadzamupanga iye atsimikizire zimenezo. Ndipo ngati kameneko mulibemo mmenemo, iwe wapita.

¹⁶³ Ine ndikukumbukira uko mu chipatala, ine ndinali pafupifupi usinkhu wa zaka twente-thuu zakubadwa, twente-firii, mwinamwake, motero, ndinali mnyamata. Ndipo bambo anga, akufera mmikono mwanga, ndipo ine ndikuyankhula ndi Mulungu ngati mchiritsi. Ndipo abambo anga omwe ali mu vuto la mtima, atagonetsa mutu wawo mu nkono mwanga, ndipo ine ndi kuwapempherera iwo; ndipo ine ndinawawona iwo akutembenuza maso amenewo ndi kumandiyang’ana ine, ndipo anagwa, kupita kukakumana ndi Mulungu. Ine ndinawatenga iwo ndipo ndinakawaika iwo pambali pa mchimwene wanga, ndipo maluwa anali atsopanobe pa manda ake, ndipo ine ndikulalikira Mulungu amene amachiritsa odwala. Ndikugwira ntchito ku Public Service Company, ndikulandira masenti twente pa ora, ndipo mkazi wanga akugwira ntchito uko ku fakitare ya zovala; kuti azitithandizira ife kupeza chakudya cha mnyamata wathu wamng’ono wa miyezi eyitini, Billy Paul, ndi mwana wa miyezi eyiti amene iye anali akumuyangata.

Ine ndamuwona Mlongo Wilson amagwedeza mutu wake. Iye akukumbukira zimenezo; Roy Slaughter ndi ena anthawiyakale.

¹⁶⁴ Kodi ine ndinachita chiyani? Ndimayenda mmisewu, ndiri ndi sangweji mdzanja langa, ndimatsika pa pholo, ndi kumachitira umboni kwa aliyense amene angadutse, za chikondi cha Yesu Khristu. Kupita ku galaja yawo ndi kukawafunsa iwo ngati ine ndingagwiritse ntchito iyo, kuti ndiyankhule ndi amakaniko. Kupita kumeneko, ndikukati, “Azibambo, kodi inu munayamba mwapululumutsidwapo? Ine ndinapeza chinachake mu mtima mwanga.” Ndimapita ku sitolo usiku. Ndimabwera kunyumba thuu kapena firii koloko mmawa, ndikuchokera

koyendera odwala usiku onse. Sindikanatha . . . Ndimangokhala pansa, kusintha ndi kuvala zovala zanga zogwirira ntchito. Ndi kukakhala pa mpando apo ndi kupumulira mpaka mmawa, nkudzukapo ndi kumapita. Ndipo nditawonda kwambiri, chifukwa chosala kudya ndi kupemphera, mpaka ndimachita kupemphera kaye kuti ndivale zitsulo, pokwera pa pholo. Kumalalikira, ndi kumalalikira kuti Mulungu ndi wamkulu, Mulungu ndi wa chifundo, Mulungu ndi chikondi, kwa anthu.

Ndipo, apa, abambo anga akufera mmikono mwanga. Ndipo azichimwene anga anafa, anaphedwa ine nditaima paguwa kumusi kuno pa tchalitchi chaching'ono ichi, cha Chipentekoste cha anthu achikuda, ndikulalikira. Anabwera kudzandiuza ine, "Mchimwene wako waphedwa mu msewu waukulu. Galimoto yamugunda iye ndipo yamupha iye." Magazi a mchimwene wake yemwe akudontha pa malaya ake, pamene iye anakamunyamula iye pa msewu waukulu. Ine nditangomuika iye, abambo anga anamwalira. Kenako, kunadzagona mkazi wanga kunjira uko.

¹⁶⁵ Ndipo ine ndinapita, ndinadzabwera kuno ku kachisi uyu. Kuchokera apa, pamene pali nsanja iyi, ndinadzawauza anthu, miyezi sikisi izo zisanachitike, "Kudzabwera kusefukira kwa madzi. Ndipo ine ndinamuwona Mngelo atatenga ndodo, ndipo akuyeza, 'Mapazi twente- thuu mu mtunda mwa Spring Street.'"

Sandy Davis ndi iwo atakhala apa, anaseka, anati, "Izo zinali pafupifupi mainchesi eyiti kapena teni okha mu 1884, mnyamata. Ndi chiyani chikuyankhula ndi iwe?"

¹⁶⁶ Ine ndinati, "Izo zidzachitika. Chifukwa, ine ndinawona chimodzi cha zizimbwizimbwi izo, ndipo Iwo anandiuza ine chomwecho. Ndipo izo zidzakhala pamenepo." Ndipo pali cholozera pa Spring Street, lero, pa mapazi twente-thuu a madzi. Ine ndinati, "Ine ndinakwera pamwamba pa kachisi uyu mu bwato." Ndipo ine ndinatero.

¹⁶⁷ Panthawi imeneyo, mkazi wanga anadwala. Ine ndinamupempherera iye. Ndipo ine ndinabwera ku kachisi, anthu anali kumudikirira iye. Ine ndinati, "Iye akufa."

"Oh, iye ndi mkazi wako yekha, zimenezo."

¹⁶⁸ Ine ndinati, "Iye akufa."

Ine ndinapita kumeneko ndipo ndinapakemphera ndi kupemphera ndi kupemphera. Ndipo ine ndinali nditakweza manja anga. Iye anadzagwira dzanja langa. Iye anati, "Billy, ine ndidzakumana nawe iwe mmawa, nditaima Pamenepo." Anati, "Ukawatenge ana onse ndipo ukakumane nane pa Chipata."

¹⁶⁹ Ine ndinati, "Udzangoyamba kufuula, 'Bill.' Ine ndidzakhala ndiri Kumeneko." Mukuona? Ndipo iye anafa. Ine ndinakamugoneka iye uko mosungira mitembo.

Ndinapita kunyumba, kuti ndikagone. Ndipo pamene ine ndinatero . . . Billy Paul wamng'ono ankakhala ndi Akazi a Broy

ndi iwo, atadwala kwambiri. Adokotala akuyembekezera kuti iye amwalira nthawi iliyonse. Ine ndikumupempherera Billy. Ndipo apa panabwera M'bale Frank ndipo anadzandipeza ine. Anati, "Mwana wako akufa, mtsikana wamng'ono."

¹⁷⁰ Ine ndinatuluka kumapita ku chipatala. Dokotala Adair sanandilole ine kuti ndilowe, anati, "Iye ali ndi meningitis. Iwe uitengera iyo kwa Billy Paul." Anamuuzana namwino kuti andipatse ine zinthu zinazake zofiira kuti ndimwe, zokhala ngati zochotsa ululu, za chinachake zoti zinditontholetse ine. Ndipo ine ndinadikirira kuti iwo achoke mchipindamo, ndinaziponyera izo kunja pa zenera. Ndinazemba kutulukira khomo lakumbuyo, ndinadzera kupansi.

Pamenepo anali atagona mwanayo apo, ku chipatala, chipinda chayekha, ntchentche ziri mmaso ake onse aang'ono monga choncho. Ine ndinatenga choingitsira udzudzu chakalecho, ndinaziingitsa izo, ndipo nkudzachiika icho pa iye. Ine ndinagwada pansu, ine ndinati, "Mulungu, apo agona abambo anga ndi mchimwene, uko, ndipo maluwa ali pa manda awo. Apo akugona Hope, wagona uko. Ndipo apa pali mwana wanga, akufa. Musamutenge iye, Ambuye."

¹⁷¹ Iye anangokokera pansu katani, ngati akufuna kunena kuti, "Khala chete. Ine sindikufuna kuti ndikumvere iwe, nkomwe." Iye samayankhula nane nkomwe.

¹⁷² Ndiye, ngati Iye sakuyankhula ndi ine, iyo ikhala nthawi ya Satana. Iye anati, "Ndipo ine ndimaganiza kuti iwe umati Iye anali Mulungu wabwino. Nanga ndi chiyani chonse ichi chimene iwe ukufuula? Iwe ndiwe mnyamata chabe. Tayang'ana konsekonse, mu mzindamu. Mtsikana aliyense ndi mnyamata aliyense amene iwe unayanjanapo naye akuganiza kuti iwe unachita misala. Iwe watero." Tsopano, iye sakanandiuza ine kuti kulibeko Mulungu, chifukwa ine ndinali nditaziwona kale Izo. Koma iye amandiuza ine kuti Iye samasamala za ine.

¹⁷³ Ndinakhala usiku wonse, utali wa tsiku lonse. Ine ndinanena izo kwa Mulungu, "Kodi ine ndachita chiyani? Ndiwonetseni ine, Ambuye. Musalole kuti osalakwa avutike chifukwa cha ine, ngati ine ndalalukwitsa." Ine sindimadziwa kuti Iye anali akundiyesa ine. Koma mwana aliyense amene amabwera kwa Mulungu amayenera kuti ayesedwe. Ine ndinati, "Ndiuzeni ine zimene ndachita. Ine ndikazikonza izo. Ndi chiyani chimene ine ndachita koma kulalikira tsiku lonse, utali wa usiku wonse, ndipo ndimangomupatsa Iye moyo wanga, mosalekeza? Kodi ine ndachita chiyani?"

Satana anati, "Izo nzoona. Iwe ukuwona, tsopano, pamene izo zafika kwa iwe, ndipo iwe wawauza onse a iwo kuti iwe umakhulupirira kuti Iye ndi mchiritisi wamkulu, ndipo ndi uyo mwana wako wagona apoyo, akufa. Iye akukana ngakhale kuti akumve. Mkazi wako anafa ndi chibayo cha chifuwa. Iwe umati

Iye amatha kuchiritsa khansa, ndipo ndi Uyo apo. Tsopano, iwe umakamba za Iye kukhala wabwino, ndi mmene Iye aliri wabwino kwa anthu. Nanga bwanji iweyo?”

¹⁷⁴ Kenako ine ndinayamba kumumvetsera iye. Kumeneko ndi kulingalira. Ine ndinaganiza, “Izo nzoona.”

Anati, “Iye akudziwa... iwe sukusowa kuchita kunena Mawu, *ungomuyang'ana* mwana wakoyo, ndipo iye akhala moyo.”

Ine ndinati, “Izo nzoona.”

“Ndipo zochuluka zimene iwe wamuchitira Iye, ndipo komabe izo ndi zimene Iye akukuchitira iwe.”

¹⁷⁵ Ine ndinati, “Uko nkulondola.” Ine ndinayamba kuganizira. “Chabwino, chiyani?” Mukuona? Chirichonse chimayamba kuphwasuka, pamene uyamba kulingalira. Koma, pamene izo zifika pa Chijachi, Icho chimagwira. Icho chinakhalabe pamenepo. Ine ndinali wokonzeka kuti ndinene kuti, “Ndiye ine ndisiya.”

Koma pamene izo zinafika pansi kufika pakuti mphamvu zolingalira zonse zatha, ndiye izo zinadzafika ku Moyo Wamuyaya uja, Kubadwa kwatsopano kuja. Nanga bwanji ngati Iwo ukanakhala kuti munalibemo umo? Nanga bwanji ngati zikanakhala kuti ndinalibe Iwo? Ife sibwenzi titadziwana wina ndi mzake mmene ife tikuchitira tsopano. Tchalitchi chino sibwenzi chiri pano monga chonchi, masauzande ndi mamillioni kuzungulira padziko. Koma, ndikuthokoza Mulungu, Icho chinali mmenemo.

¹⁷⁶ Kenako pamene ine ndinadzaganizira, “Chiyani? Kodi Ine ndi ndani, mulimonse? Kodi Ine ndi ndani, kuti ndizimufunsa wolemekezeka Wake? Kodi Ine ndi ndani, kuti ndizimufunsa Mlengi amene anandipatsa ine moyo wanga womwe kuno pa dziko lapansi? Kodi ine ndinamutenga kuti mwana ameneyo? Ndi ndani amene anampereka iye kwa ine? Si wanga, mulimonse. Iye anangondibwereka iye ine, kwa kanthawi.”

Ine ndinati, “Satana, choka kwa ine.” Ine ndinapita, ndinakaika dzanja langa pa mwanayo. Ine ndinati, “Mulungu akudalitse iwe, wokondedwa. Mu miniti, adadi akutengera iwe kumusi, akakuika iwe mmanja mwa amayi. Angelo adzatengera solo yako yaying'ono kupita nayo kutali. Ndipo ine ndidzakakumana nawe mmawa umenewo.”

Ine ndinati, “Ambuye, Inu munampereka iye kwa ine. Inu mukumutenga iye. Ngakhale Inu mutandipha ine, monga ananenera Yobu, komabe, ine ndimakukondani Inu ndipo ine ndikukukhulupirirani Inu. Ngati inu mudzanditumiza ine ku gehena, ine ndidzakukondani Inu, mulimonse. Ine sindingathe kuchoka kwa icho.” Ndi zimenezotu.

Kungokhala wa luntha, icho chonse chingaswekepo. Koma iwe ukuyenera kukhala pa ubale wa wekha. Iwe ukuyenera kubadwa mwatsopano.

¹⁷⁷ Ndi chifukwa chake atumiki amachokapo, milandu yaikulu ndi zinthu. Iwo amati, “Palibepo chinthu chotero ngati machiritso Auzimu. Palibepo chinthu chotero ngati zinthu izi.” Iwo sanayambe akhalapo pa malo opatulika awo, monga ine ndimayankhulira mmawa uja. Iwo sakudziwa kanthu ka Iwo. Iwo anganene bwanji kuti iwo ndi ana a Mulungu, ndipo nkumakana Mawu a Mulungu? Inu mungachite bwanji zimenezo, kuwukana Mzimu Woyera womwewo umene unakugulani inu?

¹⁷⁸ Oh, ingokumbukirani, Yesu anadzichepetsa Yekha, mpaka ku imfa, chifukwa cha inu. Iye sanali wofuna zokangana. Pamene iwo anamulavulira pa nkhope Yake, Iye sanawalavulire mobwezera. Pamene iwo anamumwetula ndevu Zake, Iye sanawamwetule zawozo. Pamene iwo anamumenya Iye khofi mbali imodzi ya nkhope, inayo, Iye sanawamenye iwo. Iye anawapempherera iwo, anapitirirabe, modzichepetsa. Iye anali chitsanzo cha kudzichepetsa.

¹⁷⁹ Iye anali wodzaza chikhulupiriro. Chifukwa chiyani? Iye ankadziwa kuti Mawu Ake sakanalephera. Iye anakhala moyo kwambiri mwa Mawu mpaka Iye anadzakhala Mawu.

O Mulungu! Mundilole ine ndigwire manja anga awiri onse kwa Mulungu, pamaso pa omvetsera awa. Mundilole ine ndikhale monga chomwecho. Mulole Mawu awa akhale chomwecho, kuti ine ndi Mawu awa tikhale chinthu chofanana: mulole mawu anga akhale Mawu awa; mulole kusinkhasinkha kwa mtima wanga; mulole kuti Iye azikhala mu mtima mwanga, mmalingaliro anga; mumange malamulo Ake pa chimtengo cha luntha langa; muzimangilire izo pa chimtengo cha mtima wanga; mundilole ine ndizingomuwona Iye; pamene mayesero abwera, mundilole ine ndizimuwona Khristu; pamene zinthu zalakwika, mundilole ine ndizingomuwona Iye; pamene ine ndakonzeka, ndipo mdani akuyesetsa kuti andikwiyyitse ine, mundilole ine ndizimuwona Yesu, Iye angachite chiyani?

¹⁸⁰ Iye anali mochuluka kwambiri mu Mawu, mpaka Iye ndi Mawu anadzakhala chinthu chomwe chomwecho. Penyani.

¹⁸¹ Iye samasowa kuti azikangana nawo. Iye ankadziwa kuti Iyeyo ndi Mawu anali mmodzi. Iye ankadziwa kuti Iye anali Mawu a Mulungu akuwonetseredwa, ndipo kuti kulamula kwa Mulungu pamapeto kukanadzagonjetsa dziko. Iye ankadziwa zimenezo, Mawu Ake. Iye anali ndi chikhulupiriro. Iye ankadziwa kumene Iye. Iye sankasowa kuti azichita kukambirana, ndikuti, “Pano, inu mukhoza kubwera *kuno*.”

¹⁸² Mdierekezi anati, “Tsopano, taona, Iwe ukhoza kuchita zozizwitsa. Iwe ukudziwa Iwe uli ndi chikhulupiriro chachikulu.

Iwe ukhoza kuchita zozizwitsa. Ine ndikumangira Iwe nyumba, kukula kwake pawiri kuposa ya Oral Roberts. Chifukwa, anthu onse. . . Chi—chinthu chokhacho chimene Iwe ukuyenera kuchita, uwawonetse iwo. Ulumphe kuchokera pa nyumba iyi apa, ungolumphira pansu, chifukwa kunalembedwa, mwaona, ‘Angelo akunyamulira Iwe mmwamba, kuwopa kuti nthawi iliyonse phazi lingamenye pa mwala.’” Mukuona?

Iye ankadziwa kuti Iye anali ndi mphamvu. Iye ankadziwa kuti Iye akanatha kuchita zimenezo. Iye ankadziwa kuti izo zinali mwa Iye, koma Iye sankafuna kuti ayigwiritse ntchito iyo mpaka Mulungu atamuza Iye kuti atero. Mukuona? Iye amafuna kuti izo zizikhala Mulungu mwa Iye, zizikhala Mawu mu zonse. Ndipo Iye ankadziwa zimenezo, pamene Iye ayankhula chirichonse, kuti izo zinali Mawu a Mulungu; ndipo ngakhale miyamba ndi dziko lapansi zitapita, Mawu amenewo tsiku lina adzagonjetsa.

¹⁸³ Iye sanali wokangana ndi kumadyana. Iye anali kungoyankhula Mawu a Mulungu basi. Mawu aliwonse amene abwera kuchokera mmilomo Yake amakhala Mawu odzozedwa a Mulungu.

Kodi izo sizingakhale zopambana ngati ife tinganene kuti, “Mawu anga ndi Mawu a Mulungu ndi amodzi. Chimene ine ndimanena, Iye amachilemekeza icho, chifukwa ine sindimachita kanthu mpaka Iye atandiuza Ine poyamba”? Oh, ndi chimenecho chitsanzo chanu. Ndi umenewo moyo woyenera Uthenga.

¹⁸⁴ Osati ansembe awo amene anali ophunzira kwambiri ndi opukutidwa, ndi okhala ndi maulemu aakulu onse awo, ndi kumaima ndi kumapanga mapemphero aatali, ndi kumakawononga nyumba za azimayi amasiye, ndi kumakakhala pa mipando yapamwamba mu—mu msonkhano, zinthu zonse izi kumeneko. Apo panali. . . Umenewo sunali moyo woyenera Uthenga.

Koma Iye anali woyenera Uthenga, mochuluka kwambiri, mpaka kuti Mulungu anati, “Uyu ndi Mwana Wanga wokonedwa, mwa Iye Ine ndikondwera. Mumvereni inu Iye. Mawu Anga ali Iye. Iye ndi Mawu Anga. Iye ndi Ine tiri mmodzi.”

¹⁸⁵ Dziwani, penyani ichi tsopano. Iye ankadziwa kuti Mawu Ake potsiriza adzagonjetsa dziko lapansi. Iye ankadziwa kumene Mawu Ake amachokera. Iye ankadziwa kuti Iwo sangalephere nkomwe, ndi chifukwa chake Iye anati, “Miyamba ndi dziko lapansi zidzapita, koma Mawu Anga sadzalephera konse.” Mukuona? Iye amakhoza kunena zimenezo. Ameneyo anali Munthu Amene Iye ndi Mawu a Mulungu anadzakhala mmodzi. Iye ananena kwa iwo. . .

“Inu mukuyenera kuchita *ichi* ndi *icho*.”

¹⁸⁶ Iye anati, “Ndi ndani anganditsutse Ine za tchimo? Ndi ndani anganditsutse Ine?” *Tchimo* ndi “kusakhulupirira.” “Ngati Ine, ndi chala cha Mulungu, ndimatulutsa ziwanda, ana anu amatulutsa izo ndi chiyani?” Mukuona? Izo sizinali zimenezo, chotero icho chinayenera kuti chinali chinachake. Mukuona? “Ngati ine . . .”

Iwo anati, “Chabwino, ife tatulutsa ziwanda.”

¹⁸⁷ Iye anati, “Ngati ine ndingachite izo ndi chala cha Mulungu, Mawu otsimikiziridwa a Mulungu, ndiye ana anu amatulutsa izo ndi chiyani? Ndiye inu mukhale oweruza.”

¹⁸⁸ Anthu a masiku Ake, ndipo anthu amamuseleula Iye, anali kukamba za Iye. Koma, Iye, iwo anamuchititsa manyazi Iye, mwanjira iliyonse yomwe iwo akanathera. Anamuza Iye za zoipa zonse, zomutsutsa Iye, koma Iye anapitirirabe.

Tsopano ine ndikufuna kuti nditseke mu miniti, ponena izi.

¹⁸⁹ Anthu amasiku ano ali mulu wa amanjenje. Anthu a tsiku lino ali mulu wa amanjenje. Iwo amawopa kuti atenge malonjezo a Mulungu. Amuna a tchalitchi, bungwe la tchalitchi, mabungwe a tchalitchi akuwopa kuti atenge kubetchera kwa Malemba a Mulungu a tsiku lino. Iwo akuzindikira. Iwo akuzindikira kuti zochitika zawo zamakono ndi uthenga wawo wachitukuko umene iwo amalalikira sungathane ndi chitsutso cha ora lino, chimodzimidzinso monga Samsoni sanakwaniritse izo mu chikhaliidwe chake. Izo zinatengera Mulungu.

Ndipo apa pali dongosolo limene linalonjeza izo. Ine ndifika kwa izo mu miniti.

¹⁹⁰ Ine ndikufuna kuti ndiyimike kaye liwu limenelo, miniti. Ngakhale iwo amadzitcha okha Mkristu, iwo amatenga tizikhulupiriro, tizikhulupiriro topangidwa ndi munthu, kuti tikatenge malo a Mawu a Mulungu. Chotero, iwo akhoza kutenga kachikhulupiriro, chifukwa munthu wapanga izo. Koma iwo amawopa kuti akaike chikhulupiriro chawo kunja uko mwa Mulungu amene iwo amanena kuti amamukonda. Uko nkulondola. Ndiye inu mungati moyo umenewo ndi woyenera Uthenga? Sizingatheke, ngakhale iwo atakhala mamembala a mpingo. Koma kumeneko sikukhala woyenera Uthenga. Ayi, ndithudi.

¹⁹¹ Uthenga! Yesu anati, “Pitani pa dziko lonse ndipo mukalalikire Uthenga kwa cholengedwa chirichonse. Zizindikiro izi zidzawatsatira okhulupirira.”

Ndipo pamene inu mukana kuti izo zingatsatire okhulupirira, inu mungakhale bwanji ndi moyo . . . Ziribe kanthu, inu mukhoza kusanena mawu oipa, inu mukhoza kusunga malamulo khumi onse, izo sizingakhale ndi chochita chimodzi ndi izo. Izo zikadali zosayenerabe Uthenga. Mukuona? Izo sizingakhale.

Ansembe amenewo amasunga zimenezo, ndipo komabe sanali oyenera ayi. Iye anati, “Inu ndi wa atate anu, mdierekezi.” Ndi ndani akanaloza chala pa mmodzi wa amuna amenewo? Akakhala ndi chilema chimodzi, ndipo iwo amagendedwa mopanda chifundo. Amuna oyer! Ndipo Yesu anati, “Ndinu wa atate anu, mdierekezi,” pamene Uthenga unawafikira.

¹⁹² Ngakhale iwo amadzitcha okha Akhristu, iwo amakonda kugwiritsitsa ku tizikhulupiriro, tizikhulupiriro tawo. Oh! Tizikhulupiriro timayambitsa ndi kukwaniritsa zoganza za anthu amakono a tsiku lino. Ndipo munthu amene angachite bwino mu tsiku lino, akuyenera kuyenda ndi kaganizidwe ka kachitidwe kamakono. Mundilole ine ndinene zimenezo mwabwino ndi momveka. Mukuona? Mwamuna, kuti zako zikuyendere bwino, iwe ukuyenera kuyenda ndi kaganizidwe kamakono ka tsiku lino. Izo...Iwo amapita, ndikumati, “Oh, kodi iye si wokondedwa? Kodi iye si wodabwitsa? Iye akhoza kukhala pamenepo mowongoka kwambiri, ndipo iye samatisunga ife nkomwe kupitirira maminiti fifitini. Ndipo abusa athu nthawizonse samatizazila ife za zinthu izi.”

Manyazi pa m’busa ameneyo. Mwamuna aliyense amene angaime paguwa ndi kumayang’ana pa tchimo la tsiku lino, ndipo osafuula mokweza, pali chinachake cholakwika ndi mwamuna ameneyo. Iye si woyenera Uthenga umene iye amadzinenera kuti akulalikira. Uko nkulondola. Chotero, pochita zimenezo, iwo amadzipangira okha zowiringula, ponena kuti, “Tsopano, taonani, osonkhana anga!”

¹⁹³ A—mwamuna anabwera kuno, osati kale kwambiri, ku tchalitchi chinachake chachikulu, ndipo iye amalemba lingaliro. Ndipo iye anati, “Ine ndikulemba pa machiritso Auzimu.” Anati, “M’bale Branham, ife timakukondani inu, mu chipembedzo chathu.” Chimodzi cha zipembedzo zazikulu, chimodzi cha zazikulu mu fuko, kapena mdziko. Ndipo iye anati, “Ife timakukondani inu, mu chipembedzo ichi.” Iye anali komwe kuno ku Jefferson Villa. Koma, anati, “Ine ndabwera kuti ndidzafufuze za machiritso Auzimu awa.” Iye anati, “Pali cholakwika chimodzi chokha chimene mpingo wanga umachipeza kwenikweni.” Mukuona? Iye anati, “Inu mumayanjana ndi Achipentekoste ambiri.”

Ine ndinati, “Chabwino, tsopano, inu mukudziwa, uko nkulondola.” Ine ndinati, “Izo nzoona. Inu mukudziwa, ine nthawizonse ndakhala ndikufuna mwayi woti ndichoke kwa iwo.” Ine ndinati, “Ine ndikuuzani inu chiyani. Ine ndibwera ku mzinda wanuwo, inu munditengere tchalitchi chanu chizindithandizira ine.”

“Oh,” iye anati, “iwo sangachite.”

Ine ndinati, “Ndicho chimene ine ndimaganza. Ndi zimene ine ndimaganza.”

¹⁹⁴ Anati, “Inu mukuona, chipembedzo changa sichingaima ndi zimenezo.” Chowiringula chake ndi chimenecho, monga, “Ine ndakwatira mkazi,” kapena “ine ndagula goli la ng’ombe.” Ine sindikusamala kaya muli ndi madigrii a udokotala angati, ndi mmene amakuwonerani, ndi chipembedzo chanu. Utumiki woterowo siwoyenera Uthenga umene unalembedwa mu Bukhu ili. Kulondola.

¹⁹⁵ Membala wa mpingo aliyense amene angatenge mbali ndi zinthu ngati zimenezo, ndipo nkumadzitcha yekha Mkristu! Ndipo nkumapita kunja uko ndikukhala...Ndipo akazi kumadula tsitsi lawo, ndi kumavala zovala zimene Baibulo limanena kuti iwo asamavale. Amuna kumangopitirira mmene iwo akuchitira tsopano, “maonekedwe aumulungu,” kumamwa ndi kumasuta ndudu, ndi kumakwatira kangapo ndi kumakhala madikoni a mpingo ndipo ngakhalenso azibusa, ndi zina zotero. Ndipo anthu amene amalolera zinthu ngati zimenezo, moyo wa mtundu umenewo si woynenera Uthenga.

¹⁹⁶ Mkazi amene angamayende, ndi kufika pa telefoni ndi kulalata, ndi kumayambitsa maphokoso mu tchalitchi, ndi zinthu monga zimenezo, umenewo si moyo woynenera Uthenga umene ife titi tiwuimirire. Munthu aliyense amene angagawanize tchalitchi, ndi kuyambitsa makangano pakati pa anthu, ndi zinthu monga choncho, siwoyenera Uthenga umene ife tikulalikirawu. Ndendende. “Iwo ndi mawonekedwe aumulungu, kumakana mphamvu yake,” mphamvu ya Mulungu imene imakuletsani inu kuti musachite zimenezo.

¹⁹⁷ Zindikirani, tsopano, iwo samachita zimenezo. Iwo sangachite izo basi. Iwo ali ndi chowiringula, chakuti, mpingo wawo sukhulupirira mu Zimenezo. Iwo . . .

Chabwino, koma, Yesu akhoza—kunena kwa munthu, usikuuno, kuyankhula kwa mtima wake ndikuti, “Ine ndikufuna kuti iwe upite, ukalalikire Uthenga wathunthu.”

“Mpingo wanga sumaima ndi Zimenezo, Ambuye. Inu mundikhululukira ine, ngati Inu mungathe. Ine ndimachita kutumidwa. Ine—ine—ine, Inu mukudziwa, ndine m’busa, umodzi wa mipingo yaikulu kwambiri mu mzinda uno, Ambuye. Oh, ife timatamanda Dzina Lanu kumusi uko! Inde, Bwana. Ife ndithudi timatero. Ine sindingachite zimenezo.” Chowiringula chomwecho, chinthu chomwecho. Chotero iwo samabwera ku phwando lauzimu la olonjezedwa Ake, Mawu otsimikiziridwa.

¹⁹⁸ Kodi Yesu sanati, “Komwe kuli nyama, mphungu zidzasonkhanako”? “Mphungu,” osati akhwangwala, tsopano. Mphungu! Komwe kuli zoipa, ndi—ndi—zovunda, ndiye akhwangwala amasonkhanako. Koma kumene kuli Nyama, yatsopano yabwino, mphungu zimasonkhanako. Mukuona? Ndithudi. Kumene Mawu, Chakudya cha mphungu, izo zimasonkhanako.

¹⁹⁹ Chotero iwo sakubwera ku phwando lauzimu kumene iwo aitanidwako. Kodi inu mukukhulupirira kuti Mulungu anamuitana Amerika, zaka fifitini zapitazo, ku chitsitsimutso chachikulu, ku phwando lauzimu? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Kodi iwo anabwera? Ayi, bwana. Ayi, bwana. Ndiye, kukana kuti abwere, kodi moyo umenewo ndi woyenera Uthenga, ngakhale iwo amadzitcha okha zimenezo?

²⁰⁰ Pamene munthu anabwera kwa ine, osati kale kwambiri, ndipo anadzakhala pa tebulo, ndikuti, “M’bale Branham, ine ndikufuna kufikira mbali ina ya tebulo,” bambo wachikulire, “Ine ndikufuna ndigwire dzanja lanu. Ine ndimakukondani inu.” Ine ndinali mu tchalitchi ndipo ine ndinamunva iye akulalikira. Anati, “Ine ndimakukondani inu. Ine ndikukhulupirira kuti ndinu wantchito wa Mulungu.”

Ine ndinati, “Zikomo, dokotala. Ine ndimakukondani, nanenso.”

Iye anati, “Ine ndikufuna ndikuuzeni inu mmene ndimakukonderani inu, ngati m’bale.” Ndipo anati, “Inu mwaiwona mfumukazi yanga yaing’ono yakhala apa, mkazi wanga? Inu mukumukumbukira iye?”

Ine ndinati, “Ine ndikutero.”

Anati, “Adokotala anamupatsa iye masabata awiri okhala moyo, ndi khansa ya chophuka. Ndipo inu munabwera mu mzindawo ndipo inu munamupempherera iye. Ndipo munayang’ana mmwamba, ndipo munawona masomphenya. Munayang’ana mmbuyo ndipo munandiuza ine, ‘PAKUTI ATERO AMBUYE, iye achiritsidwa.’” Dontho lalikulu kunsana kwake, linangolowa mkati monga *choncho*, linkawoneka ngati chachikulu kwambiri...ngati gawo la bere la mkazi litakokedwera mkati, kunsana kwake, pa fupa lake la kunsana penipeni. Palibepo ngakhale dontho la icho, lero. Anati, “Ndi iyo mfumukazi yanga apo, wamoyo lero.” Anati, “Ine ndingachite chiyandinso koma kukukondani inu, chifukwa chopemphera pemphero lija la chikhulupiriro? Ine ndingalekerenji kukukhulupirirani inu kuti ndinu—watchito wa Ambuye, pamene inu munandiwona ine, ndipo munadzandiuza ndendende basi zimene zikanadzachitika?” Iye anati, “Tsopano ine ndiri ndi chinachake cha inu, M’bale Branham.” Iye anati, “Ine ndi wa gulu lalikulu la Chipentekoste limene liripo.”

Ine ndinati, “Inde, bwana. Ine ndikudziwa zimenezo.”

Iye anati, “Ine ndimayankhula ndi abale, osati kale kwambiri, ndipo iwo anandiuza ine kuti ndilumikizane nanu, ndi kukuuzani inu kuti ndi zochititsa manyazi kuti inu munatengera utumiki woperekedwa ndi Mulungu uwo kwa gulu la anthu aku mtsinje ndi kozungulira monga *choncho*.”

Ine ndinati, “Uko nkulondola?”

Anati, “Inde.” Anati, “Mulungu anatumiza utumiki umenewo kuti udzakhudze malo a mtsempha, malo aakulu, monona.”

²⁰¹ Ine ndinamuwona mdierekezi akuyankhula pomwe apo. Ine ndinaganiza, “Eya. ‘Ulumphire pansu kuchokera pa phiri ili, ndipo uwonetse, iwe ukudziwa, kuchokera pa nyumba iyi.’” Mukuona? Mukuona?

Ine ndinaganiza, “Tangomutsogolera iye patali pang’ono.” Amayi anga okalamba anakonda kunena kuti, “Ukaipatsa ng’ombe chingwe chachitali, iyo imadzipachika yokha.”

Ine ndinati, “Nkulondola uko?”

“Inde.” Anati, “Ndi zamanyazi, ndi zimene inu mumachita.” Anati, “Inu ndi ndani? Lero inu mumavutika kuti mudzigulire nokha chakudya.” Ndipo anati, “Tamuwonani Oral Roberts ndi iwo, anadzabweramo, ndipo anatuluka kumeneko ndi gawo limodzi pa handiredi la utumiki umene inu muli nawo. Taonani zimene iwo ali nazo.”

Ine ndinati, “Eya. Uko nkulondola.” Mukuona?

Ndipo iye anati, “Gulu langa likutengani inu. Ife tikulowetsanimu inu, ngati—ngati mmodzi wa abale athu. Iwo onse adzakupatsani inu dzanja lamanja la chiyanjano, ndipo ife tizikutumizirani ndege, ndi kumakupatsani inu malipiro anu a faifi handiredi pa sabata, kapena zochulukirapo ngati inu mukufuna izo. Ndipo ife tidzakutumizani inu ku mzinda waukulu uliwonse mdziko.” Izi zinachitikira mu Phoenix kumene, Arizona, tikuyang’anizana pa tebulo. Ndipo iye anati, “Ndipo ife tizidzakulipirirani zanu...” Anati, “Zikadzatero tidzaliudza dziko, dziko lakunja, tiwauza akuluakulu, anthu akuluakulu, apamwamba...” Anati, “Inu nthawizonse mumayankhula za oshota. Ife tiri nawo olemera.” Anati, “Tidzafuna iwo adzawone dzanja la Ambuye. Kenako ine ndidzawalola iwo azidzayenda ndi akazi anga, ndi ena, kuti azidzatsimikizira kuti zinthu zimenezo zimene inu mumanena zimakwaniritsidwa.”

²⁰² Ndinati, “Inde, bwana. Izo zikhoza kukhala zopambana.”

Tsopano, mwaona, mwamunayo, pa udindo wa D.L., L.L.D., mlembi wa mabuku, mwaona, dokotala wa zolemba, wolemba wabwino, mwamuna wabwino. Mukuona? Iye samawadziwa Malemba.

Kodi inu mumadziwa kuti Mngelo amene anachita ntchito za mtundu umenewo sanapite konse ku Sodomu? Iye anatsala ndi gulu la oyitanidwa atuluke, Abrahamu.

Iye samazidziwa izo basi. Ine ndinangomusiya iye yekha, ndinangokhala pamenepo pang’ono chabe. Ine ndimangofuna kuti ndiwone kuti amafuna chiyani. Ine ndinati, “Chabwino, kodi ine ndikuyenera ndizichita chiyani?”

Anati, “Chabwino, M’bale Branham, chinthu chokhacho chimene iwo ananena . . . Ife tinakambirana izo, zinthu pang’ono, zinthu pang’ono zosafunikira zimene inu mumaphunzitsa, kuti inu mungozisiya izo pambali.”

Ine ndinati, “Mwachitsanzo, chiyani, m’bale?”

“Oh,” iye anati, “ubatizo wanu, inu mukudziwa. Inu mukudziwa, inu mumakhala ngati mumabatiza ngati aumodzi, chinachake monga choncho.” Anati, “Zinthu zazing’ono monga zimenezo.”

Ine ndinati, “Oh?” Ine ndinapitirira.

Ndipo iye anati, “Umboni woyambirira; ndi alaliki achikazi; ndi zinthu pang’ono zazing’ono basi monga zimenezo.”

²⁰³ Ine ndinati, “Uh-huh?” Ine ndinati, “Inu mukudziwa, ine ndikudabwa kuti wantchito mmodzi wa Mulungu akhoza kumupempha wantchito wina wa Mulungu, mutatha kupereka ulemu kwa ine mmene inu mwachitiramu, ndi kunditcha ine mneneri, ndi kumadziwa kuti Mawu a Ambuye, kapena vumbulutso la Mawu, limabwera kwa mneneri. Ndipo inu mukupotoloka, Dokotala Pope, (izo sizikuyankhula za luntha lanu labwino), ndipo mukhoza kunena ndi kumupempha, wantchito mmodzi wa Mulungu, inu mukumupempha wantchito wina wa Mulungu kuti alekelele pa chinthu chimene . . .? . . . chimatanthauza zochuluka kwa iye kuposa moyo pawokha.” Ine ndinati, “Ayi, bwana, M’bale Pope. Ine sindingachite zimenezo mwanjira iliyonse. Ayi, bwana.”

Ndi chiyani chimenecho? Ilipo njere ya Moyo Wamuyaya; kukhala moyo kapena kufa, kaya ndiwe munthu wamkulu kapena sindiwe munthu wamkulu.

²⁰⁴ Ine ndinadutsa, tsiku lina . . . Mopanda kunyozetsa amuna awiri awa. Ine ndinayang’ana kumeneko, ndipo panali chithunzi chachikulu kumeneko ku Tulsa, Oklahoma; malo atsopano a Oral Roberts akubwera, seminare yoti azikaphunzitsirako atumiki. Mtengo wake idzakhala (Ndipo ine ndikudziwa Demos Shakarian, M’bale Carl Williams, ndi iwo amene ali pa bodi ya matrastii a zimenezo.) madola fifite millions, ndi nyumba ya madolla firii-millions; mnyamata wa Chipentekoste, izo ndi zochuluka kwambiri zimene Mulungu wamuchitira iye.

²⁰⁵ Ine ndikuganiza, “Ine, ndi seminare? Ine ndimatsutsana nazo izo, kuyamba ndi kuyamba.”

²⁰⁶ Ndipo izo zinati, “Kwawo kwa mtsogolo kwa seminare yaikulu ya Oral Roberts.” Ndinapitirira kumatsika msewuwo, apo panali chinthu chachikulu chamakono. Ndipo Oral Roberts, muhema yaing’ono yong’ambika, anabwera ku msonkhano wanga mu Kansas City, Kansas.

Izo zinati, “Kwawo kwa mtsogolo kwa Tommy Osborn,” oh, anthunu, pafupifupi malo a madolla firii kapena foro milioni akukwera mmwamba monga choncho.

Ndipo pamenepo, Tommy Osborn, mmodzi wa amuna abwino Achikhristu. Iye ndi mwamuna weniweni, mwamuna weniweni wotumizidwa ndi Mulungu. Anaima tsidya lina la msewu kumeneko; mnyamata wamng’ono, wamanjenje, mnyamata wamng’ono ndi mtsikana mu galimoto; anathamanga mozungulira, anatuluka. Anati, “M’bale Branham, ine ndinali kumeneko pamene ine ndinamuwona wamisala uja akuthawa. Ndipo ine ndinakuwonani inu mukuloza chala chanu pa nkhope yake, ndikuti, ‘Mu Dzina la Yesu Khristu, tuluka mwa iye.’ Ine ndinamuwona iye akugwera pa mapazi anu; iye atatha kupereka ulosi wake, anati, ‘Usikuuno, ine ndikugwetsera iwe pakati pomwe pa omvetsera a anthu sikisite-faifi handiredi awo.’” Ndipo anati, “Ine ndinakuwonani inu mutaima pamenepo, simunakweze mawu, ndipo munati, ‘Mu Dzina la Ambuye, chifukwa choti iwe watsutsana ndi Mzimu Woyera, usikuuno, iwe ugwera pa mapazi anga.’ Iye anati, ‘Ine ndikuwonetsa iwe mapazi a amene ine nditi ndigwerepo.’”

²⁰⁷ Ndipo ine ndinati, “Tuluka mwa iye, Satana.” Iye anangogwera chagada ndipo anakanikizira phazi langa pansi.

Iye anati, “Mulungu ndi Mulungu, M’bale Branham. Ndizo zonse.” Anati, “Ine ndinazikhomera ndekha mnyumba kwa masiku awiri kapena atatu.” Iye samabweza nk'honya. Iye amanena za izo. Iye samachita manyazi ndi izo. Anati, “Inu mukuganiza kuti ine ndiri ndi mphatso ya machiritso?”

²⁰⁸ Ine ndinati, “Uyiwale zimenezo, Tommy. Iwe unatumizidwa kuti udzalalikire Uthenga. Pita, ukalalikire Iwo. Uzipita ndi M’bale Bosworth uko.”

²⁰⁹ Ine ndinayang’ana kumeneko, ndipo ine ndinawona. Ine ndinayamba awiri onsewo asanayambe.

Ine ndinaganiza, “Apo pali Oral Roberts ndi makina faifi handiredi, amene ngakhale dzanja la munthu silimagwira makalata ake; madola foro milioni mmakalata, chaka chatha.” Foro milioni; gawo limodzi la magawo foro a ndalama zonse zimene zinatoleredwa, mu dziko lonse la Chikhristu, konsekonse. Gawo-limodzi la magawo foro a ndalama mu Chikhristu chonse zimabwera kwa munthu mmodzi. Ndi malo bwanji! Ine ndinapita kumeneko kuti ndikawawone iwo.

²¹⁰ Ndipo, tsopano, Oral ndi m’bale wanga. Mai! Ine ndimamukonda iye. Iye ndi munthu weniweni, mwamuna weniweni, ndipo ine ndimamukonda iye. Ndipo iye amangoganizira moposetsa za ine, ndipo ine ndimatero za iye, nanenso. Ife basi sitimagwirizana pa—pa Malemba.

Ndipo, Tommy Osborn, chimodzimidzinsu. Ine ndimangoganizira moposetsa za iye. Iye ndi mmodzi wa amuna abwino amene ine ndakumanapo nawo, Tommy Osborn.

“Ndipo amuna amenewo,” ine ndinaganiza, pamene ine ndinapita mu ofesi yawo ndikuwona zimene iwo ali nazo, “Ine ndikuganiza ine ndingachite manyazi kuti iwo abwere, adzawone zanga”: taipilaita yaing’ono imodzi, ndipo ife kumayesetsa kutumiza makalata. Ndipo ndi chinthu bwanji! Chitakidwa kumapeto kwa ngolo, pa nthawi imeneyo. Ine ndinaganiza, “Izo zingakhale chiyani?”

Kenako ine ndinatuluka panja. Ine ndinaganiza, “Chabwino, ‘Kwawo kwamtsogolo kwa Oral Roberts.’ ‘Kwawo kwamtsogolo kwa Tommy Osborn.’ Wina samayakhulitsana ndi mzake.”

Chotero, ine ndimayenda chotsika msewu. Ine ndinaganiza, “Koma nanga bwanji ine?”

²¹¹ Ndipo Chinachake chinati, “Yang’ana mmwamba.”

²¹² Ndinaganiza, “Inde, Ambuye, mundilole ine ndisungitse chuma changa Kumwamba, pakuti uko ndi kumene kuli mtima wanga.” Tsopano, ine sindikunena zimenezo kuti ndimveredwe chisoni. Ine ndikungonena zimenezo chifukwa izo zinandichitikira, ndipo Mulungu akudziwa kuti izo nzoona. Mukuona?

²¹³ Chuma chanu chiri kuti? Kodi inu mukufuna kukhala wamkulu winawake? Ngati inu muli, sindinu kanthu. Inu mufike pa malo akuti inu sindinu wamkulu winawake. Inu mukufuna kukhala wantchito wamng’ono wodzichepetsa kwa Khristu. Ndiyo njira yake. Ndizo zonse.

²¹⁴ M’bale Boze ndi iwo akuyambitsa tchalitchi mu Chicago. Iwo anangowasiyira achipembedzo aja tchalitchi chaku Filadefiya. Tsopano iwo anali akuyankhula zomupeza munthu wina wa chikhothi chake mmbuyo monga *chonchi*, DD ina. Ine ndinati, “Inu mwasochera kale. Ngati inu mukufuna kuti mupeze m’busa weniweni wa tchalitchi chimenecho, mukampeze bambo wachikulire pang’ono wodzichepetsa amene sangathe nkome kuwerenga dzina lake, ndipo mtima wake uli pamoto kufuna Mulungu. Mukangomutenga bambo ameneyo. Ameneyo ndi amene inu mukuyenera kumutenga, winawake amene sakuzidziwa zinthu zonsezi, winawake amene samadzalamulira mwankhanza ndi kumayendetsa, ndi kudzakuikani inu mu mitundu yonse ya ngongole, china chirichonse, ndipo kumadzangokudyetsani inu Mawu a Mulungu. Ameneyo ndiye munthu woyenera kumutenga.”

Chotero, iwo sadzabwera ku phwando lauzimu. Ine ndikuyenera kuti nditseke. Ine ndadutsitsa nthawi tsopano. Mu pafupifupi maminiti sikisi, ife tikhala tikutseka, Ambuye akalola.

²¹⁵ Ine ndimamva ena akuti, “Koma, M’bale Branham, inu mukuyenera kubweza maneno amenewo.” Kumati, “Anthuwo si amisala. Anthu awa si amisala. Iwo angokhala kuti ndi ophunzira.” Iwo ndi amisala ophunzira, ndiye. Uko nkulondola. Eya. “Iwo si amisala. Iwo ndi ophunzira.”

Ndiye ine ndikufuna kuti ndikufunsi inu funso. Mukuona? Inu mukumvetsa. Ine ndikufuna kuti ndikufunsi inu funso ndiye. Chonde tafotokozani zochita zawo za lero, ngati iwo si amisala. Ndiuzeni ine chimene chimawapangitsa iwo kumachita mmene iwo akuchitiramu, ngati iwo si amisala; mwaona, munthu aliyense akukokerera chipembedzo chake, kudzikonda. Yesu sanali chomwecho. Iye sanali pachangu ndi chirichonse. Mukuona? Iye sanali wodzikonda. Iye anali chitsanzo chathu.

²¹⁶ Umbanda, fuko, fukoli liri ndi umbanda wochuluka kuposa umene linayamba lakhalapo nalo. Chavuta ndi chiyani? A zaka zammamini, mamembala a mpingo, akuchotsa miyoyo, amuna kuwombera akazi awo ndi banja, ndi kumawotcha ana awo. Ndipo taonani mmene umbanda ukupitira. Iwo si amisala? Ndiye vuto lawo ndi chiyani? Machitidwe awo ndi chiyani?

Mafuko openga ndi mphamvu, aliyense akufuna kutenga lililonse. . . onsewo ndi kuwapanga iwo akhale mbendera imodzi, fuko limodzi, kuti ikhale mbendera yawo ndi fuko lawo. Kupenga nazo mphamvu!

²¹⁷ Chivundi, bwanji, dziko lasanduka lachivundi kwambiri kuposa mmene linayamba lakhalirapo. Akazi ovula mmisewu, akazi ovula, ndipo nkumati iwo ali mmalingaliro awo abwino bwino? Iwo sangakhale. Iwo sangakhale basi.

²¹⁸ Mvetserani. Analipo munthu mmodzi mu Baibulo amene anadzivula zovala zake, ameneyo anali Legio. Iye anali atachita misala. Pamene Yesu anamupeza iye ndipo nkumupangitsa iye kuti aziganiza bwino, iye anadzavala zovala zake. Kulondola.

Nchiyani chimakupangitsani inu kuvula zovala? Mdierekezi. Uko nkulondola. Ndiye mukuti iwo si amisala? Muyambe kumapita chotsika msewu kuno, ndipo mudutse mabuloko foro a mzinda opanda kumuwona mkazi wovula, ndipo mubwerere mudzandiuze ine. Chabwino. Kafufuzeni.

²¹⁹ Ndiye inu mukuti iwo si amisala? Ndiye chavuta ndi chiyani? Iwo sangakhale kuti akuganiza bwino bwino. Mkazi woganiza bwino sangachite zimenezo; iye ali nako kuganiza kwabwinoko. Iye amadziwa zimene iye akudziveka yekha: gulu la adierekezi osilira kumeneko, basi amuna awutchisi, auve, otsika, oledzera, akupha, china chirichonse. Inu mukuti. . .

²²⁰ Dziko likumwa mowa kwambiri tsopano. Iwo akuwononga ndalama zambiri pa mowa, mu United States, kuposa zimene iwo amawononga pa zofunika za pakhomo. Ine ndikuganiza ndizo. . . Ine ndaiwala kuti ndi kangati kuchuluka kwake mmene ngongole ya mowa imakwanira chaka chirichonse, mu

fukoli, kuposa mmene izo zinkachitira. Ndipo kodi uchidakhwa umachita chiyani? Umakutumizani inu kwa azamisala.

²²¹ Khansa. Pamene madokotala azamankhwala ochokera pa dziko lonse amalemba mmagazini, ndi kukuuzani inu, “Khansa yozadza mmagalimoto.” Ndudu. Kukaiyika iyo pa makoswe, ndipo zatsimikiziridwa kuti izo zimakupatsani inu khansa ya mmapapo. Sevente peresenti ya iwo amakhala ndi khansa ya mmapapo chifukwa chosuta ndudu. Ndipo akazi amenewo ndi amuna amasuta izo ndi kupemerera izo pa nkhope yanu. Ngati zimenezo si misala, misala ndi chiyani?

²²² Pamene, Uthenga wa Yesu Khristu ukhoza kulalikidwa ndi kutsimikiziridwa, ndipo Mulungu wa Kumwamba mmawonekedwe a Lawi la Moto Lake nkuweyulira pa anthu ndi kuwonetsera kuti Yesu Khristu ali mu gawo lomaliza la Kubwera Kwake, kuwapatsa iwo chizindikiro chomaliza. Ndipo nkumaseka pa Iwo ndi kumauseleula Iwo, ndi kumadzitcha okha mamembala a mpingo; ndiyeno nkumati iwo si amisala? Tafotokozani zimenezo. Nthawi yanga ikupitabe. Koma ndikungofunsa ngati iwo si amanjenje. Ndithudi. Iwo ndi amisala ophunzira. Ndizo ndendende. Tafotokozani chikhaliidwe chawo. Inu simungathe.

²²³ Iwo amadula tsitsi lawo, amavala zovala zachidziko, amakayenda kunja pa msewu monga choncho. Ndipo Baibulo la Mulungu limachenjeza motsutsa izo, ngakhale mpaka kumuletsa mkazi kuti asapemphere ndi tsitsi lodula. Ndipo kumanena kuti mwamuna... Ndipo iye amachita zimenezo. Iye amadzinenera, iyemwini, kwa mwamuna wake, kuti iye ndi wopanda makhalidwe, iyemwini, ndipo iye ali ndi ufulu wamngwiro kuti akhoza kumusudzula iye ndi kumuchotsa kwa iye. Uko nkulondola ndendende. Mawu a Mulungu amanena zimenezo, ndipo akazi amamva zimenezo, ndipo akumapitirirabe kumavala tsitsi lalifupi, ndipo nkumadzitcha yekha Mkristu. Ngati iyo si misala, misala ndi chiyani? Ine ndikufuna winawake kuti andiuze ine kuti misala ndi chiyani, ndiye. Inde. Iwo ndi amisala.

²²⁴ Ophunzira mwapamwamba, madigrii, koleji! Ife timaika nthawi yambiri powaphunzitsa ana athu, a—algebra ndi biology, kuposa imene ife tikuyenera kuchitira ku Baibulo ndi Yesu Khristu. Mulibemo mwana mdziko lino amene sangakuuzeni inu kuti David Crockett ndi ndani. Palibepo magawo atu a iwo amene angakuuzeni inu kuti Yesu Khristu ndi Ndani. Ndiye, zimenezo si misala? Ndithudi, ndi choncho. Mmene ife tikhoza kumapitirira ndi kumapitirira ndi kumapitirira, mmene iwo akuchitira!

²²⁵ Ingokumbukirani. Ndipo mipingo ikuvomereza zimenezo, pamene Baibulo limatsutsa izo. Kodi utumikiwo ndi wamisala?

Amisala ophunzira. Ndizo ndendende. Mipingo ikuvomereza izo.

²²⁶ Kumbukirani Loti. Iye anali mwamuna wanzeru. Tayang’anani pa iye, miniti chabe tsopano. Musati—musati... Tiyeni tisatero... .

Mundikhululukire ine popitiriza maminiti angapo. Izi ndi—izi ndi zofunikira kwambiri. Izo zizipita... Inu mwabwera kuti mudzandimvere ine ndikupanga tepi iyi.

²²⁷ Taonani. Taonani. Tiyeni ife tiimikire miniti. Mupemphere mphindi chabe, mumtima mwanu, “Ambuye, mundilole ine ndiwone izo.” Atsegule kumvetsa kwanu. Mulole Mulungu achite izo. Tayang’anani pa... Mungotenga fuko lino, palokha. Tiyeni tiwone zimene Mulungu ananena.

²²⁸ Baibulo linanena, kuti, “Machimo a Sodomu amakhumudwitsa solo yolungama ya Loti tsiku ndi tsiku.” Iye analibe basi mtsempha wopanda psyete kuti ayime motsutsa izo. Kulondola uko? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Iye sakanakhoza kuchita izo, pakuti iye anali meya wa mzinda. Iye sakanakwanitsa. Koma Baibulo linanena, kuti, “Machimo a—a Asodomu anasautsa solo yake.” Iye ankadziwa kuti izo zinali zolakwika, koma iye analibe kulimba mtima kuti achite zimenezo, kuti atsutsane nazo izo.

²²⁹ Tsopano taonani. Ndi a Loti angati mu Amerika, dzulo, anawerenga Baibulo lawo, kuti akonzekere uthenga wawo wa tsikuli, ndipo anapezamo za ubatizo wa mmadzi mu Dzina la Yesu Khristu? Ndi angati a iwo amene anapezamo za ubatizo wa Mzimu Woyera? “Yesu Khristu yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse”? Marko 16, “Zizindikiro izi zidzawatsata iwo amene akhulupirira”? Yohane 14:12, “Iye amene akhulupirira pa Ine, ntchito zimene Ine ndikuchita iye adzazichita nayenso”? “Ngati inu mukhala mwa Ine, ndipo Mawu Anga mwa inu, pemphani chimene inu mukukhumba ndipo icho chidzachitidwa”? Ndi a Loti angati anawona Zimenezo? Koma, chifukwa cha kuwiringula kwawo, kwa chipembedzo chawo! Izo... Yang’anani ndipo muwone mu Baibulo.

²³⁰ Tayang’anani pa osonkhana awo a akazi odula tsitsi, ndipo iwo akudziwa kuti Baibulo limatsutsa zimenezo. Amawawona akamayenda mu msewu, mamembala awo omwe a mpingo akuyenda mu msewu, atavala zazifupi, ndipo amadziwa kuti Mawu amatsutsana ndi zimenezo. Koma iwo alibe kulimba mtima kuti atsutsane nazo izo. Koma, komabe, munthuyo nkumadzinenera kuti ndi Mkristu, solo yake mkati mwake imalira motsutsa izo, koma iye alibe kulimba mtima. Ngati izo si Sodomu wamakono, kodi izo ziri pati?

Mulungu, tipatseni ife winawake amene ati adzafuule motsutsa izo. Uko nukulondola. Monga Yohane M’batizi anati,

“Nkhwangwa yaikidwa ku muzu wa mtengo.” Ndizo zimene ife tikuzisowa lero.

²³¹ Penyani. Iwo ndi Sodomu wamakono. Kumbukirani. Mukuona? Dziko lonse lasanduka Sodomu ndi Gomorrah wamakono. Loti kenanso akukhala moyo. Ayi. . . Akukhalanso moyo, pakuti zikumbumtima zake zoonza zikumuuza iye mwa Mawu kuti iye akulakwitsa.

²³² Taonani mu Chicago, Chicago wamkulu, pamene alaliki firii handiredi amenewo atakhala pamenepo. Ndipo Ambuye anandiuza ine usiku umenewo zimene amati adzachite. Iwo anali ndi khwekhwe atanditcherera ine. Ine, ndikupitabe kumeneko. Ine ndinapita ndipo ndinakamuuza M’bale Carlson. Ine ndinati, “Inu simukachititsira iwo mu hotelo imeneyo. Inu muyenera kudzautengera iwo ku malo ena, ndipo icho chidzakhala chipinda cha girini. Ndipo iwo andiikira ine khwekhwe, kodi iwo sanatero, M’bale Carlson?” Iye anagwetsa mutu wake.

Iye anadzakhala uko mu ofesi yanga, masiku angapo apitawo, kuti ine ndibwere, msonkhano waku Chicago. Anati, “Ine sindidzaiwala konse zimenezozo M’bale Branham.”

Ndipo ine ndinati, “Iwo andiikira ine khwekhwe. Chifukwa chiyani, M’bale Carlson? Kodi inu mukuopa kundiuza ine chifukwa chake, inu ndi Tommy Hicks?” Iwo anagwetsa mitu yawo. Ine ndinati, “Tommy, bwanji iwe osapita ukayankhule?”

Anati, “Ine sindingakwanitse kuchita zimenezozo.”

Ine ndinati, “Ine ndimaganza iwe umati iwe undikomera ine mtima.”

²³³ Ine ndinati, “Usiku wathawu Ambuye anadzandiuza ine. Inu mukupita kumeneko lero, ndipo inu mukapeza kuti inu simukapeza chipinda chijachi. Inu mukapita ku chipinda china. Dokotala Mead adzakhala mbali *iyi*. Mwamuna wachikuda uja, mkazi wake, amene amaimba, adzakhala atakhala pomwe *apa*, ndi zina zoterozo, kumene onsewo adzakhale atakhala.” Ine ndinati, “Kukakhala wansembe wachi Buddha kumeneko.” Ndipo ine ndinati, “Tsopano fufuzani. Iwo akukanditsutsa ine chifukwa ine ndimalalikira ubatizo wa mmadzi mu Dzina la Ambuye wathu Yesu Khristu. Iwo akukanditsutsa ine chifukwa ine ndimalalikira mbewu ya serpenti; ndipo akukatsutsa umboni, kuti, munthu aliyense amene amayankhula ndi malirime ali nawo Mzimu Woyera, ndi zinthu.” Ine ndinati, “Mubwere kumeneko ndipo mudzamuwone Mulungu.”

²³⁴ Ndinafika kumeneko. . . Iwo anapita kumusi uko, ndipo maora awiri kumene kuyambira pamenepo, kapena mwabwinoko, nthawi ina masana amenewo, iwo anamuimbira M’bale Carlson. Ndipo iye anati, “Munthu amene anamuloleza iye kupeza icho, ndipo analipira theka pa icho, anati, ‘Ife tikuyenera kuimitsa, chifukwa amanenjala akuti anali

atachipereka kale kwa gulu loyimba usiku umenewo, kapena mmawa umenewo.” Ndipo iwo sanathe kuchipeza icho.

²³⁵ Chotero ife tinapita ku Town and Country. Ndipo mmawa umenewo pamene ife tinakafika kumeneko, ndipo anaimirira mmenemo, ndipo—ndipo M’bale Carlson anati, “Pali chinthu chimodzi. Abale inu mukhoza kusagwirizana ndi M’bale Branham, koma,” anati, “Iye samachita mantha kunena chimene iye amakhulupirira.” Iye anati, “Iye anandiuza ine kuti zinthu izi zikanadzachitika ndendende basi mmene izo ziliri.” Iye anati, “Tsopano ndi uyu apa. Ndimulole iye adziyankhulire yekha.”

²³⁶ Ine ndinangotenga Lemba, “Sindine wosamvera masomphenya ammwambamwamba,” monga ananenera Paulo. Ine ndinati, “Inu mwazibweretsa izo kwa ine, pa ubatizo wa mmadzi mu Dzina la Yesu Khristu. Abwino kuposa firii handiredi a inu mwadzisonyeza nokha kuti ndi Dokotala *Wakuti-ndi-wakuti*, ndi Dokotala *Wakuti-ndi-wakuti*.” Ine ndinati, “Ine ndiribe ngakhale maphunziro a sukulu ya galamara. Koma ine ndikumutsutsa mwamuna aliyense pano kuti mubweretse Baibulo lanu ndipo mudzaima apa pambali yanga, ndipo mudzakane amodzi a Mawu amene anenedwa.”

Inu muli nazo izo pa tepi kunja kuno, ngati inu mukufuna kudzamvera izo. Limenero linali gulu la chete kwambiri limene inu munalimvapo. Ine ndinati, “Vuto ndi chiyani?” Kodi alipo aliyense pano, usikuuno, amene anakhalapo mu msonkhano wa mmawa uja? Tiyeni tiwone inu mukweze dzanja lanu. Eya. Chabwino, ndithudi, yang’ananiponseponse.

Ine ndinati, “Ndiye, ngati inu simungaziimire kumbuyo zimenezo, ndiye chokani kumbuyo kwanga.” Kulondola. Amafuula kwambiri, pamene iwo ali pa kona. Koma akabwera maso ndi maso ndi nkhaniyo, izo zimakhala zosiyana. Uko nkulondola. Ndizo . . . Amuna amenewo anatuluka panja.

²³⁷ Tommy Hicks anati, “Ine ndikufuna firii handiredi a matepi amenewo, kuti nditumize kwa wolalikira Wautatu wonyengezera aliyense amene ine ndikumudziwa.”

Amuna amenewo akugwira chanza dzanja langa, anati, “Ife tibwera ku kachisi ndi kudzabatizidwa.”

Kodi iwo ali kuti? Zowiringula. “Ine sindingachite zimenezo. Chipembedzo changa sichingandilole ine kuti ndichite izo. Ine ndakwatira mkazi. Ine ndagula ng’ombe ya goli, kapena goli la ng’ombe, kani. Ine—ine ndagula malo. Ine ndikuyenera kupita kukawawona iwo.” Mukuona? Zina za zinthu zimenezo, zoterozo, zowiringula. Kodi nkulondola uko? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Kodi moyo umenewo ndi woyenera Uthenga? [“Ayi.”]

Ngati Uthenga uli woona, tiyeni tigulitse chirichonse chimene ife tiri nacho ndipo tikhalire moyo Iwo. Tikhale

Mkhristu. Inde, bwana. Ameni. Zindikirani tsopano, pamene ife tikutseka.

²³⁸ Koma zowiringula zawo ndizo tizikhulupiro tawo ndi zipembedzo zawo.

Izo ziri ngati mtengo. Ine ndinali kuyang’ana pa M’bale Banks tsiku lina. Ine ndinali ndi—ndi mtengo wa paini, ine ndinaudzala pamene ine ndinasamukira uko koyamba, pafupifupi, oh, pafupifupi zaka fifitini zapitazo, kapena kuposa. Ndipo ine ndimazisiya nthambi zimenezo, nthambi zimakula pa mtengo wa painiwo, ndipo ife timalephera kudutsitsanso chotchetchera pansi pamenepo. Ndipo panalibepo katsamba ka udzu pamenepo, mulimonse. Ndipo ine ndinapita kumeneko ndipo ndinatenga macheka ndipo ndinakadula nthambi zimenezo, mpaka mtengo wa painiwo unali mmwamba *apa*, kufika pakuti iwe umatha kumayenda pansi pake ndi chotchetchera. Ndipo udzu wowoneka bwino kwambiri umene inu munayamba mwawuwonapo uli pansi pake tsopano. Izo zinali chiyani? Mbewu inali pamenepo. Iyo imayenera kuti ilandire kuwala.

²³⁹ Ndipo bola ngati chipembedzo, zowiringula zanu, zikuyesera kuti ziyike mthunzi pa Mbewu iyo imene inu mukudziwa kuti ndithudi ili pamenepo, inu mukutenga gawo la Loti. Zitaireni kutali zinthu zimenezo, ndipo mulole Kuwala kwa Uthenga kuwalire pamenepo, mphamvu ya Yesu Khristu. Inde. Kuchotsapo Kuwala pa iyo, zimapangitsa kuti iyo isakhale moyo. Pakuti, ngati Kuwala kudzafike pa iyo, iyo idzaphukira ku Moyo.

Ndi chifukwa chake anthu amati, “Musapite ku msonkhano wa mtundu umenewo.” Iwo amawopa kuti Kuwala kwina kukawombera pa mmodzi wa mamembala amenewo.

²⁴⁰ Kumbukirani mkazi wa pa chitsime. Iye anali hule.

Kumeneko kunali ansembe amenewo. Iwo anamuwona Yesu akumuza Nataniele, “Ine ndinakuwona iwe, pamene iwe unali pansi pa mtengo wa mkuyu.”

Ndipo ansembe anati, “Iye ndi Bezezebule. Iye ndi wambwebwe. Ameneyo ndi mdierekezi.”

²⁴¹ Mkazi wamng’ono uyu, pamene iye anayendera cha kumeneko, mu chikhalidwe chake chovunda, akukhala ndi amuna sikisi. Ndipo pamene iye anayendera cha kumeneko mu chikhalidwe chimenecho, mu chikhalidwe icho chimene iye anali. Ndipo Yesu anati, “Ndibweretsere Ine akumwa.” Kuyankhulanako kunayambika. Iye anati, “Pita ukamutenge mwamuna wako ndipo ubwere kuno.”

Iye anati, “Ine ndiribe aliyense.”

Anati, “Iwe wanena zoon. Iwe uli nawo asanu, ndipo uyo amene iwe ukukhala naye, si mwamuna wako.”

Iye anati, “Ine ndazindikira kuti Inu ndi mneneri, Bwana. Ine ndikudziwa Mesiya adzachita zimenezo pamene Iye adzabwera.”

Yesu anati, “Ine ndine Iye.”

²⁴² Izo zinakhazikitsa izo. Pamene Kuwala kumeneko kunadzawalira kudutsa Mbewu imeneyo itakhala mwa hule wamng’ono wokalambayo, masiku a uhule anatha. Anapita mu msewu, akulemekeza Mulungu, anati, “Bwerani, mudzamuwone Munthu Amene wandiuza ine zinthu zimene ine ndachita. Kodi Uyu si Mesiyo?” Icho chinali chiyani? Kuwalako kunadzafika kwa mbewu imeneyo pansi pa mthunzi wa chotchinga cha uchiwerewere. Inde, bwana.

Tsopano tiyeni titseke, ponena izi. Ine sindikudziwa kuti ndatsala ndi masamba angati, koma ine—ine ndikutsimikiza sinditenga onsewo. Pafupifupi teni, koma iwo ndi pafupifupi theka limodzi amene ndamaliza. Koma tiyeni titseke, ponena izi.

²⁴³ Tiyeni tifanizitse chinachake, nthawi ina, cha moyo woyenera. Tiyeni tifanizitse moyo wa Paulo Woyera kwa mnyamata mwini chuma. Kuwala komweko kunawamenya amuna awiri onsewo. Awiri onsewo anali ndi kuitanidwa komweko kuchokera kwa Yesu Khristu. Nkulondola uko? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Awiri onsewo anali ophunzitsidwa bwino mu Malemba. Iwo onse anali ophunzira mawu. Membala, Yesu anamuza—anamuuza mnyamata mwini chuma, “Sunga malamulo.”

²⁴⁴ Anati, “Ine ndazichita izi, kuyambira unyamata wanga.”

Iye anali mwamuna wophunzitsidwa. Chomwechonso Paulo Woyera. Awiri onsewo anali ophunzitsidwa bwino mu Lemba. Koma, awiri onsewo anali ndi Mawu. Mmodzi anali nawo Iwo kuchokera ku chidziwitso; winayo anali ndi mbewu ya Moyo mwa iye. Pamene Kuwala kuja kunadzawala modutsa, patsogolo pa Paulo, iye anati, “Ambuye, Ndinu Ndani?”

Anati, “Ndine Yesu.”

“Ndine pano, ndiye.” Iye anali wokonzeka.

²⁴⁵ Kuwalako kunadzawakhudza amuna awiri onsewo. Mmodzi anaphukira; winayo sanatero. Umo ndi mmene izo zikukhalira lero: mpingo wauzimu, mpingo wathupi.

²⁴⁶ Mnyamata mwini chuma anali ndi chowiringula chake. Iye sakanatha kuchita zimenezo. Iye anali wolemetsedwa kwambiri ndi abwenzi ambiri a mdziko. Iye sankafuna kusiya kuyanjana nawo.

Ndiro limene liri vuto ndi anthu ambiri lero. Inu mumaganiza, chifukwa inu ndi wa loji, inu simungasiye basi ubale umenewo. “Iwo onse amamwa ndi zinthu monga zimenezo ndipo iwo amachita *izi*.” Chabwino, pitirirani nazo izo; sindikutsutsana ndi loji, sindikutsutsana ndi mpingo. Ine

ndikukamba za inu. Mukuona? Eya. Mukuona? Sindikutsutsana ndi zimenezo. Pakuti, sikisi ya chimodzi, ndi theka la dazeni la chinacho. Ine ndangotsiriza kumene kukuuzani inu kuti mpingo si china koma loji, chipembedzo, ngati iwo angakane Mawu a Mulungu.

²⁴⁷ Zindikirani. Mnyamata mwini chuma anali ndi zowiringula zake. Iye sanasiye umboni wake, ngakhalebe. Ife tikupeza kuti iye anapita ku malonda aakulu. Iye anali ndi chidziwitso. Ndipo iye anapita ku malo oterowo mpaka iye anachulukitsa zochuluka chomwechi, mpaka iye anamanga nkhekwe zatsopano kuti ayikemo zinthu zake. Ndipo pamene iye anafa; ndipo wa batchala wina, ndi kolala yake ataitembenuza, analalikira maliro ake, sindikukaikira. Ndipo pamene iye anatero, iye mwinamwake ananena kuti... Iwo anatsitsa mwatheka mbendera, ndipo anati, “M’bale wathu wokonedwa, meya wa mzinda uno, tsopano ali mmanja a Wamphamvuzonse, chifukwa iye anali membala wamkulu wa mpingo. Iye anachita *zakuti-ndi-zakuti*, ndi *zakuti*.”

Ndipo Baibulo linati, “Mu gehena iye anakwezera mmwamba maso ake, pokhala anali mmazunzo.” Mukuona?

²⁴⁸ Ndipo kumbukirani, iye ankafunabe kuti agwiritsitse chodzinenera chake ku gehena. Iye anamuwona Lazaro, ali pa zifuwa za Abrahamu, ndipo iye anati, “Atate Abrahamu, mtumizeni Lazaro kuno.” Akumutchulabe iye “atate.” Mukuona?

Iye anatenga chidziwitso chake, ndipo anapita ku mpingo wa luntha. Pamene Kuwala kunadzamukhudza iye, iye anakukana Iko.

Ngati ako si kachitidwe kamakono ka mpingo lero, ine sindikudziwa izo. Ziribe kanthu kuti Mulungu awalitsira chiyani kudutsa pa njira yawo, Lawi la Moto kapena chirichonse chimene icho chingakhale; iwo apobe, ndi chidziwitso chawo, iwo akhoza kuzifotokoza Izo mophotchola, ndi kupita kwa gulu la aluntha, chifukwa cha maimidwe a pagulu.

²⁴⁹ Koma Paulo anali kale mu kuima kwa pagulu, ndi chidziwitso chapamwamba, wophunzira wamkulu pansu pa Gamaliele, wapafupi kwa wanseme wamkulu, mpaka mwakuti iye anapita kwa ansembe ndipo anakatenga chilolezo kuti akawaike oyera odzigudubuzwa onse mu ndende. Koma pamene Kuwala uko kunadzakhudza njira yake, ndipo iye nkuwona kuti Lawi la Moto lomwe lija limene linatsogolera Israeli kudutsa chipululu anali Yesu Khristu, iye anasiya zonse zimene iye ankazidziwa. Iye anabwera ku Moyo.

²⁵⁰ Inu mungautche moyo wa mwamuna wachuma uja moyo woyenera Uthenga umene iye anaumva? Ngakhale iye anali wokhulupirira, kodi inu mungautche mtundu wa moyo umenewo... Pakati pa aluntha ndi zikondwerero, usiku uja uko

pa . . . pamene dzuwa limalowa, akupereka msangulutso, ndipo mwinauwake wansembe wina akunena pemphero, pamwamba kumeneko. Ndipo iye anali akusangalala, ndipo wopempha atagona pa chipata chake kumusi uko. Ndipo iye anapereka msangulutso wake, ndipo anayankhula za chikhulupiriro chake chachikulu chimene iye anali nacho mwa Mulungu. Ndipo kusanache, mmawa wotsatira, dzuwa lisanatuluke, iye anali mu gehena. Uko nkulondola. Ndi amenewo aluntha anu.

²⁵¹ Koma Paulo, pamene Kuwala kunadzamukhudza iye, tiyeni tifanizitse moyo wake ndipo tiwone ngati iwo uli woyenera. Chinachitika ndi chiyani? Pamene, Paulo, Kuwala kunadzamukhudza iye, iye anasiya nzeru zake zonse ndipo anachoka kwa gulu la aluntha lija, ndipo iye anayenda mu Mzimu wa Yesu Khristu. Ulemelero kwa Mulungu! Wanzeru monga mmene iye analiri, iye sanagwiritse ntchito nkomwe mawu aakulu.

Pamene iye anadzabwera pakati pa Akorinto awo, iye anati, “Ine sindinabwere kwa inu ndi nzeru za munthu. Ine sindinabwere kwa inu ndi mawu aakulu, chifukwa inu muika chikhulupiriro chanu mu zimenezo. Koma ine ndabwera kwa inu mophweka, mu mphamvu ya chiukitsiro cha Yesu Khristu, kuti chikhulupiriro chanu chikakhale mmenemo.” Ndi umenewo moyo. Penyani izo.

²⁵² Iye sanagwiritse ntchito nkomwe maphunziro ake. Iye sanayende nkomwe ndi gulu la aluntha. Iye anayenda mu Mzimu wa Khristu, wodzichepetsa, womvera ku Mawu a Mulungu, pamene Iwo anali otsutsana kwambiri ndi tizikhulupiriro tawo. Koma Paulo anawona Kuwala ndipo anayenda mu Iko (nkulondola uko?), kulola Moyo wa Khristu unyedzimiritse Yesu Khristu kwa m’badwo umene iye amakhalamo, kuti anthu akhoze kuwona Mzimu wa Mulungu mwa iye.

Ndipo odzichepetsa anakhulupirira izo, mochuluka kwambiri, mpaka kuti iwo ankafuna kubweretsa mipango. Iwo amaichotsa iyo kuchokera pa thupi lake. Ndipo iwo amakhulupirira izo, mochuluka kwambiri, iye ndi choimira chotero cha Yesu Khristu, mpaka, chirichonse chimene iye amachigwira, iwo amakhulupirira, chinali chitadalitsidwa. Inde. Ndi munthu wotani amene iye anali, anapereka moyo wake, chuma chake, chirichonse chimene iye anali nacho! Maphunziro ake; anaiwala zonsezo, kuti azikayenda pansu ndi asodzi, ndi opempha ndi opanda kokhala mu msewu, kuti akalole kuwala kwake kukawonetsere chikondi cha Yesu Khristu.

Iye anati, “Ine ndakwapulidwa ku nsana, ka forte ndi naini; sizikundisautsa ine.” Ananena chomwecho, “Ine ndikunyamula mthupi mwanga zipysera za Yesu Khristu.” Munthu wamng’ono wosauka ali mu chikhaliidwe choipa choterocho, iye anati, “Ine ndikunyamula mthupi mwanga zipysera za Yesu Khristu.”

Zinali zosiyana bwanji ndi munthu wa ulemu wamkulu uyu ndi ansembe onse atamuzungulira iye.

²⁵³ Ndipo pamene iye anali ku Romu, ndipo wopanda aliyense woti nkuima ndi iye. Ndipo iwo anali kumanga chinsanja, kuti akamudulirepo mutu wake, kunja uko. Kumeneko ndi kumene iye anakanena izo. Oh, mai! Iye anati, “Uko kwaikidwa korona wa ine, amene Ambuye, Woweruza wolungama adzandipatsa ine pa Tsiku limenero; ndipo osati ine ndekha, koma tsopano iwo onse amene amakonda kuwonekera Kwake.” Ndi umenewo moyo woyenera Uthenga, mwana wamwamuna weniweni.

²⁵⁴ Iye anali kumuimirira Khristu. Iye anawulola Uthenga kuti unyezimire kudutsa mwa iye. Iye asanatero, iye anapita ndipo anakaphunzira Uthenga. Anapita uko mu Arabia ndipo anakakhalako zaka zitatu, ndipo anatenga Chipangano Chakale. Ndipo anawonetsera, mwa Chipangano Chakale, kuti Iye anali Yesu Khristu. Ndipo iye analola kuti Iwo unyezimire kudzera mwa iye, kwa gulu lodzichepetsa la anthu. Kuti, iye, pamene . . . Iye anati, “Ine ndikudziwa kukhala wokhata, ndipo ine ndikudziwa kukhala ndi njala ndi kukhala wosowa.”

Mwamuna wamaphunziro monga iyeyo, ndiponso wophunzira monga iyeyo, ataima kwa . . . ndi maphunziro kuchokera kwa Gamaliele, mmodzi wa aphunzitsi aakulu amene analipo a tsikulo, ndipo anaima dzanja ndi dzanja ndi wansembe wamkulu. M’bale, mtengo wake ukanakhoza kukhala madola mamillioni ndipo anali ndi mitundu yonse ya manyumba. Uko nkulondola. Koma iye anati, “Ine . . .”

²⁵⁵ Iye analibe konse koma chikhothi chimodzi. Ndipo Demas anamuwona munthu wa utumiki wonga umenewo! Timoteo Wachiwiri, mutu wa 3, iye anati, “Demas wandisiya ine, ndi amuna ena onse, akonda dziko latsopano ili.” Anati, “Pamene inu mukubwera, mundibweretsere ine chikhothi chija chimene ine ndinachisiya kumeneko. Kwayamba kuzizira.” Mwamuna wa utumiki ngati umenewo, ndipo nkungokhala ndi chikhothi chimodzi chokha? Ulemelero kwa Mulungu!

²⁵⁶ Zikundikumbutsa ine za Martin Woyera, pamene iye ankayesetsa kuti aime ndi Uthenga, ndi chirichonse, iye asanatembenuke. Mu—mu Pre-Nicene, kapena Nicaea council, *Nicaea Fathers*, mu mbiriyakale. Tsiku lina, iye anali kudutsa zipata kumeneko. Iye amachokera ku Tours, France. Ndipo kumeneko kunali anthu . . . Wopempha wokalamba atagona kumeneko, akufa, analibe zovala. Ndipo anthu ankamudutsa, amene akanatha kumupatsa iye zovala, ndipo iwo samachita zimenezo. Iwo amamudutsa iye ndipo samamulabadira mwamuna wokalambayo. Ndipo Martin Woyera anaima pamene ndipo anamuyang’ana iye. Iwo anati iye . . .

²⁵⁷ Msilikali aliyense amakhala ndi—amakhala ndi munthu wopukuta jombo zake. Ndipo iye anapukuta jombo za wantchito wake.

Ndipo anavula chikhothi chake, ndipo anatenga mpeni ndipo anachidula icho, theka, pakati, lupanga lake. Anamufunditsa wopempha wokalambayo mu chimenecho, anati, “Ife awiri tonse tikhoza kukhala moyo.”

Iye anapita kwawo ndipo anakagona. Atagona pamenepo, akuganizira kuti mwamuna wokalamba uja amalira. Molunjika, Chinachake chinamudzutsa iye. Iye anayang’ana. Ataima mchipinda, apo panadzaima Yesu Khristu atafundira chidutswa cha chovala chomwe chija chimene iye anamufunditsa wopemphayo. Anati, “Monga mmene iwe wachitira kwa ochepa aang’ono awa, iwe wachitira izo kwa Ine.” Umenewo ndiye moyo woyenera Uthenga. Inu mukudziwa mmene iye anasindikizira moyo wake, nayenso, sichoncho inu?

²⁵⁸ Tamuwonani Polycarp, akuima ndi ubatizo wa Dzina la Yesu, motsutsana ndi mpingo wa Roma Katolika. Ndipo iwo anamuwotcha iye pa nkuni; anagwetsera pansi bafa ndipo anamuwotchapo iye. Tamuwonani Irenaeus, ena onse a iwo, amene anazunikira izi. Ndiyo miyoyo yoyenera.

²⁵⁹ Taonani zimene Paulo ananena mu Bukhu la Ahebri, mutu wa 11. Anati, “Iwo anadulidwa pakati, anakhadzulidwa pakati; ankakhala akuyendayenda, atavala zikopa za nkhusa ndi zikopa za mbuzi, ndipo amakhala mu chipululu, ndipo opanda pokhala ndi zina zotero; miyoyo imene dziko lino siliri lowayenera.” Ndi zimenezotu. Moyo umenewo ndi woyenera Uthenga. Kodi wanga ndi wanu udzaima bwanji pa Tsiku la Chiweruzo, ndi amuna ngati amenewo?

²⁶⁰ Tayang’anani pa Paulo tsopano. Ife titsikira mmusi. Iye anauimirira Uthenga, anamulola Yesu kuti ayenderere kudutsa mwa iye. Zinalibe kanthu kaya ndi motani, chiyani, mosalabadira chimene wina aliyense ankaganizira za izo. Kutu, wansembe wamkulu, bwanji, iye anapita ndipo anakadulidwa mutu wake, chifukwa cha Iwo. Iye anali woimira woyenera wa Uthenga. Kulolera...Tayang’anani pamenepo. Mosalabadira zimene anthu ankaganiza, kulolera mphamvu ya Moyo Wamuyaya kuti iyenderere kudutsa mwa iye, mpaka kuti iye anati, “Ine ndingakhale wotembereredwa kwa Khristu, chifukwa cha abale anga.”

Tsopano inu mukudziwa chimene inu mumachita pamene inu mwalandira Moyo Wamuyaya? Ndi limenero funso lanu. Ndi limenero yankho lanu. Inu mumatenga mbali ya luntha; kapena, mumatenga mbali *Iyi*, ngati inu mwaupeza kwenikweni Moyo Wamuyaya. Izo ndi zimene zimachitika.

261 Izo ndi zimene zinachitika. Paulo, anakonzeka kuti atembereredwe ndi Khristu, anawalola anthu ake. . . Akhungu, anthu osaphunzira amene sakanamvetsera ku Uthenga wake!

Ine ndikuganiza, manyazi pa ine mwini. Ine ndinali wokonzeka kuti ndiwasiye iwo, chifukwa iwo samamvetsera kwa ine. Ine ndikumverera ngati ndilape. Ndipo ine ndalapa. Mukuona?

262 Zindikirani. Mosalabadira zimene ena amaganiza, moyo wa mtundu uwu ndi woyenera Uthenga.

Tsopano ine ndikutseka.

263 Mnyamata wachuma, monga ambiri a ife lero, anadzitsekera ndipo anawakana Mawu a Moyo, ndipo anadzakhala membala wa mpingo; ndipo anawonetsera moyo, umene umatsimikizira mu Baibulo, kuti unali wosayenera Uthenga umene iye anafunsidwa kuti awulandire. Nkulondola uko? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Uthenga ukanawala bwanji podutsira mu kuwala kwa mdima ngati kumeneko, kumakana mphamvu ya Mulungu?

264 Tsopano, njira yokhayo yokhalira moyo woyenera, ndi pomulola Khristu ndi Mawu Ake (chimene, Iye ndi Mawu) azidzinyezimiritsa Okha mwangwiro kwambiri mwa iwe mpaka Mulungu atatsimikizira zimene Iye ananena mu Mawu. Pakuti, Khristu anafa kuti Iye adzathe kudzipereka Yekha pamaso pa Mulungu, Nsembe. Ndipo Iyo inadzabwereranso mmawonekedwe a Mzimu Woyera, kuti adzadzinyezimiritse Iyemwini kudzera mwa anthu Ake, kuti adzapitirize ntchito Yake; kudzinyezimiritsa Yekha kudzera mwa Inu, kuti adzakwaniritse Mawu Ake olonjzedwa mmasiku a mtsogolo ano.

Monga Yohane M’batizi anamvera, pamene iye anamva kuti Khristu wabwera. Ndipo Khristu anayenda kukalowa mmadzi. Ndipo Yohane anati, “Taonani Mwanawankhosa wa Mulungu.”

Palibe wina amene anakuwona Iko. Koma iye anakuwona Iko, Kuwala kuja kukutsika kuchokera Kumwamba, monga nkunda. Ndipo Liwu likuti, “Uyu ndi Mwana Wanga wokonedwa mwa Iye Ine ndikondwera kukhalamo.” Iye anakuwona Iko kukubwera.

Ndipo Yesu anayenda kukalowa mmadzi, Immanueli, pamaso pa—pa mlaliki amene amayenera kukhala wokakamula. Anayenda kukalowa mmadzi, pamaso pa anthu, ndipo anati, “Ine ndikufuna kuti ndibatizidwe ndi iwe.”

265 Yohane anati, “Ambuye, ine ndiwosowa kuti ndibatizidwe ndi Inu. Chifukwa chiyani Inu mukubwera kwa ine?” Maso awiri onsewo anakumana pamodzi, mneneri ndi Mulungu wake. Ameni. Mukanakhoza inu. . . ine. . . Kodi ine sindingakonde kuima ndi kumawonerera zimenezo? Kuwawona maso

okhazikika, olowa mkati awo a Yohane akukungunukira mmusi ndi kudzakawapeza maso okhazikika, olowa mkati awo a Yesu; asuwani achiwiri kwa wina ndi mzake, mu thupi.

266 Yesu anati, “Yohane, balola kuti izo zikhale chomwecho tsopano, pakuti chikutikakamiza ife. Ndife Uthenga wa ora lino. Izo zikutikakamiza ife kuti tikwaniritse chirungamo chonse.”

267 Yohane anaganiza, “Inde, Iye ndi Nsembe. Nsembe imayenera kutsukidwa Iyo isanaperekedwe.” Kenako iye anati, “Bwerani.” Ndipo anamubatiza Iye. Amen. Mawu ena, “Izo zikutikakamiza ife kuti tikwaniritse chirungamo chonse.”

Yesu, podziwa kuti mwamuna ameneyo anali weniweni, anati, “Sipanakhalepo mwamuna wobadwa mwa mkazi, wonga iye. Iye ndi woposa mneneri; inu mukhoza kulandira izo, uyu ndi woposa mneneri.” Ndipo Yesu, atayang’ana mu mtima wake, ndipo anadziwa izo. Msuwani Wake yemwe anakumana naye Iye kumeneko, maso ndi maso.

268 Yohane anati, “Ambuye, ine ndiwosowa kuti ndibatizidwe ndi Inu. Ndipo nchifukwa chiyani Inu mukubwera kwa ine?”

269 Anati, “Balola izo kuti zikhale chomwecho, Yohane. Koma, kumbukira, izo zikutikakamiza ife kuti tikwaniritse zonse zimene Mulungu analonjeza. Ndipo Ine ndi Nsembe. Ine ndikuyenera kuti nditsukidwe ndisanakaperekedwe.” Oh, mai! Mai!

270 Ndipo, lero, pamene Kuwala kwamadzulo kukuwala, pamene palibepo munthu woganiza bwino koma amene angati (wophunzira Baibulo aliyense, akayang’ana mu Baibulo, amadziwa) ili ndi tsiku lotsiriza. Ndiye, izo zikutikakamiza ife kuti tigwe kuchokera ku makoma aakulu awa, kapena kuti tichoke ku zinthu izi, ndipo tikalowe mu zirungamo za Yesu Khristu mu tsiku lotsiriza lino, ndi kukatenga Chisindikizo cha Mulungu mdierekezi asanatipatse ife chiremba cha chirombo. Oh, mai. Inde.

271 Kumupempha Mulungu kuti aloleze Kuwala kwa tsiku lino kuwuke mwa inu, kuti mukhale wantchito womvera kwa Mulungu. Ndiyeno nkulola chipatso cha Mzimu chikhalebe mmoyo mwanu kwanthawizonse. Ndipo umenewo ndi moyo woyenera Uthenga.

272 Mundirole ine ndinene izi, potseka. Njira yokhayo, njira yokhayo imene inu mungakhalire moyo woyenera Uthenga, ndi kuwulola Uthengawo Pawokha, gawo lililonse la Uthenga, libwere mwa inu ndipo lidzanyezimiritse malonjezo Ake, kuwapanga iwo atsimikiziridwe. Kumulola Mulungu akhale moyo mwa inu, kuti adzatsimikizire malonjezo a tsiku lino.

Chimodzimodzi monga Yohane, monga Yesu ananena kwa Yohane, “Balola izo zikhale chomwecho, Yohane. Uko

nkulondola. Koma ife ndi amthenga a tsiku lino, ndipo ife tikuyenera kukwaniritisa chirungamo chonse.”

Ndipo ngati ife tiri Akhristu a tsiku lino, tiyeni timulandire Yesu Khristu mu mtima mwathu. Ndipo Iye ndi Mawu. Musakane aliwonse a Iwo. Muziti, “Iwo ndi Choonadi.” Ndipo muwakhazike Iwo mu mtima mwanu, muwone chipatso cha Mzimu pa inu, ndipo mukwaniritse lonjezo lirilonse limene Iye anapanga mu Baibulo. Mulungu akufuna kuti akwaniritse Mawu Ake, ndipo Iye alibe manja aliwonse koma anga ndi anu. Iye alibe maso aliwonse koma anga ndi anu. Iye alibe lirime koma langa ndi lanu. “Ine ndi Mpesa. Inu ndi nthambi.” Nthambi zimabala chipatso. Mpesa umapereka mphamvu kwa nthambi. Umenewo ndiwo moyo umene uli woyenera.

²⁷³ Pemphero langa ndi lakuti, kwa iwo amene ali pa waillesi kapena mu...ku dziko la tepi, ndi iwo amene ali pompano. Mulole Mulungu wa chisomo chonse, wa Kumwamba, awalitsire Mzimu Woyera Wake wodala pa ife tonse, kuti ife, kuyambira usiku uno, mpakana, tikakhoze kukhala moyo umene Mulungu akhoza kunena kuti, “Ndine wokondwera kwambiri. Lowani mu zimwemwe Zamuyaya zimene zinakonzedwera inu chikhazikitsireni maziko a dziko lapansi.” Mulole Mulungu wa Kumwamba atumize madalitso Ake pa anthu nonse inu.

²⁷⁴ Ine ndikupemphera kuti Mulungu akudalitseni akazi inu, usikuuno, amene muli ndi tsitsi lalifupi, mwa njira yakuti inu muwone, ndipo muchokeko ku kachitidwe kamakono kano ka tsikuli, ndipo muzindikire kuti Baibulo limanena kuti inu musachite zimenezo. Ndipo ngati inu mukutsutsika povala zovala zosayenera, kuti Mulungu wa Kumwamba atsanulire chisomo Chake mu mtima mwanu, kuti inu musadzachite konse izo kenanso, kuti inu musadzakhale wolakwa kwa chinthu choterocho kenanso. Mulole Mzimu Woyera ungotsegulira izo kwa inu ndi kukuwonetsani inu. Zikhale kuti, amene alibe ubatizo wa Mzimu Woyera...

²⁷⁵ Zikhale kuti amuna inu amene muli ndi akazi anu, ndipo mmawalola iwo kukhala bwana wa mnyumba ndi kumakutogolerani inu, Mulungu wa Kumwamba akupatseni inu chisomo kuti mupondetse phazi lanu pansu ndi kumubwezeretsa mkazi ameneyo ku malingaliro ake olondola kenanso, eya, ndipo nazindikire kuti amenewo ndi malo anu mwa Khristu. Osati bwana, tsopano, koma inu ndi mutu wa nyumbayo. Kumbukirani, iye sali nkomwe mu chirengedwe chapachiyambi. Iye wangokhala wotuluka mwa inu, anaperekedwa ndi Mulungu, kwa inu, kuti azikusamalirani inu, kuti azichapa zovala zanu ndi kukuphikirani zakudya, ndi zina zotero. Iye si wokulamulirani mwankhanza wanu.

²⁷⁶ Inu akazi Achimerika mumayendayenda muli ndi mulu wa penti pa nkhope zanu, ndi mphuno yanu mmwamba

mumlengalenga, ngati itati yavumba, iyo ingakumizeni inu, ndiyeno nkumaganiza kuti ndinu ngati wolamulira mwankhanza. Inu mukhoza kukhala chimenecho, kwa wachikazi, koma osati kwa mwana wamwamuna weniweni wa Mulungu. Kulondola.

²⁷⁷ Mulungu akupatseni amuna inu chisomo, ngati ana aamuna a Mulungu, kuti musiye zam'kutu monga zimenezo. Uko nkulondola. Iye akupatseni inu chisomo, kuti mukataire ndudu zimenezo pansi, mukasiye kumvetsera nthabwala zauve izo, zam'kutu zonse izo. Tiyeni tikhale ana aamuna a Mulungu, kuti tikakhoze kuyenda moyo woyenera Uthenga.

Ndipo winawake akamayenda mu msewu, aziti, “Ngati panayamba pakhalapo Mkhristu, ndi ameneyo apo. Ndi ameneyo apo amene Mulungu wangodziwonetserapo Yekha, ndipo mwamuna ameneyo ndi Mkhristu weniweni, ngati panakhalapo Mkhristu. Inu mukhoza kuganiza kuti iye akuwoneka wachikale. Iye ndi dona weniweni.” Ndi zimenezo apo.

²⁷⁸ Mukakhale Mkhristu wambiri yabwino, pakuti ndife alendo kuno. Kuno si Kwathu. Kwathu ndi Kumwamba. Ife ndi ana aamuna ndi aakazi a Mfumu, a Mfumu. Tiyeni ife ti-... tilole miyoyo yathu ikhale mo—moyo wambiri yabwino. Tiyeni ife ti-...pakhale moyo umene uti udzalemekeze chinthu icho chimene ife timadzinenera kuti tiri: Mkhristu. Ndipo ngati inu simungakhale moyo wa mtundu umenewo, ndiye musiye kumatchedwa Mkhristu, chifukwa inu mukungobweretsa chitonzo pa Ntchitoyo.

²⁷⁹ Zikomo, anthu inu, usiku wotentha uno, mwakhala pano. Ine ndikudalira kuti sipadzakhala mmodzi wa inu adzataike, pa Tsiku limenero. Ine—ine—ine ndikudalira kuti inu ndi ine, pamodzi, tidzakapeza chisomo pamaso pa Mulungu, kuti ine ndidzakhala wothequera nthawizonse kudzaima ndi chimene chiri Choonadi, osadzakupwetekani inu konse, koma osadzabweza konse nkhonya pa inu. Mukuona? Ngati ine ndingatero, ine sindingakhale bambo woyenera, ngati ine nditangomamulola mwana wanga kuti azichita chirichonse. Ine ndingawakonze iwo. Chikondi chirichonse chingachite zimenezo. Chikondi chimakonza. Ine ndikukumbukira inu mukundilemba ine cholemba chija, tsiku lija, Pat. Ine ndikadali nachobe icho. Ndipo chikondi chimakonza. Baibulo linanena chomwecho. Ndipo ngati ziri zosalondola, ndi chifukwa chake Mulungu amatikonza ife. Iye amatikonda ife.

²⁸⁰ Tiyeni ife tikhale moyo, kuyambira pano mpakana, umene uli woyenera, wokhala ndi kukoma ndi kuleza. Musamakhale nazo chidwi, ndi zakuti, “Chabwino, Mulungu adalitsike, ine ndikudziwa iye waupeza Iwo. Iye anayankhula mmalirime. Iye anavina mu Mzimu.” Zimenezo ndi zabwino. Koma ngati iye alibe chipatso cha Mzimu, Mzimu siuli mmenemo.

Iye akungosanzira kutengeka kwa mtundu wina, kapena chinachake, chifukwa Mzimu Woyera ukhoza kokha kukhala moyo wa chipatso cha Mzimu. Ndiyo njira yokhayo imene Iye angachitire.

²⁸¹ Mulungu akudalitseni inu. Tiyeni tiweramitse mitu yathu, mphindi chabe.

Mulole...Mulungu, amene wapereka Kuwala Kwake mu tsiku lotsiriza lino, Kumene kuli apa patsogolo panga, kwa Baibulo Lake; ndi chithunzi cha Angelo awa, Kuwala kwachinsinsi uku mu maonekedwe a piramidi, kumene ngakhale asayansi sakudziwa mmene Iko kunafikira apa. Iwo sangathe kuzifotozoza Izo. Koma, Atate, ndife othokoza. Inu munatiuza ife, miyezi izo zisanachitike, ndipo ndife oyamikira kwa Inu.

²⁸² Mulole anthu, amene akutchedwa ndi Dzina Lanu, achoke ku tchimo, usikuuno, Ambuye, kusakhulupirira. Mulole, monga... Ine ndimayenera kuyankhula molimba chomwecho motsutsa alongo athu, osati chifukwa ine sindimawakonda iwo, Ambuye, koma ine sindikufuna kudzamuwona Mdierekezi akuwavyunyuza iwo mpaka kugwa ndikufa, limodzi la masiku awa, ndipo kenako nkudzayesera kudzakumana ndi Inu mu chikhalidwe cha mtundu umenewo, titatha kumvetsera Choonadi cha Mulungu, ngati ichi. Mulole iwo amverere kuti izo ndi za iwowo, kuti apite ndi kukafufuza Malemba, ndi kukawona ngati izo ziri zolondola. Kukagwada pansu pamaondo awo pamenepo, moonamtima, ndikuti, “Mulungu, kodi chimenecho ndi Choonadi?” Ndiye izo zidzakhala zonse zimene ziri zoyenera, Ambuye, ngati iwo ati adzakhale owonamtima za izo, pakuti Mawu Anu ali Choonadi.

²⁸³ Anthu akhala. Ambiri a iwo, mwinamwake, anali ndi zinthu zimene zimawapweteka iwo. Koma Mzimu wa Mulungu wayankhula ndi iwo, ndipo iwo anakhala bata ndipo amamvetsera. Ora likupita kumapeto. Ora latha pano ndi usiku, ndipo nthawi yathanso mu nthawi imene ife tikukhalamo. Dzuwa likukalowa. Dziko likuzizira. Mulungu, mdima pompano uziyamba, ndipo kenako Kubwera kwa Ambuye, kudzautenga Mpingo Wake. Momwe ife tikukuthokozerani Inu chifukwa cha izi, Ambuye!

²⁸⁴ Ife tikupemphera tsopano kuti Inu mumudalitse munthu aliyense mu Kukhalapo Kwaumulungu. Aliyense amene ati adzamvere tepi iyi, Ambuye, kuzungulira dziko, mulole iwo adzachoke ku tizikhulupiriro takale ito ndi zinthu, ndipo adzabwere ndi kudzatumikira Mulungu wamoyo, adzabwere ndi kudzasungitsa Mmenemo, adzachite monga mfumukazi ya Kummwera inachitira. Iye anabwera, zinamutengera iye miyezi itatu kuti adzafike kumene munthu ankamuimira Yesu Khristu, kapena Mulungu wa Kumwamba; Solomoni. Yesu anati, “Iye anabwera kuchokera kothera kwa dziko lapansi, kuti adzamvere nzeru za Solomoni, ndipo taonani wamkulu woposa Solomoni

ali pano.” Ndipo ife tikudziwa “wamkulu woposa Solomoni” ali pano, Mzimu Woyera wawukulu Mwiniwake ali pano, akugwira ntchito kudzera mwa anthu. Mmene ife tikukuthokozerani Inu chifukwa cha izi, Atate. Ine ndikupempherera mdalitso tsopano.

²⁸⁵ Adalitseni abusa athu okonedwa, M’bale Neville. Ambuye, pamene ine—pamene ine ndikuyang’ana pa iye ndi kuganizira za ntchito zake za chikondi, mtima wanga umangolumpha. Ine ndimamukonda iye. Kumuwona iye pamene iye akuyang’ana pa mkazi wake ndi ana ake aang’ono, ine—ine ndikupemphera, Mulungu, kuti Inu mumulimbikitse iye. Mpatсени iye kulimba mtima. Mumudalitse iye kwa zambiri, zaka zina zochuluka za kutumikira mmunda waukulu wokolola uwu umene ife tirimo.

²⁸⁶ Adalitseni abale onse otumikira awa amene akhala pano usikuuno. Ambiri a iwo ndi alendo akuchokera ku malo ena. Ine ndikupemphera kuti Inu mukakhale nawo uko, Junie ndi M’bale Ruddell, ndi amuna ofunika awo amene ali mipingo yaubale ndi mpingo uno kuno, aima ndipo akugwira Kuwala kwa Uthenga mu zigawo zosiyanasiyana za mizinda yozungulira, pa Kuwala komweku uku, tikulimbanira Iko. Zikomo Inu chifukwa cha amuna amenewo, Ambuye. Alimbikitseni iwo. Ndipo apatseni iwo chisomo kuti akaima mmayesero aakulu ndi zinthu zimene zikabwere pa dziko lapansi kuti zikawatsimikizire Akhristu onse.

²⁸⁷ Achiritseni odwala ndi osautsika, Ambuye. Mukhale nafe kudutsa sabata ikubwera iyi tsopano. Tipatseni ife kulimbika. Mulole maphunziro oswekasweka, aang’ono a Sande sukulu a tsikuli asakachoke pa mtima wawo. Mulole iwo akasinkhesinkhe, usana ndi usiku. Perekani madalitso awa, Atate. Mu Dzina la Yesu Khristu, ine ndikupempha izi. Amen.

²⁸⁸ Inu mumamukonda Iye? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Inu mukukhulupirira Izo? [“Ameni.”] Tiyeni tiyimbe nyimbo yathu yabwino kenanso, “ine ndimkonda Iye, ine ndimkonda Iye,” pamene ife tikulumikizana tokha pamodzi. Alikuti Mlongo Ungren? Kodi iye ali pano, mmodzi wa iwo, kapena mlongo amene waimba limba, mmodzi wa madonawo pano? Ine sindikumuwona iye. Eya, ndi uyu apa, dona apa. Uko nkulondola.

²⁸⁹ Ine ndimafuna, usikuuno, ndi ulemu onse, koma ine sindinamuwone M’bale Ungren. Ine ndimafuna kuti iye andiimbire ine, usikuuno, *Ndinu Wamkulu Bwanji!* Ndipo ine ndikuganiza m’baleyo wapita kunyumba. Mukuona? Ine ndinaimva nyimbo imeneyo mmawa uno, ndipo ine ndithudi ndinaiyamikira iyo. Mai, oh, mai! Imeneyo inangolira kudutsa mu mtima mwanga. Ndipo ine—ine—ine ndimafuna kuti ndimuve iye akuimba *Ndinu Wamkulu Bwanji!*

²⁹⁰ Tsopano tiyeni tiyimbe *Ine ndimkonda Iye*, aliyense, pamodzi. Tsopano mungotseka maso anu. Ndipo tiyeni

tiyang'ane kwa Iye tsopano, ndikuti, “Ambuye, ngati pali chathupi chirichonse ichi mwa ine, chichotsenimo icho, pakali pano. Chichotseni icho.” Ndipo inu, uko, mudzamvetsere tepi iyi, pamene inu mudzamvere nyimbo iyi, mudzaimbe nafe, ndiye, pa mpando wanu kumene pamene inu mwakhalapo.

Ngati alipo amenewo, ngati inu mwatsutsidwa ndi Mawu, ngati inu simukuganiza kuti Iwo ndi Mawu, fufuzani Malemba, muone ngati Iwo akulondola. Izo zikukukakamazani inu. Izo zikutanthauza Moyo kapena imfa.

Ndiyeno pamene ife tikuimba nyimbo iyi, ngati muli zachithupi mmoyo mwanu, kodi inu simungakweze dzanja lanu mmwamba, pa mpando wanupo? Apangitseni ana anu ndi mkazi kuti akweze dzanja lawo, okonedwa anu amene akuzungulirani inu. Muziimba *Ine Ndimkonda Iye*, ndipo mupereke moyo wanu kwa Iye. Munene, “Ndiyetseni ine, Ambuye, kwa zoipa zonse.”

Pamene ife tikuimba tsopano, tiyeni tiimirire.

Ine ndimkonda Iye, ine . . .

Ambuye Yesu, ine ndikupemphera kuti Inu muwachiritse anthuwa, awa amene ati akavale mipango iyi. Ine ndikuwadalitsa iwo, mu Dzina la Yesu Khristu. Amen.

Nandigulira chipulumutso changa

Pa mtengo wa Kalvari.

²⁹¹ Tsopano, mu mdalitso waukulu uwu! Ingopitirirani kuimba iyo, mlongo. Mungotseka maso anu ndi kumaganizira, miniti tsopano. Tiyeni tipemphere, mu mtima mwathu, “Ambuye Yesu, ndifufuzeni ine. Kodi ine ndimakukondanidi Inu? Inu munati, ‘Ngati inu mundikonda Ine, inu mudzasunga zonena Zanga. Ngati inu mundikonda Ine, inu mudzasunga Mawu Anga.’” Ndiyeno mu mtima mwanu, munene, “Ambuye, ndiloleni ine ndisunge Mawu Anu. Ndiloleni ine ndiwabise Iwo mu mtima mwanga, ndisadzachimwe konse motsutsa Inu, ndizo, kusakhulupirira chirichonse chimene Inu munanena.”

²⁹² Tsopano pamene ife tikuyimba *Ine Ndimkonda Iye*, tiyeni tigwirane chanza ndi winawake yemwe tayandikana naye. Mungofikirako, ndikuti, “Mulungu akudalitseni inu, m'bale, kapena mlongo.” Mwachete kwenikweni tsopano.

“Ine . . .” Mulungu akudalitseni inu, m'bale. “Ine . . .” Mulungu akudalitseni inu, mlongo wanga. Mulungu akudalitseni inu, mlongo. Mulungu akudalitseni inu. Mulungu akudalitseni inu, mlongo. “Ndipo pur- . . .” Mulungu akudalitseni inu, mlongo wanga. Mulungu akudalitseni inu. Mulungu akudalitseni inu. Mulungu akudalitseni inu. “ . . . - mtengo.”

²⁹³ Tsopano tiyeni tikwezere manja athu kwa Iye.

Ine—ine ndimkonda Iye

Chifukwa . . .

Muli ndi chinachake, chowonjezera, chimene mukufuna kuti muchite? Ndikufuna kuti inu mutibalalitse.

...ine
Nandigulira chipulumutso changa
Pa mtengo wa Kalvari.

²⁹⁴ Inu mumamukonda Iye? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Kodi Iye si wodabwitsa? [“Ameni.”] Ine ndikupempherera mmodzi aliyense wa inu, ana. Ndi cha ubwino wANJI ine kuima pano ndi kumanena zinthu zimenezi ngati ine, mu mtima mwanga, sindikuganizira kuti izo zikakuthandizani inu? Pamene, ine ndatopa ndi kufooka. Ine ndikulephera basi kuti ndiime pano. Mapazi anga akupweteka. Ndipo nsapato zanga, ine ndaima mmenemo mpaka ndikupanga thukuta mmenemo, ndi chirichonse, mpaka mapazi anga afooka. Ndipo ine ndatopa kwambiri! Ine si mwana, panonso. Ndipo ine ndalalikira atatu- kapena maulaliki a maora anayi, ndi kupempherera odwala, ndi kumapita usana ndi usiku. Ine ndingamaimirenji pano, ndikumachita izo?

Inu mukudziwa, zaka sate zonsezi, ngati izo zikanakhala chifukwa cha kutchuka, ine ndazithawa zimenezo. Inu mukudziwa ine sindimatenga ndalama. Inu mukudziwa zimenezo. Ndipo ine sindinatero... Kodi ine ndinakuuzanipo inu chirichonse mu Dzina la Ambuye koma chimene chinadzakwaniritsidwa? Inu mukudziwa izo nzoona.

Ine ndimakukondani inu. Ndi chikondi cha Mulungu chimene chiri mu mtima mwanga kwa wina aliyense wa inu. Ine ndikukhumba ndikanati... Ine ndikukhumba ndikanaima pamaso pa Mulungu, ndikuti, “Mulungu, mulole—mulole—mundilole ine ndiwathandize iwo. Mundilole—mundilole ine ndichite *izi*.” Ine sindingachite izo. Munthu aliyense akuyenera kudziimira yekha. Mukuona?

²⁹⁵ Ine—ine—ine ndikukhulupirira ife tonse tikupita mmwamba tsopano, limodzi la masiku awa. Ndipo ngati zitachitika kuti ife tagona nthawi imeneyo isanafike, ine kudzachotsedwa kwa inu, kumbukirani, ine ndidzakakumana nanu Kumeneko. Ine ndikudziwa kuti Iko kulipo kumeneko. Masomphenya kumene amene anakuuzani inu chirichonse, kukhala changwirowo, akwaniritsidwa basi munga mmene Iye ananenera. Palibepo aliyense, wa zaka zonsezi, yemwe angathe nkomwe kunena pano kuti ine ndinayamba ndakuuzanipo inu chirichonse chimene chikanati chidzachitike koma chimene chinachitika. Dziko lonse, limadziwa zimenezo. Inu simunayambe mwaziwonapo izo pa nsanja, zimene zizamuuza aliyense ndendende Choonadi. Mukuona? Izo nthawizonse zakhala ziri chomwecho. Mulungu yemweyo anandilola ine kuti ndiyang’ane kudutsa katani la nthawi. Ine ndinawawona akazi amenewo ndi amuna akuponya

manja awo mondizungulira ine ndi kumandikumbatira ine, anati, “Oh, M’bale Branham.”

²⁹⁶ Ine—ine sindingati ndingokhala. Chotero, ngati ine ndatopa, ine ndizipita, mulimonse. Nsana wanga ukupweteka. Ndipo ine, tsiku lirilonse. . . Ndine—ndine—ndine wa usinkhu wa zaka forte foro zakubadwa. Inu mukudziwa, iwe umapeza kupweteka kowonjezera tsiku ndi tsiku.

Pemphero langa ndiro, “Mulungu, ndigwireni ine pamodzi. Ndigwireni ine pamodzi, kuti ndilalikire Mawu, ndiime pa Choonadi chimenecho, mpaka ine ndidzamuwone mnyamata wanga, Joseph, atakula mokwanira, ndipo atadzadzidwa ndi Mzimu Woyera; ine ndikhoza kudzatenga Baibulo lakale long’ambika ili, ndikudzaliika Ilo mdzanja lake, ndikuti, ‘Mwana, ulinyamule Ilo mpaka kumapeto a moyo wako. Usadzalekerere pa Ilo.’”

²⁹⁷ Ine ndinkaganiza kuti mwina Billy akanadzalalikira Uthenga. Mulungu sanamuitane iye konse.


Koma ine ndikukhulupirira, Joseph, ngakhale iye ali mnyamata wamng’ono wamakani, ine ndikukhulupirira Mulungu wamuitana iye. Ndi chifukwa chake ana samagwirizana naye, iye ndi mtsogoleri. Ndipo ine—ine—ine ndikudziwa kuti Mulungu wamuitana iye. Ine ndikufuna ndimuphunzitse iye mu njira ya Mawu, njira ya Mawu a Ambuye, kuti iye asadzawasiye Mawu amenewo. Ine ndikufuna ndichite zimenezo, ndekha, ngati Mulungu alola. Ndipo ine ndikadzakalamba ndi kudzakhala kumbuyo, ndipo nkukhoza kumadzamuwona iye pamenepo, ataima paguwa, ndikumati, “Uthenga womwewu uwu, umene adadi anga ankaima nawo. Iwo akhala uko, akalamba ndipo atopa, usikuuno. Koma ine ndikufuna kuti nditenge malo awo ndi kulowa mu nsapato zawo, kuima pamenepo.”

²⁹⁸ Kenako ine ndidzayang’ana mmwamba, ndikuti, “Ambuye, mulole wantchito Wanu achoke mu mtendere.” Izo ndi zimene ine ndikufuna ndidzaziwone, moipa kwambiri. Kufikira nthawi imeneyo ikadzafika. . .

²⁹⁹ Ndiye nanga bwanji ngati ine ndingadzauke mu m’badwo wina? Ine sindingathe. Ine ndikuyenera ndidzabwere ndi m’badwo uno. Ine ndidzayenera kuti ndidzaima ndi inu. Inu ndi amene ine ndidzayenera kuti ndidzakuimireni, ndi kudzakuyankhirani pamaso pa Mulungu, za Uthenga umene ine ndalalikira. Kodi inu mukuganiza kuti ine ndingaima pano ndi kumayesera kuti ndikupotozeni inu, kukuchotsani kwa Chinachake chimene ine ndimaganiza chinali cholondola? Ine ndingakhale ndikukulimbikitsani inu kuti mupite mukachite Ichu. Koma ine ndikudziwa kuti, pamene izo ziri zolakwika, ine ndikufuna kukutulutsani inu mmenemo, kukakulowetsani mu chimene chiri cholondola.

Moonadi, kuchokera mu mtima mwanga, Mulungu andichitire ine umboni, ine ndimakukondani inu, aliyense, ndi chikondi, chenicheni Chaumulungu Chachikhristu. Mulungu akudalitseni inu. Mundipempherere ine.

³⁰⁰ Ine sindikudziwa chimene tsogolo langa lasungira, koma ine ndikumudziwa Amene wagwira tsogolo langa, chotero ine ndimapumula mmenemo.

³⁰¹ Ine ndikupereka, guwa ili kulibwezera kwa munthu amene ine ndiri naye chidaliro chapamwamba, ngati wantchito wa Yesu Khristu, m'busa wathu, M'bale Neville. 

KODI MOYO WANU NDI WOYENERA UTHENGA? CHA63-0630E
(Is Your Life Worthy Of The Gospel?)

Uthenga uwu wa M'bale William Marrion Branham, woperekedwa mu Chingerezi Lamlungu usiku, Juni 30, 1963, ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., unatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nudindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingerezi. Kumasulira kwa Chichewa uku kunadindidwa ndi kugawidwa ndi Voice Of God Recordings.

CHICHEWA

©2020 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org